2026
JUL - SEP

Vol. 102, No. 3
**Maphunziro a M'Baibulo a Lasabata**
Chigawo Cha Akulu



# Kuyenda ndi Yesu

Kuyenda Chifupi ndi Mulungu Kudzera mu *Mapazi Opita kwa Khristu*

# Za Mkatimu

1. Chikondi cha Mulungu pa Munthu ....................5
2. Kusoweka kwa khristu kwa Munthu Wochimwa....................10
3. Kulapa....................15
4. Kubvomereza....................20
5. Kudzipatula....................26
6. Chikhulupiriro ndi Kubvomereza....................31
7. Yeso la Kukhala Ophunzira....................36
8. Kukula mwa Khristu....................41
9. Ntchito komanso Moyo....................46
10. Kudziwa Mulungu....................52
11. Mwayi wa Pemphero....................57
12. Kodi tingachite motani ndi chikayiko?....................62
13. Kukondwera mwa Ambuye....................67

Maphunziro a Baibulo apa Sabata, maphunziro a tsiku ndi tsiku, ndi ochokera mu Baibulo ndi Mzimu wa Chinenero okha basi opanda ndemanga zoonjezera. Mawu a ndemanga za m'baibulo ndi mu Mzimu wa Chinenero ndi achidule oti apereke malingaliro ofunikira achidule komanso achindunji. Zikutiro [ ] zimaperekedwa mu nthawi zina kuti zitsimikize kumveka bwino, nkhani yoyenera, ndi kuwerenga kosalala. Kuphunzira kopitilira kupyolera mu mmene mwachokera ndemanga kumalimbikitsidwa kwambiri.

**Zithunzi ndi Chikutiro:** Honduran Union, Rwandan Union Mission, AMAPI, H. Cibalde

Copyright © 2025 by the Seventh Day Adventist Reform General Conference, Chigawo cha Sabata Sukulu, 5240 Hollins Road, Roanoke, Virginia 24019, USA. Telefoni: 1—540—362—1800 • Webusaiti: www.sdarm.org • Imelo: info@sdarm.org Kumalawi: SDARM Malawi Mission P.O. Box 200069 Lilongwe 2. Foni: +265 999 701 423, +265 884 288 535

Maphunziro a Baibulo pa Sabata (USPS 005—118), Vol. 101, No. 2, Apulo – Juni 2025. Lofalitsidwa pa kotala ndi Seventh Day Adventist Reform General Conference, chigawo cha Sabata Sukulu Kusindikizidwa, ndi kugawidwa ndi Reformation Herald Publishing Association, 5240 Hollins Road, Roanoke, Virginia 24019–5048, U.S.A. Malipiro anthawi ndi nthawi ku Roanoke, Virginia 24022—9993.

**U.S.A. ndi Canada**

Lumikizanani: Telefoni 1—540—366—9400 • Webusaiti: www.reformationherald. com • Imelo: info@reformationherald.org Kulembetsa pachaka ku U.S.A.: U.S. $22.00. Kusindikiza kwakukulu $33.00. Mayiko $21.00 kuphatikiza kutumiza. Kusindikiza kwakukulu kwapadziko lonse $31.00 kuphatikiza kutumiza. Kope limodzi $6.00. Kusindikiza kwakukulu $9.00. Chonde tumizani zopempha zolembetsa ndi zolipira (mu ndalama zaku U.S. zokha) pa keyala ali pansipa. Mitengo zitha kusintha popanda chidziwitso. POSTMASTER, chonde tumizani kusintha maadiresi ku: Maphunziro a Baibulo a Sabata,

**South Africa**

Lumikizanani: Telefoni & Fax 27—011—336—7064 • Webusaiti: www.sdarm sa.org. za •Imelo: admin@sdarm sa.org.za Kulembetsa kwapachaka mu South Africa: R120—00 (kope limodzi R35—00). Chonde tumizani zopempha zolembetsa ndi zolipira ku adilesi ili pansipa. POSTMASTER, chonde tumizani kusintha maadiresi ku: Maphunziro a Baibulo a Sabata, P. O. Box 7950, Johannesburg 2000, South Africa

**Malawi**

Lumikizanani: Telefoni +26 999 701 423, +265 884 288 535 za•Imelo: sdarmmalawi@yahoo.com Kulembetsa kwapachaka Malawi: MK 2000 (kope limodzi MK 500). Chonde tumizani zopempha zolembetsa ndi zolipira ku adilesi ili pansipa. POSTMASTER, chonde tumizani kusintha maadiresi ku: Maphunziro a Baibulo a Sabata, P. O. Box 20069, Lilongwe 2, Malawi.

# Mawu Otsogolera

Mndandanda wa maphunziro oti aphunziridwe m'kotala ino, "Kuyenda ndi Yesu," ndi wachokera m'buku la *Steps to Christ.* Bukuli likhoza kuwerengedwa, mutu ndi mutu, ngati ndemanga pa maphunziro a Malemba.

Ophunzira ena a Sabata Skulu adzakumbukira nthawi yomwe nkhaniyi idakambidwa mu kota yoyamba ya chaka cha 1980. Ndichikondwero chathu kuiperekanso phunziroli ndi kapangidwe katsopano ndi zipangizo zina zowonjezera, koma ndi zoonadi zozama zomwezo zomwe zidanenedwa kalekale.

Kawirikawiri anthu amaganiza kuti Atate wawo wakumwamba ndi wouma mtima komanso otalikana nawo, woweruza wankhanza komanso wouma mtima. Iwo samawona kuzama kwa chikondi Chake pa iwo, komanso chisamaliro Chake chachikondi chomwe ali nacho mumtima Mwake pa ana ake onse.

Chikondi cha Mulungu chiyenera kukhala chinthu choyamba chomwe chikuwonetsedwa. Kenako chiyenera kutsatirapo ndi mfundo yakuti wochimwayo ndi wopanda thandizo komanso wopanda chiyembekezo, ndipo ndiwosowa Mpulumutsi. Moyo wa Khristu, yemwe anabwera kudzapulumutsa ochimwa, umasonyeza kuti pali njira yotsimikizika yobwerera kwa Atate wakumwamba.

Mitu yomwe yakambidwa m'maphunzirowa ikukhudzana ndi zochitika zazikulu m'moyo wachikhristu ndipo makamaka imagwirizana ndi wokhulupirira watsopano m'chikhulupiriro amene akufuna kukula mu chisomo. Okhulupirira onse ayenera kuwunikanso mituyi nthawi ndi nthawi—osati ku phindu laokha, komanso kuti adziwe nawonso njira yabwino kwambiri yothandizira ena kubwera kwa Khristu.

Kupereka mfundo za choonadi mwadongosolo kungathandize munthu kumvetsa bwino ndi kuzilandira izo, ndipo kumathandiza munthu kulandiridwa kukhala membala wa mpingo. Koma ngati munthu wotereyu salumikizidwa ndi Khristu, alibe moyo weniweni—moyo wosatha. Zoonadi, "yekhayo amene akhulupirira Mwanayo ali ndi moyo wosatha" (Yohane 3:36).

Aliyense wa Sabata Skulu ayenera kukhala ndi umboni wa Mzimu ndi mzimu wake kuti walandiridwadi m'banja la Mulungu. Aliyense ayenera kuzindikira kuti chitsanzo chake, kudalira kwawo kosalekeza pa Atate wakumwamba, nthawi zonse komanso pazinthu zonse, kuyenera kukhala kwenikweni komanso koonekera mmachitachita. Pakufunika zambiri kuposa chikondi chofooka cha anthu. Onse amafunikira chikondi cha Mulungu—chikondi chopanda dyera cha Mulungu—chobzalidwa mumtima ndi m'miyoyo yawo kuti akonde monga momwe Iye anakondera.

Izi zikhale zodutsamo za moyo za membala aliyense wa m'Sabata Skulu.

*Nthambi ya Sabata Skulu ya General Conference*

# Zopereka Za Sabata Loyamba

**Lasabata, Julayi 5, 2026**



## Kukuza Mpingo ku Chennai, India

Chennai, yomwe kale inkadziwika kuti Madras, ndi likulu komanso mzinda waukulu kwambiri wa Tamil Nadu, boma lakum'mwera kwambiri kwa India. Liri pagombe la Coromandel wa mpepete mwa Nyanja ya Bengal. Malinga ndi kalembera wa anthu aku India wa 2011, Chennai ndi mzinda wachisanu ndi chimodzi wokhala ndi anthu ambiri ku India ndipo ndi mzinda wachinayi wokhala ndi anthu ambiri mumzinda. Greater Chennai Corporation, yomwe idakhazikitsidwa mu 1688, ndi kampani yakale kwambiri ya boma ku India ndipo ndi yachiwiri ya ma kampani akale kwambiri padziko lonse lapansi pambuyo pa London. Iyo ili ndi malo ochitira malonda owe ali ndi mafakitale pafupifupi 15,000 ndipo ndi malo ochitirako zokopa alendo azachipatala, otchedwa "likulu la zaumoyo ku India."

Mzindawu ulinso ndi gawo lalikulu la mafakitale a magalimoto ku India, motero dzina lake lina ndi, "Detroit of India." Chennai inali mzinda wokhawo waku South Asia womwe udayikidwa pamndandanda wa "Mizinda 10 Yapamwamba Kwambiri Yazakudya" ya *National Geographic* mu 2015 ndipo yayikidwa pamndandanda wachisanu ndi chinayi pamizinda yabwino kwambiri padziko lonse lapansi *ya Lonely Planet .*

Chiwerengero cha anthu ku Chennai tsopano chaposa 12 miliyoni, ndipo pakali pano chikuwonjezeka ndi 2.34% pachaka chilichonse. Mzindawu uli ndi anthu osiyanasiyana ochokera m'mitundu yosiyanasiyana yachipembedzo. Malinga ndi kalembera wa anthu wa chaka cha 2011, anthu ambiri ku Chennai anali Ahindu (80.73%), kutsatiridwa ndi 9.45% Asilamu, 7.72% Achikhristu, 1.27% ena ndi 0.83% omwe sali ndi chipembedzo chilichonse.

Mu 2019, 40% mwa mabanja 1.788 miliyoni mumzindawu amakhala pansi pa mzere wa umphawi. Mu 2017, mzindawu unali ndi mabanja 2.2 miliyoni, ndipo 40% ya okhalamo analibe nyumba yawo yawo. Pali nyumba zaosauka pafupifupi 1,131 mumzindawu, zomwe zimakhalidwa ndi mabanja oposa 300,000. Anthu amitundu yonse amakhala kuno, ndipo onse amafunika kumva uthenga wabwino wosatha wa Yesu Khristu m'masiku otsiriza ano.

Chifukwa cha mavuto azachuma, sitinathe kumaliza kumanga tchalitchi ku Chennai panthawi yomwe tinkayembekezera. Tsopano, popeza ntchito ikupitirira, tazindikiranso kufunika kokulitsa ntchitoyi ndi kumanga nyumba zina za abusa, holo ya misonkhano, ndi makalasi ya ana a Sabata Skulu. Kuti tikwaniritse izi, tifunika kupempha kukoma mtima kwa mipingo yathu yokondedwa padziko lonse lapansi.

Ndi pempho lathu lofunika kwambiri kwa abale athu, alongo athu, ndi achinyamata athu chonde perekani zopereka zanu zachifundo pa ntchitoyi.

Zikomo kwambiri, ndipo Ambuye akudalitseni nonse.

*Abale ndi alongo anu ku Chennai*

LASABATA, JULY 4, 2026

Phunziro 1

# Chikondi cha Mulungu kwa Munthu

**Vesi Loloweza:** "Taonani chikondi chimene Atate watipatsa, kuti titchedwe ana a Mulungu; chifukwa chake dziko lapansi silitidziwa ife, chifukwa silinam'dziwe Iye" (1 Yohane 3:1).

**Zowerenga Zoonjezera:** *Steps to Christ,* pp. 9–15.

"Mulungu ndi chikondi. Monga kuwala kwa dzuwa, chikondi ndi kuwala ndi chimwemwe zimatuluka kuchokera kwa Iye kupita ku zolengedwa Zake zonse."—*Thoughts from the Mount of Blessing,* p. 77.

## 1. MULUNGU NDI CHIKONDI

**Loyamba, Juni 2**

a. **Ndi umboni wotani wa chikondi cha Mulungu womwe waperekedwa kwa anthu? Eksodo 34:6, 7; Yona 4:2 (gawo lomaliza); Yeremiya 31:3.**

____________________________________________________________

____________________________________________________________

____________________________________________________________

"Mawu a Mulungu amavumbulutsa khalidwe Lake. Iye mwini walengeza chikondi Chake chosatha ndi chifundo Chake. Pamene Mose anapempha, 'Ndionetseni ulemerero Wanu,' Yehova anayankha, 'Ndidzapititsa ukoma Wanga wonse pamaso pako.' Eksodo 33:18, 19. Uwu ndi ulemerero Wake. Ambuye anadutsa pamaso pa Mose, nati, 'Yehova, Yehova Mulungu, wachifundo ndi wachisomo, woleza mtima, ndi wodzala ndi ubwino ndi choonadi, wosungira chifundo anthu zikwi, wokhululukira mphulupulu ndi zolakwa ndi uchimo.' Eksodo 34:6, 7. Iye ndi 'wosakwiya msanga, ndi wachifundo chachikulu,' 'chifukwa Iye akondwera ndi chifundo.' Yona 4:2; Mika 7:18."—Steps *to Christ,* p. 10.

b. **Kodi cholinga cha Mulungu potumiza Mwana wake chinali chiyani? Mateyu 11:27; Yohane 14:8, 9.**

____________________________________________________________

____________________________________________________________

____________________________________________________________

"Satana anatsogolera anthu kuganiza kuti Mulungu ali ngati munthu amene khalidwe lake lalikulu ndi loweruza mwankhanza—yemwe ndi woweruza wankhanza, wokongoza ngongole mopanda chilungamo ndi mwankhanza. Iye amayerekezera Mlengi ndi munthu amene akuyang'ana ndi maso ansanje kuti azindikire zolakwa ndi zolakwitsa za anthu, kuti awapatse chilango. Yesu anabwera kudzakhala pakati pa anthu kuti achotse mdima umenewu, mwa kuonetsera chikondi chosatha cha Mulungu."—Ibid., p. 11.

**a. Kodi Yesu anafotokozera bwanji za ntchito yake ya padziko lapansi? Luka 4:16–18.**

“[Kuchokera pa Luka 4:18] Iyi inali ntchito ya [Yesu]. Iye anayendayenda akuchita zabwino ndi kuchiritsa onse omwe anali oponderezedwa ndi Satana. Kunalibe midzi yonse kubuura kwa matenda m'nyumba iliyonse, chifukwa Iye anadutsamo ndi kuchiritsa odwala awo onse. Ntchito yake inapereka umboni wa kudzozedwa kwake kwaumulungu. Chikondi, chifundo, ndi kukoma mtima zinaonekera mu chochita chilichonse cha moyo wake; mtima wake unakhala wachifundo kwa ana a anthu. Iye anatenga chibadwa cha munthu, kuti afikire zosowa za munthu. Osauka kwambiri komanso odzichepetsa sanaope kumuyandikira. Ingakhale ana aang'ono ankakopeka naye. Iwo ankakonda kukwera pa mawondo ake ndikuyang'ana nkhope yowalabadirayo, yokoma mtima ndi chikondi.”—*Steps to Christ,* pp. 11, 12.

“Yesu anaona mwa munthu aliyense munthu amene ayenera kupatsidwa kuyitanira ku ufumu Wake. Iye anafika pa mitima ya anthu mwa kupita pakati pawo ngati munthu amene amawafunira zabwino. Iye anawafunafuna m’misewu ya anthu onse, m’nyumba za anthu, m’mabwato, m’sunagoge, m’mphepete mwa nyanja, ndi pa phwando la ukwati. Iye anakumana nawo pa ntchito zawo za tsiku ndi tsiku, ndipo anasonyeza chidwi mu zochitika zawo za tsiku ndi tsiku. Iye anapereka malangizo ake m’nyumba, kubweretsa mabanja m’nyumba zawo pansi pa chikoka cha kukhalapo Kwake kwaumulungu. Chifundo chake champhamvu chinathandiza kukopa mitima. Nthawi zambiri ankapita kumapiri kukapemphera payekha, koma izi zinali kukonzetsera ntchito Yake pakati pa anthu omwe anali ndi moyo wotanganidwa. Kuchokera nthawi imeneyi Iye ankatuluka kudzathandiza odwala, kulangiza osadziwa, ndi phwanya maunyolo a akapolo a Satana.”—*The Desire of Ages,* p. 151.

**b. Ngakhale kuti anali wodzaza ndi chikondi ndi chifundo, kodi ndi chitsanzo chotani cha kukhulupirika kwa Khristu mu kudzudzula zolakwika? Yohane 9:39–41; Mateyu 21:12, 13.**

“Yesu sanapondereze mawu amodzi a choonadi, koma nthawi zonse ankawanena mwachikondi. Ankachita zinthu mwanzeru kwambiri komanso molingalira, chidwi cha chifundo mu kulumikizana ndi anthu. Iye sanali wamwano, sanalankhule mawu amphamvu mosayenera, sanamvetse ululu wosafunikira kwa munthu wokhudzika. Iye sanadzudzule kufooka kwa anthu. Analankhula choonadi, koma nthawi zonse mwachikondi. Anadzudzula chinyengo, kusakhulupirira, ndi kusayeruzika; koma misozi inali m’mawu Ake pamene ankalankhula mawu ake odzudzula mwamphamvu. . . Munthu aliyense anali wamtengo wapatali m’maso mwake. Ngakhale kuti nthawi zonse ankadzionetsera ulemu waumulungu, anawerama ndi ulemu waukulu kwa membala aliyense wa banja la Mulungu. Mwa anthu onse Iye anaona miyoyo yogwa yomwe cholinga chake chinali kuipulumutsa.”—*Steps to Christ,* p. 12.

**a. Ndi katundu wolemera wotani amene Mpulumutsi wathu ananyamula panthawi ya moyo wake padziko lino lapansi? Yesaya 53:5–7; Luka 2:48, 49.**

___

___

___

"Yesu ananyamula udindo waukulu woopsya wopulumutsa anthu. Iye ankadziwa kuti pokhapokha ngati pakhala kusintha kwakukulu pa mfundo ndi zolinga za mtundu wa anthu, onse adzatayika. Uyu anali katundu wa moyo Wake, ndipo palibe amene akanatha kuyamikira katundu amene anali pa Iye. Mu umwana, unyamata, ndi ukulu wake, Iye ankayenda yekha. Komabe, kunali kupezeka kumwamba kungokhala chabe pamaso pake. Tsiku ndi tsiku Iye ankakumana ndi mayeso ndi mayesero; tsiku ndi tsiku ankakumana ndi choipa, ndipo anaona mphamvu ya choipa pa iwo amene ankafuna kuwadalitsa ndi kuwapulumutsa. Komabe sanalephere kapena kukhumudwitsidwa.

“Mu zinthu zonse Iye analondoloza zofuna zake kukukwaniritsa ntchito Yake. Iye analemekeza moyo Wake mwa kupanga chilichonse cha moyo wake kukhala chogonjera chifuniro cha Atate Wake. Pamene Iye ali mnyamata, amayi Ake, atamupeza mu sukulu ya arabi, anati, 'Mwana, wativutitsiranji chonchi?' Iye anayankha— ndipo yankho Lake ndilo mfundo yaikulu ya ntchito Yake ya moyo— 'Munali kundifunafuna chifukwa chiyani? Simudziwa kuti ndiyenera kukhala m'ntchito ya Atate Wanga?'

"Moyo wake unali wodzipereka msembe nthawi zonse. Iye analibe pokhala m'dziko lino, kupatulapo pamene kukoma mtima kwa abwenzi kunamupatsa Iye monga wapaulendo. Iye anabwera kudzakhala moyo wosaukitsitsa m’malo mwathu, ndi kuyenda ndi kugwira ntchito pakati pa osowa ndi ovutika. Wosazindikirika komanso wosalemekezedwa, Iye anayenda kupita ndi kutuluka pakati pa anthu omwe Iye anawachitira zambiri.”— *Gospel Workers,* pp. 42, 43.

**b. Kodi kufalikira kwa chikondi chachikulu cha Mulungu kumatiphunzitsa chiyani za Atate wathu wakumwamba? Yohane 3:16; 1 Yohane 4:9, 10.**

___

___

“Nsembe yaikulu iyi sinapangidwe kuti ipange mumtima mwa Atate chikondi pa munthu, osati kuti Iye afune kupulumutsa. Ayi, ayi! ‘Mulungu anakonda dziko lapansi, kotero kuti anapereka Mwana wake wobadwa yekha.’ Yohane 3:16. Atate amatikonda, osati chifukwa cha dipo lalikulu, koma Iye anapereka dipo chifukwa amatikonda. Khristu anali njira yomwe Iye akanatha kutsanulira chikondi chake chopanda malire pa dziko lochimwa. ‘Mulungu anali mwa Khristu, kuyanjanitsa dziko lapansi kwa Iye mwini.’ 2 Akorinto 5:19. Mulungu anazunzika ndi Mwana wake. Mu ululu wa Getsemane, imfa ya pa Kavale, mtima wa Chikondi Chopanda malire chinalipira mtengo wa chiwombolo chathu.” — Steps *to Christ,* p. 13.

**a. Kodi maziko a chipulumutso cha miyoyo yathu ndi chiyani? 1 Akorinto 1:30; Machitidwe 16:31.**

---

“O, Khristu anali ndi njala ndi chikhumbo chachikulu chotani nanga cha moyo kuti apulumutse chomwe chinatayika! Thupi lopachikidwa pamtanda silinachepetse umulungu Wake, mphamvu Yake ya Mulungu yopulumutsa kudzera mu nsembe ya anthu, onse omwe angalandire chilungamo Chake. Pofa pamtanda, Iye anasamutsa mlandu kuchokera kwa munthu wochimwa kupita kwa Wolowa m'malo wake wa umulungu kudzera mu chikhulupiriro mwa Iye monga Mombolo wake. Machimo a dziko lolakwa, omwe m'chifaniziro akuimiridwa ngati 'ofiira ngati kapezi,' adawerengedwa kwa dipo la umulungu.”—This *Day With God,* tsamba 236.

**b. Kodi Khristu anachita chiyani kuti atipulumutse chomwe chili choposa khama kapena nzeru za munthu? Yohane 10:17; Aroma 5:6–8.**

---

'Atate wanga wakhala akukukondani inu kwambiri kotero kuti amandikondanso Ine koposa chifukwa chopereka moyo wanga kuti ndikuwomboleni. Pokhala Wolowa m'malo mwanu ndi dipo lanu, popereka moyo wanga, potenga mangawa anu, zolakwa zanu, ndimakondedwa ndi Atate wanga kwambiri; pakuti ndi nsembe Yanga, Mulungu akhoza kukhala wolungama, komanso wolungamitsa iye amene akhulupirira Yesu.'

“Palibe wina koma Mwana wa Mulungu amene akanatha kutipulumutsa; pakuti Iye yekha amene anali pachifuwa cha Atate ndiye akanatha kumulengeza Iye. Iye yekha amene ankadziwa kutalika ndi kuya kwa chikondi cha Mulungu ndiye akanatha kuchiwonetsa. Palibe china chocheperapo kupatula nsembe yopanda malire yoperekedwa ndi Khristu m'malo mwa munthu wochimwa yomwe ikanatha kusonyeza chikondi cha Atate kwa anthu otayika.”—*Steps to Christ,* p. 14.

**c. Kodi Yohane akanachitira umboni chiyani za wotiyimira pampando wachifumu wa Mulungu? 1 Yohane 1:1–3.**

---

“Pali ochepa okha amene amazindikira khalidwe loipa la uchimo, ndipo amamvetsetsa kukula kwa chiwonongeko chomwe chabwera chifukwa cha kuswa lamulo la Mulungu. Mwa kufufuza dongosolo lodabwitsa la chiwombolo chobwezeretsa wochimwa ku chifaniziro cha makhalidwe abwino a Mulungu, tikuona kuti njira yokhayo yopulumutsira munthu inapangidwa kudzera mukudzipereka msembe, ndi kudzitsitsa kosayerekezeka ndi chikondi cha Mwana wa Mulungu. Iye yekha ndiye anali ndi mphamvu yomenya nkhondo ndi mdani wamkulu wa Mulungu ndi munthu, ndipo, monga wolowa m'malo mwathu ndi dipo lathu, Iye wapereka mphamvu kwa iwo amene amamugwira Iye ndi chikhulupiriro, kuti akhale ogonjetsa m'dzina Lake, komanso kudzera mu ubwino Wake. ” — *Christian Education,* p. 112.

## 5. YESU ANALIPIRA DIPO

**Lachisanu, Julayi 2**

**a. Kodi n'chiyani chinapangitsa Khristu kukhala woyenera kulipira dipo la chiwombolo chathu? 1 Petro 1:18, 19; Ahebri 5:8, 9.**

___

___

___

"Mtengo wolipidwa kutiwombola, nsembe yopanda malire ya Atate wathu wakumwamba popereka Mwana wake kuti atifere, iyenera kutipatsa ife malingaliro apamwamba a zomwe tingakhale kudzera mwa Khristu. Monga tauziridwa ndi mtumwi Yohane poona kutalika, kuzama, ndi kukula kwa chikondi cha Atate kwa mtundu wowonongeka, anadzazidwa ndi kuyamikira ndi ulemu; ndipo, polephera kupeza chilankhulo choyenera chofotokozera ukulu ndi kukoma mtima kwa chikondi ichi, anaitana dziko lonse kuti lichione… . . . Ndi mtengo wanji umene izi zimaika pa munthu! Kudzera mu kuchimwa ana a munthu amakhala akapolo a Satana. Kudzera mu chikhulupiriro mu nsembe yotetezera ya Khristu ana a Adamu akhoza kukhala ana a Mulungu. Mwa kutenga khalidwe la umunthu, Khristu amakweza mtundu wa anthu. Anthu okugwa amaikidwa komwe, kudzera mu kulumikizana ndi Khristu, iwo angakhaledi oyenerera kutchedwa 'ana a Mulungu.' " —Steps *to Christ,* p. 15.

**b. Ndi mawu ati omwe mtumwi Yohane anagwiritsa ntchito pofotokoza kukula kwa chikondi cha Mulungu? 1 Yohane 3:1, 2.**

___

___

"Chikondi choterechi chilibe chofanana nacho. Ana a Mfumu yakumwamba! Lonjezo lamtengo wapatali! Mutu wa kusinkhasinkha kwakukulu! Chikondi chosayerekezeka cha Mulungu ku dziko lomwe silinamukonde lye! Lingaliroli lili ndi mphamvu yogonjetsa moyo ndipo limabweretsa malingairo mu ukapolo ku chifuniro cha Mulungu. Pamene tikuphunzira kwambiri khalidwe la Mulungu mu kuwala kwa mtanda, timaona kwambiri chifundo, kukoma mtima, ndi chikhululukiro zikugwirizana ndi kupanda tsankho ndi chilungamo, ndipo timazindikira bwino kwambiri maumboni osawerengeka a chikondi chomwe chilibe malire ndi chifundo choleza choposa chifundo cha mayi kwa mwana wake wopanduka." —Ibid.

## MAFUNSO OBWEREZA PAWEKHA

**Lachisanu n'chimodzi, Julayi 3**

1. Fotokozani makhalidwe ofunikira kwambiri a khalidwe la Mulungu.
2. Kodi Yesu anaulula bwanji khalidwe la Mulungu ali padziko lapansi?
3. Kodi ntchito ya Khristu inakhudza bwanji zisankho zake?
4. Mwa kukhala mlowa m'malo wathu, kodi Yesu amaphunzitsa maphunziro otani?
5. Fotokozani mphatso yomaliza ya Khristu m'malo mwathu.

LASABATA, JULAYI 11, 2026

Phunziro 2

# Kusoweka kwa Nkhristu kwa Munthu Wochimwa

**Vesi Loloweza:** "Yesu anayankha nati kwa iye, indetu, indetu, ndinena kwa iwe, ngati Munthu sabadwa mwatsopano, sangathe kuona ufumu wa Mulungu" (Yohane 3:3).

**Zowerenga Zoonjezera:** *Steps to Christ,* pp. 17–22.

"Chiyembekezo chokhacho cha chiwombolo cha mtundu wathu wokugwa chili mwa Khristu."—*The Desire of Ages,* p. 147.

## 1. MMENE MUNTHU ANALIRI PACHIYAMBI — Loyamba, Julayi 5

**a. Fotokozani mmene munthu analiri mu Edeni. Genesis 1:26, 27, 31; Masalmo 8:4–6.**

---

"Poyamba munthu anapatsidwa mphamvu zaulemu ndi maganizo okhazikika bwino. Iye anali wangwiro m'chikhalidwe chake, ndipo anali mu mgwirizano ndi Mulungu."—*Steps to Christ,* p. 17.

"Munthu anayenera kusonyeza chifanizo cha Mulungu, pa maonekedwe akunja komanso pa khalidwe. Khristu yekha ndiye 'chifanizo chenicheni' (Ahebri 1:3) cha Atate; koma munthu analengedwa m'chifanizo cha Mulungu. Chikhalidwe chake chinali mu mgwirizano ndi chifuniro cha Mulungu. Maganizo ake anatha kumvetsa zinthu zaumulungu. Zokonda zake zinali zoyera; zilakolako ndi zikhumbo zake zinali pansi pa ulamuliro wa nzeru. Iye anali woyera ndi wokondwa chifukwa chonyamula chifanizo cha Mulungu ndi kumvera mwangwiro chifuniro Chake."—*Patriarchs and Prophets,* p. 45.

**b. Kodi Satana anagwira ntchito bwanji kuti awononge cholinga chaumulungu pakulengedwa kwa munthu? Genesis 3:1–7; Aroma 6:16; 1 Yohane 2:16.**

---

"Kudzera mu kusamvera, mphamvu za [munthu] zinapotozedwa, ndipo kudzikonda kunalowa m'malo mwa chikondi. Chikhalidwe chake chinafooka kwambiri chifukwa cha kuchimwa moti zinali zosatheka kwa iye, mwa mphamvu zake yekha, kukana mphamvu ya choipa. Iye anakhala kapolo wa Satana, ndipo akanakhalabe choncho mpaka kalekale Mulungu akanapanda kulowererapo mwapadera. Cholinga cha woyesa chinali kusokoneza dongosolo la Mulungu pakulengedwa kwa munthu ndi kudzaza dziko lapansi ndi chisoni ndi chiwonongeko. Ndipo akanasonyeza zoyipa zonsezi ngati zotsatira za ntchito ya Mulungu yolenga munthu."—*Steps to Christ,* p. 17.

**a. Atachimwa, Adamu ndi Hava anachita bwanji atamva mau a Mulungu? Genesis 3:8–10.**

______________________________________________________________

______________________________________________________________

**b. N'chifukwa chiyani anthu ochimwa sakwanitsa kuyima pamaso pa Wosathayo? Eksodo 33:20; Deuteronomo 4:23, 24.**

______________________________________________________________

______________________________________________________________

"Mu chikhalidwe chake chosachimwa, munthu anali ndi ubwenzi wosangalala ndi Iye 'amene mwabisidwa chuma chonse cha nzeru ndi chidziwitso.' Akolose 2:3. Koma atachimwa, sanathenso kusangalala ndi chiyero, ndipo anayesera kubisala pamaso pa Mulungu. Umenewu ndi m'mene mtima wosabadwanso umakhalirabe mpaka lero. Suli mu mgwirizano ndi Mulungu ndipo supeza chisangalalo mu chiyanjano ndi Iye. Wochimwa sangathe kukhala wokondwa pamaso pa Mulungu; angapewere kukhala pamodzi ndi oyera mtima. Ngati ataloledwa kulowa kumwamba, kumeneko sikukanakhala kosangalatsa kwa iye. Mzimu wa chikondi chosadzikonda womwe umalamulira kumeneko, mtima uliwonse ukuyankha mtima wa Chikondi Chopanda Malire, sukanakhudza chilichonse mu moyo wake. Maganizo ake, zokonda zake, ndi zolinga zake zikanakhala zosiyana ndi za anthu opanda tchimo okhala kumeneko. Akanakhala ngati mawu osagwirizana m'nyimbo ya kumwamba. Kumwamba kungakhale kwa iye malo ozunzika; akanalakalaka kubisika kwa Iye amene ali kuunika kwake ndi pakati pa chisangalalo chake. Sikuti ndi lamulo lopanda chilungamo la Mulungu lomwe limatseka oipa kunja kwa kumwamba; iwo amatsekedwa ndi kusayenerera kwawo kukhala pamodzi ndi oyera. Ulemerero wa Mulungu ukadakhala kwa iwo moto wowawononga."—*Steps to Christ,* pp. 17, 18.

**c. N'chifukwa chiyani n'zosatheka kuti munthu mwa iye yekha athawe chilango cha tchimo? Yobu 14:4; Aroma 8:7, 8; Yesaya 64:6.**

______________________________________________________________

______________________________________________________________

"N'zosatheka kwa ife, mwa ife tokha, kuthawa dzenje la tchimo limene tagweramo. Mitima yathu ndi yoyipa, ndipo sitingaisinthe. 'Ndani angatulutse choyera m'chonyansa? Palibe mmodzi.' Yobu 14:4. . . . Maphunziro, chikhalidwe, kugwiritsa ntchito chifuniro, ndi khama laumunthu, zonsezi zili ndi malo ake; koma pa nkhaniyi zilibe mphamvu. Zingapange khalidwe labwino looneka kunja, koma sizingasinthe mtima; sizingayeretse magwero a moyo. Payenera kukhala mphamvu yogwira ntchito kuchokera mkati, moyo watsopano wochokera kumwamba, munthu asanasinthidwe kuchoka mu tchimo kupita ku chiyero. Mphamvu imeneyo ndi Khristu. Chisomo Chake chokha chingapereke moyo ku mphamvu zakufa za moyo wamkati, ndi kukokera moyo kwa Mulungu, ku chiyero."—Ibid., p. 18.

**a. Kodi tiyenera kuzindikira chiyani za mtima wa munthu? Masalimo 14:1–3; Aroma 3:9–11.**

____________________________________________________________________

____________________________________________________________________

"Mawu a Mulungu alengeza kuti, 'Onse anachimwa, naperewera pa ulemerero wa Mulungu' (Aroma 3:23). 'Palibe wochita zabwino, palibe ngakhale mmodzi' (Aroma 3:12). Ambiri amanyengedwa pa nkhani ya chikhalidwe cha mitima yawo. Sadziwa kuti mtima wachibadwa ndi wachinyengo koposa zinthu zonse, ndipo ndi woipa kwambiri. Amadzifunda ndi chilungamo chawo, ndipo amakhutitsidwa pofika pa muyezo wawo waumunthu wa khalidwe; koma alephera koopsa pamene safika pa muyezo waumulungu, ndipo mwa iwo okha sangathe kukwaniritsa zofuna za Mulungu."—Selected Messages, bk. 1, p. 320.

**b. N'chifukwa chiyani ife monga anthu sitingathe kuzindikira dziko lauzimu ndi kuona ufumu wa Mulungu? 1 Akorinto 2:14; 2 Akorinto 4:4.**

____________________________________________________________________

____________________________________________________________________

"Mpulumutsi anati, 'Munthu akapanda kubadwa kuchokera kumwamba,' pokhapokha atalandira mtima watsopano, zokhumba zatsopano, zolinga zatsopano, ndi njira zatsopano zotsogolera ku moyo watsopano, 'sangathe kuona ufumu wa Mulungu.' Yohane 3:3, kumapeto. Lingaliro lakuti munthu amafunikira kokha kukulitsa zabwino zomwe zili mwa iye mwachibadwa, ndi chinyengo chowopsa. 'Munthu wachibadwa salandira zinthu za Mzimu wa Mulungu, chifukwa zili zopusa kwa iye; ndipo sangathe kuzidziwa, chifukwa zidziwika mwa uzimu.' 'Musadabwe kuti ndinati kwa iwe, Muyenera kubadwanso.' 1 Akorinto 2:14; 3:7. Za Khristu kwalembedwa kuti, 'Mwa Iye munali moyo; ndipo moyowo unali kuunika kwa anthu' ndi 'dzina lokhalo pansi pa thambo lopatsidwa mwa anthu limene tiyenera kupulumutsidwa nalo.' Yohane 1:4; Machitidwe 4:12."—Steps to Christ, pp. 18, 19.

**c. Ngakhale sitingathe kudzipulumutsa tokha, kodi tingachite chiyani? Mateyu 11:28–30; Yohane 3:3.**

____________________________________________________________________

____________________________________________________________________

"Mulungu anayenera kuonetsedwa mwa Khristu, 'kuyanjanitsa dziko lapansi ndi Iye mwini.' 2 Akorinto 5:19. Munthu anali atatsika kwambiri chifukwa cha tchimo moti zinali zosatheka kwa iye, mwa iye yekha, kubwera mu mgwirizano ndi Iye amene chikhalidwe Chake ndi chiyero ndi ubwino. Koma Khristu, atawombola munthu ku chiweruzo cha lamulo, akanatha kupereka mphamvu yaumulungu kuti igwirizane ndi khama laumunthu. Motero, mwa kulapa kwa Mulungu ndi chikhulupiriro mwa Khristu, ana a Adamu ogwa akanatha kukhalanso 'ana a Mulungu.' 1 Yohane 3:2."—Patriarchs and Prophets, p. 64.

**a. Kodi vuto la mtumwi Paulo linali chiyani pamene anazindikira mokwanira mmene analiri ngati wochimwa pamaso pa Mulungu? Aroma 7:12, 14, 24.**

---

---

“Sikokwanira kungoona kukoma mtima kwa Mulungu, kuona ubwino ndi chisamaliro chaubambo cha khalidwe Lake. Sikokwanira kuzindikira nzeru ndi chilungamo cha lamulo Lake, ndi kuona kuti lakhazikitsidwa pa mfundo yosatha ya chikondi. Mtumwi Paulo anaona zonsezi pamene anafuula kuti, ‘Ndikuvomereza kuti lamulo ndi labwino.’ ‘Lamulo ndi loyera, ndipo chilamulocho ndi choyera, cholungama, ndi chabwino.’ Koma anawonjezera, mu kuwawa kwa moyo wake ndi kusimidwa, kuti, ‘Ine ndine wathupi, wogulitsidwa ku tchimo.’ Aroma 7:16, 12, 14. Iye analakalaka chiyero ndi chilungamo, zimene mwa iye yekha analibe mphamvu yopezera, ndipo anafuula, ‘Ine munthu watsoka, ndani adzandilanditsa ku thupi ili la imfa?’ Aroma 7:24, kumapeto. Kulira kotereku kwakwera kuchokera ku mitima yolemetsedwa m’maiko onse ndi m’nthawi zonse. Kwa onse, yankho lake ndi limodzi lokha, ‘Onani Mwanawankhosa wa Mulungu, amene achotsa tchimo la dziko lapansi.’ Yohane 1:29.”—*Steps to Christ,* p. 19.

“Pali ambiri amene amazindikira kusathekera kwawo, ndipo amalakalaka moyo wauzimu umene ungawabweretse mu mgwirizano ndi Mulungu; koma akuyesera mopanda pake kuupeza. . . . Mpulumutsi akuweramira pa chinthu chimene anachigula ndi mwazi Wake, akunena ndi chifundo ndi chisoni chosafotokozeka kuti, ‘Kodi ufuna kuchiritsidwa?’”—*The Desire of Ages,* p. 203.

**b. Kodi Yakobo anatsimikiziridwa bwanji ndi Mulungu kuti sanasiidwe pamene anathawa m’bale wake Esau? Genesis 28:10–13.**

---

---

“[Yakobo] anamva kuti ali ngati wotayidwa, ndipo anadziwa kuti mavuto onsewa abwera chifukwa cha njira yake yolakwika. Mdima wa kusimidwa unalemera pa moyo wake, ndipo sanalimbikire ngakhale kupemphera. Koma anali yekhayekha kwambiri moti anamva kufunikira kwa chitetezo cha Mulungu monga sanamvere kale. Ndi kulira ndi kudzichepetsa kwakukulu anavomereza tchimo lake, ndipo anapempha umboni wakuti sanasiyidwe konse. Komabe mtima wake wolemetsedwa sunapeze mpumulo. Anataya chidaliro chonse mwa iye yekha, ndipo anaopa kuti Mulungu wa makolo ake wamukana.

“Koma Mulungu sanasiye Yakobo. Chifundo Chake chinapitiriza kufikira mtumiki Wake wolakwa ndi wosakhulupirira. Mwachifundo, Yehova anaonetsa Yakobo chimene ankafunikira, Mpulumutsi. Iye anachimwa, koma mtima wake unadzazidwa ndi chiyamiko pamene anaona njira yoonetsedwa imene akanabwezeretsedwanso ku chisomo cha Mulungu.”—*Patriarchs and Prophets,* p. 183.

## 5. KULUMIKIZA KUMWAMBA NDI DZIKO LAPANSI — Lachisanu, Julayi 9

**a. Kodi phunziro loti tiphunzire kuchokera pa makwerero amene Yakobo anaona m'chipululu ndi liti? Genesis 28:16, 17; Yohane 1:51.**

“M'masomphenya amenewo dongosolo la chiwombolo linaonetsedwa kwa Yakobo, osati lonse, koma mbali zimene zinali zofunika kwa iye pa nthawiyo. Makwerero achinsinsi amene anaonetsedwa kwa iye m'lotolo anali omwewo amene Khristu anatchula pokambirana ndi Natanayeli. [Yohane 1:51 kotedi]. Kufikira pa nthawi imene munthu anawukira boma la Mulungu, panali ubwenzi waulere pakati pa Mulungu ndi munthu. Koma tchimo la Adamu ndi Hava linalekanitsa dziko lapansi ndi kumwamba, kotero kuti munthu sakanathanso kukhala ndi chiyanjano ndi Mlengi wake. Komabe dziko silinasiidwe lokha lopanda chiyembekezo. Makwererowo akuimira Yesu, njira yosankhidwa yolankhulirana.”—*Patriarchs and Prophets,* p. 184.

**b. Fotokozani kulumikizana komwe kuyimira kwa Khristu kwakhazikitsa. Aroma 3:23–26; Ahebri 1:14.**

“Mu kupanduka, munthu anadzipatula kwa Mulungu; dziko lapansi linalekanitsidwa ndi kumwamba. Pa phompho limene linali pakati pake, sipakanakhoza kukhala chiyanjano. Koma kudzera mwa Khristu, dziko lapansi linalumikizananso ndi kumwamba. Ndi ubwino Wake mwini, Khristu wamanga mlatho pa phompho limene tchimo linapanga, kotero kuti angelo otumikira athe kukhala ndi chiyanjano ndi munthu. Khristu amalumikiza munthu wokugwa, wofooka ndi wosowa thandizo, ndi Gwero la mphamvu zopanda malire. . . .

“Mtima wa Mulungu umalakalaka ana Ake a pa dziko lapansi ndi chikondi choposa imfa. Popereka Mwana Wake, watitsanulira kumwamba konse mu mphatso imodzi. Moyo wa Mpulumutsi ndi imfa Yake ndi kupembedzera Kwake, utumiki wa angelo, kupempha kwa Mzimu, Atate akugwira ntchito pamwamba ndi kudzera mwa zonse, chidwi chosatha cha zolengedwa zakumwamba, zonsezi zikugwira ntchito m'malo mwa chiwombolo cha munthu.”—*Steps to Christ,* pp. 20, 21.

## MAFUNSO OBWERENZA PA WEKHA — Lachisanu n'chimodzi, Julayi 10

1. Yerekezerani chikhalidwe cha anthu atagwa ndi asanagwe.
2. Munthu atagwa, anachita chiyani ndipo chifukwa chiyani?
3. Kodi yankho lokhalo ku vuto la tchimo linali liti?
4. Fotokozani tanthauzo la chizindikiro chodabwitsa chimene chinapatsidwa kwa Yakobo m'lotolo.
5. Kodi Mulungu amasunga njira iti yolankhulirana ndi anthu?

# Kulapa

**Vesi Loloweza:** "Chifukwa chake lapani, bwererani kuti afafanizidwe machimo anu, kotero kuti zidze nyengo zakutsitsimutsa zochokera kunkhope ya Ambuye" (Machitidwe 3:19).

**Zowerenga Zoonjezera:** *Steps to Christ,* pp. 23–35.

"Mulungu sadzawataya iwo amene agwetsedwa mu uchimo koma iwo abwerera kwa Iye ndi kulapa kwenikweni."—*Patriarchs and Prophets,* pp. 202, 203.

## 1. CHISONI CHIFUKWA CHA TCHIMO — Loyamba, Julayi 12

**a. Kodi Yohane M'batizi anafuna umboni otani wa kulapa kwenikweni? Luka 3:7–14.**

______________________________________________________________________
______________________________________________________________________
______________________________________________________________________
______________________________________________________________________
______________________________________________________________________
______________________________________________________________________

"Kulapa kumaphatikizapo kumva chisoni chifukwa cha tchimo ndi kulisiya tchimolo. Sitidzasiya tchimo mpaka titaona kuipitsitsa kwake; mpaka titalisiya kuyambira mu mtima, sipadzakhala kusintha kwenikweni m'moyo."—*Steps to Christ,* p. 23.

**b. Kodi tiyenera kudziwa chiyani za kulapa kwenikweni komwe kumasintha mtima ndi moyo? 2 Akorinto 7:9, 10.**

______________________________________________________________________
______________________________________________________________________
______________________________________________________________________
______________________________________________________________________
______________________________________________________________________

"Chisoni chenicheni chifukwa cha tchimo ndi zotsatira za ntchito ya Mzimu Woyera. Mzimu amaonetsa kusayamika kwa mtima umene wapeputsa ndi kuvulaza Mpulumutsi, ndipo umatibweretsa ife mwachisoni ku mapazi a mtanda. Pa tchimo lililonse Yesu amavulazidwanso mwatsopano; ndipo tikayang'ana pa Iye amene tamubaya, timva chisoni chifukwa cha machimo amene abweretsa zowawa pa Iye. Kulira kotereku kudzatsogolera ku kusiya tchimo."—*The Desire of Ages,* p. 300.

"Pamene mtima wadzipereka ku chikoka cha Mzimu wa Mulungu, chikumbumtima chidzadzutsidwa, ndipo wochimwa adzazindikira za kuya ndi kupatulika kwa lamulo loyera la Mulungu, maziko a boma Lake kumwamba ndi pa dziko lapansi."—*Steps to Christ,* p. 24.

**a. Kodi pempho la Davide linali lotani pamene anazindikira kulemera kwa mlandu wake? Masalimo 51:1–4.**

____________________________________________________________

"Pemphero la Davide atagwa limasonyeza chikhalidwe cha chisoni chenicheni pa tchimo. Kulapa kwake kunali koona ndi kozama. Panalibe kuyesa kuchepetsa mlandu wake; panalibe chikhumbo chothawa chiweruzo choopsezedwa chimene chinasonkhezera pemphero lake. Davide anaona kuipitsitsa kwa kulakwa kwake; iye anaona kudetsedwa kwa moyo wake; iye anada tchimo lake. Sanangopempha chikhululukiro chokha, koma kupatsidwa chiyero cha mtima. Iye analakalaka chisangalalo cha chiyero, kubwezeretsedwa ku mgwirizano ndi chiyanjano ndi Mulungu."—*Steps to Christ,* pp. 24, 25.

**b. Kodi kulapa koona kwa Davide kunamutsogolera kufuna chiyani? Masalimo 51:10–13.**

____________________________________________________________

____________________________________________________________

"'Lengani mwa ine mtima woyera.' Uku ndikuyamba kwa bwino, pa maziko enieni a khalidwe lachikhristu; chifukwa mu mtima mumatuluka zinthu za moyo. Ngati onse, atumiki ndi anthu, angawone kuti mitima wawo uli bwino ndi Mulungu, tikanawona zotsatira zazikulu kwambiri kuchokera mu ntchito imene ikuchitika. Ntchito yanu ikakhala yofunika ndi yolemetsa kwambiri, m'pamene kufunikira kwa mtima woyera kumakhala kwakukulu. Chisomo chofunikira chaperekedwa, ndipo mphamvu ya Mzimu Woyera idzagwira ntchito ndi khama lililonse limene muchite pa njira imeneyi. Ngati mwana aliyense wa Mulungu akanamufunafuna Iye moona mtima ndi molimbika, kukula kwakukulu mu chisomo kukanakhalapo. Kusamvana kukanatha; okhulupirira akanakhala ndi mtima umodzi ndi malingaliro amodzi; chiyero ndi chikondi zikanalamulira m'mipingo. Tikamayang'ana, timasinthidwa. Mukaganizira kwambiri khalidwe la Khristu, mudzasandulika kwambiri mofanana ndi chifanizo Chake. Bwerani kwa Yesu mmene mulili, ndipo adzakulandirani, ndi kuyika nyimbo yatsopano m'kamwa mwanu, matamando kwa Mulungu."—*Gospel Workers* (1892), pp. 451, 452.

**c. Kodi Baibulo limaphunzitsa chiyani za kulapa ndi kudzipereka kwathunthu kwa Khristu? Aroma 2:4; Machitidwe 3:19; 5:31.**

____________________________________________________________

____________________________________________________________

"Sitingalape popanda Mzimu wa Khristu kudzutsa chikumbumtima, monga momwe sitingakhululukidwe popanda Khristu.

"Khristu ndiye gwero la chilimbikitso chilichonse chabwino. Iye yekha ndi amene angabzale mu mtima udani wa tchimo. Chikhumbo chilichonse cha choonadi ndi chiyero, ndi kuzindikira kulikonse kwa uchimo wathu, ndi umboni wakuti Mzimu Wake akugwira ntchito pa mitima yathu."—*Steps to Christ,* p. 26.

**a. Kodi kulapa kwa Esau, Farao, ndi Yudasi kunali kotani pamene anazindikira zotsatira za tchimo lawo? Ahebri 12:16, 17; Eksodo 12:30–32; 14:3–5; Mateyu 27:3–5.**

---

---

"Anthu ambiri amamva chisoni kuti achimwa ndipo amasintha khalidwe lawo la kunja chifukwa amaopa kuti zolakwa zawo zidzabweretsa zowawa pa iwo eni. Koma uku si kulapa m'lingaliro la Baibulo. Iwo amalira chifukwa cha kusautsika, osati chifukwa cha tchimo lenilenilo. Umenewu ndi mmene unalili ululu wa Esau pamene anaona kuti mwayi wake chifukwa choti anali oyamba kubadwa watayika kwamuyaya. . . . Yudasi Isikariote, atampereka Mbuye wake, anafuula, 'Ndachimwa pakuti ndapereka mwazi wosalakwa.' Mateyu 27:4.

"Kuvomereza kwake kunakakamizidwa kuchokera mu moyo wake wochimwa ndi kumva koopsa kwa mlandu wake ndi kuyembekezera kochititsa mantha kwa chiweruzo. Zotsatira zimene zimayembekezera kumugwera zinamudzaza ndi mantha, koma m'moyo mwake munalibe chisoni chozama, chakusweka mtima, kuti anapereka Mwana wa Mulungu wopanda banga ndi kukana Woyera wa Israeli. Farao, pamene anali kuvutika ndi ziweruzo za Mulungu, anavomereza tchimo lake kuti athawe chilango china, koma anabwerera ku kuchita mwano motsutsa Kumwamba miliri itangochotsedwa. Onsewa analira zotsatira za tchimo, koma sanamve chisoni ndi tchimo lenilenilo."—*Steps to Christ,* pp. 23, 24.

"Mulungu anapatsa Farao umboni woonekera kwambiri wa mphamvu yaumulungu, koma mfumu ija inakana kumvera kuunika. Kuwonetsedwa kulikonse kwa mphamvu yopanda malire kumene anakana, kunamupangitsa kukhala wotsimikiza kwambiri m'kupanduka kwake. Mbewu za kupanduka zimene anafesa pamene anakana chozizwitsa choyamba, zinabereka zipatso zake."—Patriarchs and Prophets, p. 268.

**b. Kodi chimachitika n'chiyani pamene wochimwa salapa ndipo achedwetsa kulapa kwake kuyembekezera kuti adzalapa nthawi ya mtsogolo? Yohane 12:35, 36; Ahebri 3:12–15.**

---

"Iwo amene amadzitcha a Khristu amene adzakumane ndi nkhondo yotsiriza yoopsayo osakonzekera, mukusautsika kwawo, adzavomereza machimo awo ndi mawu a ululu owawitsa pamene oipa akusangalala ndi mavuto awo. Kuvomerezaku ndi kwa khalidwe lomwelo longa la Esau kapena la Yudasi. Iwo amene amachita zimenezi amalira *zotsatira* za zolakwa zawo, osati mlandu wa zolakwazo. Samva kulapa kwenikweni, kapena kudana ndi choipa. Amavomereza tchimo lawo chifukwa choopa chilango; koma, monga Farao wakale, akadabwereranso ku kutsutsa kwawo Kumwamba ngati ziweruzo zikachotsedwa."—*The Great Controversy,* pp. 620, 621. [Zolemba zopendeka Mzaolemba.]

**a. Kodi kusiyana pakati pa Mfarisi ndi wamsonkho m'nkhani ya Khristu kunali kotani? Luka 18:10–13.**

______________________________________________________________________

"Mu fanizo la Mfarisi ndi wamsonkho, pemphero lodzimva kukhala wokwanira loti, 'Mulungu, ndikuyamika kuti sindili monga anthu ena onse,' linaima mosiyana kwambiri ndi pempho la wolapa loti, 'Mundichitire chifundo ine wochimwa.' Luka 18:11, 13, R. V., kumapetom. Motero Khristu anadzudzula chinyengo cha Ayuda."—*The Desire of Ages,* p. 495.

**b. Kodi Yesu ananena chiyani za zotsatira za pemphero la wamsonkho? Luka 18:14.**

______________________________________________________________________

______________________________________________________________________

"Wamsonkho wosauka uja amene anapemphera kuti, 'Mulungu, mundichitire chifundo ine wochimwa' (Luka 18:13), anadziwona yekha ngati munthu woipa kwambiri, ndipo ena anamuonanso iye kukhala wotere; koma anazindikira chosowa chake, ndipo ndi kulemera kwa mlandu wake ndi manyazi iye anabwera pamaso pa Mulungu, kupempha chifundo Chake. Mtima wake unali wotseguka kuti Mzimu wa Mulungu achite ntchito Yake ya chisomo ndi kumasula iye ku mphamvu ya tchimo. Pemphero lodzitama ndi lodzilungamitsa yekha la Mfarisi linasonyeza kuti mtima wake unali wotsekedwa kuletsa chikoka cha Mzimu Woyera. Chifukwa cha kutalikirana kwake ndi Mulungu, sanamve kudetsedwa kwake, mosiyana ndi ungwiro wa chiyero chaumulungu. Sanamve kusowa kulikonse, ndipo sanalandire kanthu."—*Steps to Christ,* pp. 30, 31.

**c. Pofotokoza nkhaniyi, kodi Yesu ankafuna kukonza maganizo ati owononga? Luka 18:9; 2 Akorinto 10:12; Miyambo 16:18.**

______________________________________________________________________

______________________________________________________________________

"Chipembedzo cha Mfarisi sichikhudza moyo. Iye sakufuna kufanana ndi Mulungu mu khalidwe, mtima wodzaza ndi chikondi ndi chifundo. Iye akukhutitsidwa ndi chipembedzo chokhudza moyo wa kunja wokha. Chilungamo chake ndi chake yekha, chipatso cha ntchito zake, ndipo chiweruzidwa ndi muyezo waumunthu.

"Aliyense amene amadzikhulupirira yekha kuti ndi wolungama, adzanyoza ena. Monga Mfarisi amadziweruza yekha podziyerekezera ndi anthu ena, choncho amaweruzanso ena potengera iye mwini. Chilungamo chake chimayesedwa ndi cha ena, ndipo akakhala oipa kwambiri, iye amaoneka wolungama kwambiri pofananiza. Kudzilungamitsa yekha kumamutsogolera kukuimba ena mlandu. 'Anthu ena' amawaweruza ngati ophwanya lamulo la Mulungu. Motero akuwonetsa mzimu womwewo wa Satana, woneneza wa abale. Ndi mzimu umenewu n'zosatheka kwa iye kulowa mu chiyanjano ndi Mulungu."—*Christ's Object Lessons,* p. 151.

## 5. MUSAUMITSE MTIMA WANU — Lachisanu, Julayi 16

**a. Kodi kuopsya kwa kusagonjera kukhudzika kapena kuzengereza kuyankha kukhudzikaku n'chiyani? 2 Akorinto 6:2; Ahebri 3:7, 8; Luka 12:20, 21.**

________________________________________

________________________________________

"Ambiri akukhazika pansi chikumbumtima chosautsika ndi malingaliro oti angathe kusintha njira ya zoipa pamene iwo eni afuna; kuti angaseweretse ndi mayitanidwe a chifundo, komabe n'kumakhudzikabe mobwerezabwereza. Iwo amaganiza kuti atatha kunyoza Mzimu wa chisomo, atatha kuponya chikoka chawo kumbali ya Satana, mu nthawi ya yoopsya yaikulu angathe kusintha njira yawo. Koma izi sizophweka kuchita choncho. Zodutsamo za moyo, maphunziro, a moyo wonse, amakhala asintha khalidwe kwambiri moti ochepa okha ndiwo amafuna kulandira chifanizo cha Yesu."—*Steps to Christ,* pp. 33, 34.

**b. Kodi tiyenera kuchita chiyani tikazindikira kuti mtima ndi moyo wathu sizili mu mgwirizano ndi Mulungu? Masalimo 139:23, 24; 51:10.**

________________________________________

________________________________________

________________________________________

"Phunzirani mawu a Mulungu mwapemphero. Mawu amenewo amayika pamaso panu, mu lamulo la Mulungu ndi mu moyo wa Khristu, mfundo zazikulu za chiyero, zimene popanda izi 'palibe munthu adzaona Mulungu.' Ahebri 12:14. Amatsutsa tchimo; amaonetsa momveka bwino njira ya chipulumutso. Amvereni wo ngati mau a Mulungu omwe akuyankhulidwa ku moyo wanu. . . .

"Ife takhala ochimwa kwambiri, koma Khristu anafa kuti tikhululukidwe. Ubwino wa nsembe Yake ndi wokwanira kutiyimira ife pamaso pa Atate. Iwo amene wawakhululukira kwambiri adzamukonda kwambiri, ndipo adzaima pafupi kwambiri ndi mpando Wake wachifumu kuti amtamande chifukwa cha chikondi Chake chachikulu ndi nsembe Yake yosasimbika. Ndi pamene timvetsa mokwanira chikondi cha Mulungu ndipamene timazindikira bwino kuipitsitsa kwa tchimo. Tikawona kutalika kwa unyolo umene unatsitsidwa chifukwa cha ife, ndipamene timamvetsetsa za nsembe yosasimbika imene Khristu anapereka m'malo mwathu, mtima umasungunuka ndi kuleza ndi kulapa."—Ibid., pp. 35, 36.

## MAFUNSO OBWEREZA PAWEKHA — Lachisanu n'chimodzi, Julayi 17

1. Kodi Mulungu amapereka mphatso yodabwitsa iti kuti tilandire chisomo cha kumwamba?
2. N'chifukwa chiyani patokha sitingalape moona mtima?
3. N'chiyani chinasowa mu kulapa kwa Esau, Farao, ndi Yudasi?
4. N'chifukwa chiyani Yesu ananena za fanizo la Mfarisi ndi wamsonkho?
5. Kodi sitepe yofunika kwambiri ndi iti yobweretsa munthu mu chiyanjano chapafupi ndi Mulungu?

LASABATA, JULAYI 25, 2026

Phunziro 4

# Kubvomereza

**Vesi Loloweza:** "Wobisa machimo ake sadzaona mwai; koma wakuwabvomereza ndi kuwasiya adzachitiridwa chifundo" (Miyambo 28:13).

**Zowerenga Zoonjezera:** *Steps to Christ,* pp. 37–41.

“Kuvomereza komwe kuli kutsanulidwa kuchokera mkati mwa moyo kumapeza njira yopita kwa Mulungu wachifundo chosatha.” — *Steps to Christ,* p. 38.

## 1. CHIFUNDO CHA MULUNGU — Loyamba, Julayi 19

**a. Pamene takhudzika ndi uchimo omwe tinachita, tikuyenera kuchita chiyani? Miyambo 28:13; Yakobo 5:16.**

___

___

“Zoyeneraza zoti munthu alandire chifundo cha Mulungu ndi zosavuta komanso ndi zolungama ndinso zanzeru. Ambuye safuna kuti tichite chinthu chinachake chopweteka ndi cholinga chakuti machimo athu akhululukidwe. Sitikuyenera kuyenda maulendo ataliatali komanso otopetsa, kapena kuchita mapemphero opweteka, kuti tipeze chivomerezo cha miyoyo yathu kwa Mulungu wakumwamba, kapena kuti atikhululukire machimo athu; koma iye amene avomereza machimo ake ndikuwasiya adzachitiridwa chifundo.”— *Steps to Christ,* p. 37.

**b. Kodi zimenezi zimafuna kuti tikhale ndi khalidwe lotani? Miyambo 15:33; 19:23; Masalmo 34:18.**

___

___

___

“Iwo amene sanadzichepetse pamaso pa Mulungu pozindikira kulakwa kwawo, sanakwaniritsebe mfundo yoyambirira ya kuvomereza. Ngati sitinachiteko kulapa koteroko komwe sichikuyenera kulapidwa, ndipo ngati sitinavomereze machimo athu modzichepetsa moona, komanso mwa mtima osweka, ndi kuda uchimo wathu, sitinafunefunepo chikhululukiro cha uchimo moona mtima; ndipo ngati sitinafunefunenepo, ndiye kuti sitinawupeze mtendere wa Mulungu. Chifukwa chokhacho chimene sitimakhululukidwa machismo omwe tanachita kale, ndi chakuti sitimafuna kudzichepetsa mitima yathu, komaso sitimafuna kugonjera ku zoyenerera za mawu a choonadi. Malangizo omveka bwino aperekedwa pankhani imeneyi. Kuvomereza tchimo, kaya kwa pagulu kapena mwa mtseri, kukuyenera kukhala kochokera pansi pa mtima, komanso kufotokozedwa momasuka.” —Ibid., pp. 37, 38

**a. Kodi timakhumudwitsanso ndani, pamene takhumudwitsa munthu wina? Masalmo 51:4.**

"Mtumwi akuti, 'Muvomerezane wina ndi mnzake machimo anu, ndipo mupempherane wina ndi m'nzake, kuti tichiritsidwe.' Yakobo 5:16. Vomerezani machimo anu kwa Mulungu, yekhayo amene angathe kukhululukira, ndi kuvomereza zolakwa zanu kwa wina ndi m'nzake. Ngati mwamukhumudwitsa m'nzanu kapena m'nansi wanu, mukuyenera kuvomereza zolakwa zanu, ndipo ndi udindo wake kukukhululukirani mwa ulere. Kenako mukuyenera kupempha chikhululukiro kwa Mulungu, chifukwa m'bale amene mwamuvulazayo mwini wake ndi Mulungu, ndipo pomuvulaza iye mwachimwira Mlengi wake ndi mombolo wake."—*Steps to Christ,* p. 37.

**b. Ndi chifukwa chani tikuyenera kuwakhululukira ena? Mateyu 6:14, 15; Aefeso 4:32.**

"Iye yemwe sakhululuka ena amadula njira yokhayo yomwe iye akanalandirira chifundo chochokera kwa Mulungu. Tisalingalire kuti timalungamitsidwa posawakhululukira iwo omwe ativulazawo, chifukwa choti iwo sanabwere kwa ife kudzavomereza cholakwacho. Ndi udindo wawo, mosakayikiranso, kuti adzichepetse mu kulapa ndi kuvomereza; koma tikuyenera kukhala nawo mzimu wachifundo kwa iwo amene atilakwira, posatengera kuti avomereza zolakwa zawo kapena ayi. Posatengera kuti ativulaza bwanji ife, sitikuyenera kusunga mangawa athu ndi kudzimvera chisoni tokha chifukwa cha kuvulazidwa kwathu; koma pamene tikuyembekezera kukhululukidwa machimo athu otsutsana ndi Mulungu, tiyenera kuwakhululukira onse omwe atichitira zoipa." —*Thoughts From the Mount of Blessing,* pp. 113, 114.

**c. Kodi ndi chayani chomwe chikuyenera kutiphunzitsa udindo wathu kwa anthu? 1 Petro 4:8; Aroma 13:8.**

"Muloleni Khristu, Moyo wa umulungu, akhale mwa inu, ndi kuti akavumbulutse za chikondi chochokera ku mwamba kudzera mwa inu, chomwe chingawutse chiyembekezo kwa anthu opanda chiyembekezo, ndikubweretsa mtendere wakumwamba ku mtima wosweka ndi uchimo. Pamene tikupita kwa Mulungu, chimenechi ndicho choyenerezo choti tichikwaniritse pamayambiriro pamene, kuti, polandira chifundo chochokera kwa Iye, timadzipereka tokha kuti tikawonetsere chisomo chake kwa ena."—Ibid., pp. 114, 115.

"Tchimo lathu lalikulu ndi kusowa kwa khalidwe la umunthu lochitirana kwa munthu mzathu. Ambiri amalingalira kuti akuwonetsera chilungamo cha Mulungu pomwe akulephereratu kuwonetsera kukoma mtima kwake ndi chikondi chake chachikulu. Kawirikawiri anthu amene iwo amakumana nawo mwaukali ndi mwa nkhanza amakhala ali pansi kulimbana ndi mayesero. Satana akulimbana nayo miyoyo imeneyi, ndipo mawu ankhanza, komanso opanda chisoni amawafooketsa ndi kuwapangitsa kuti agwere mu mphamvu ya wonyengayo."—*The Ministry of Healing*, p. 163.

**a. Kodi ndi machimo ati omwe akuyenera kuvomerezedwa poyera pamene ena akuyenera kubvomerezedwa kwa Mulungu yekha? Masalmo 32:5; Mateyu 5:23, 24.**

---

“Kuvomereza koona nthawi zonse kumakhala ndi khalidwe lachindunji, ndipo kumavomereza machimo ena ake. Iwo akhoza kukhala amtundu woti mkubweretsedwa kwa Mulungu yekha; akhozanso kukhala machimo omwe akuyenera kuvomerezedwa kwa anthu yemwe adavulazidwa chifukwa cha machimowo; kapena akhoza kukhala oti anachitidwa poyera, pa gulu la anthu, ndipo machismo otere ayenera kuvomerezedwa pagulunso. Koma kuvomereza konse kuyenera kukhala kolunjika, komanso komveka bwino, kuvomereza machimo eni eni omwe walakwitsa”—*Steps to Christ,* p. 38.

“Tchimo la mtseri likuyenera kuvomerezedwa kwa Khristu, yemwe ali mkhalapakati yekhayo pakati pa Mulungu ndi munthu. . . . Tchimo lililonse ndi mlandu pamaso pa Mulungu, ndipo likuyenera kuvomerezedwa kwa Iye kudzera mwa Khristu. Tchimo lililonse lapoyera liyenera kuvomerezedwanso poyera.”—*Gospel Workers,* p. 216.

**b. Kodi cholinga cha kubvomereza koona ndi chani? 1 Samueli 12:19.**

---

“M'masiku a Samueli, Aisrayeli anapatuka kuchoka kwa Mulungu. Iwo anali akuvutika ndi zotsatira za uchimo; chifukwa choti anataya chikhulupiriro chawo mwa Mulungu, nataya kuzindikira kwa mphamvu ndi nzeru Zake zolamulilira mtunduwo, anataya chidaliro chawo cha kuthekera kwake kowateteza ndi kuvumbulutsa njira Yake. Iwo anamusiya wolamulira wamkulu wa chilengedwe chonse, ndi kufuna kulamulidwa monga momwe mafuko owazungulira analili. Iwo asadawupeze mtendere adavomereza motsimikiza kuti: ‘Pamwamba pa zoipa zathu zonse tinaonjezerapo choipa ichi, chakuti tinadzipemphera mfumu.’ 1 Samueli 12:19. Tchimo lomwelo limene iwo anakhudzika nalo linayenera kuvomerezedwa.”—*Steps to Christ,* pp. 38, 39.

**c. Ndi machitachita otani omwe akuyenera kuchitidwa patsogolo pa kuvomereza? Yesaya 1:16, 17; Ezekieli 33:15.**

“Kuvomereza sikudzalandiridwa ndi Mulungu popanda kulapa moona mtima ndi kukonzanso. Pakuyenera kukhala kusinthika kotheratu m'moyo; chilichonse chomukhumudwitsa Mulungu chikuyenera kuchotsedwa. Ichi chidzakhala chotsatira chenicheni chomva chisoni ndi uchimo.” — Ibid., p. 39.

“Moyo uliwonse wotembenuka mtima, monga Zakeyu, udzawonetsera kulowa kwa Khristu mumtima mwake posiya machitidwe osalungama, omwe akhala ukudziwika nawo m'moyo wake. Monga mkulu wa msonkho, moyowo udzapereka umboni wa kuona mtima kwake kudzera mu kubwenzeretsa.”—*The Desire of Ages,* p. 556

**a. Pamene Ambuye anamufunsa Adamu ndi Hava za tchimo lawo, kodi iwo anawonetsera bwanji kuti silinali vuto lawo kwenikweni? Genesis 3:12, 13.**

---

“Adamu sakanatha kukana kapena kudzikanira za tchimo lake; koma m'malo mosonyeza kukhudzika mtima, iye anayesa kuyika mlandu wake pa mkazi wake, moteronso pa Mulungu Mwini: ndipo Iye anati, ‘Mkazi *amene Inu munandipatsa* kuti akhale nane anandipatsa ine chipatso cha mtengowo, ndipo ndinadya.’”—*Patriarchs and Prophets,* p. 57.

“Adamu ndi Hava atadya chipatso choletsedwa, iwo anagwidwa ndi mantha komanso manyazi. Pamayambiliro lingaliro lomwe anali nalo linali la momwe angalikanire tchimo lawo ndi kuthawa chilango choopsa cha imfa. Pamene Ambuye anawafunsa za tchimo lawo, Adamu anayankha, poyika mlanduwo mbali imodzo pa Mulungu ndi mbali ina pa bwenzi lake. ‘Mkazi *amene* Inu munandipatsa kuti akhale nane anandipatsa ine chipatso cha mtengowo, ndipo ndinadya.’ Ndipo Mkaziyo anayika mlandu wake pa njoka, nati, ‘Njoka inandinyenga ine, ndipo ndinadya.’ Genesis 3:12, 13. Chifukwa chani munapanga njoka? Ndi chifukwa chani munayilola kuti ibwere mu Edeni? Awa anali mafunso omwe amatanthawuza mukuwiringura kwake chifukwa cha tchimo lake, kotero kuti amamuyimba Mulungu mlandu pa kugwa kwawo.”—*Steps to Christ,* p. 40.

**b. Ndi chifukwa chani kudzilungamitsa kumapangitsa kuti kuvomereza kusakhale kopindulitsa? Yobu 9:20; Luka 16:15.**

---

---

“Mzimu wodzilungamitsa unayambira mwa atate wamabodza ndipo wakhala ukuonetseredwa ndi ana amuna ndi akazi onse a Adamu. Kuvomereza kwa dongosolo ili sikumatsogozedwa ndi Mzimu wa Mulungu, ndipo sikudzalandiridwa kwa Mulungu. Kulapa kwenikweni kudzamutsogolera munthu kunyamula mlandu wake yekha ndi kuwuvomereza mopanda bodza kapena chinyengo.”—Ibid., p. 40.

“Tisayesere kuchepetsa mlandu wathu podzikanira tchimo. Tivomereze mlingo umene Mulungu alionera tchimo, ndi kuti tchimolo ndi lalikuludi. Kalvari yekha angavumbulutse za koopsa ndi kuyipa kwa tchimo. Tikanawusenza mlandu wathu tokha, ukanatiphwanya. Koma m'modzi wosachimwayo watenga malo athu; ngakhale kuti sanayenera kutero, Iye wanyamula mphulupulu zathu. ‘Ngati tivomereza machimo athu, ali wokhulupirika ndi olungama Iye, kuti atikhululukire machimo athu, ndi kutisambitsa kutichotsera chosalungama chili chonse.’ 1 Yohane 1:9. Chowonadi chaulemerero! —olungama ku lamulo lake lomwe, komanso olungamitsa onse amene akhulupirira mwa Yesu. ‘Ndani Mulungu wofanana ndi Inu, wakhululukira mphulupulu, wakupitirira zolakwa za otsala a cholowa chake? Iye sasunga mkwiyo wake ku nthawi yonse, popeza akondwera nacho chifundo.’ Mika 7:18.”— *Thoughts from the Mount of Blessing,*116.

## 5. KUBVOMEREZA POYELA — Lachinayi, Julayi 23

**a. Kodi Paulo anavomereza bwanji tchimo lake modzichepetsa komanso mwachindunji? Machitidwe 26:10, 11.**

“Zitsanzo m’mawu a Mulungu za kulapa kwenikweni ndi kudzichepetsa zimawonetsera mzimu wa kuvomereza, womwe mulibemo chodzikanira cha uchimo kapena kuyesera kudzilungamitsa. Paulo sanafune kudziphimba yekha; Iye anapenta uchimo wake ndi mtundu wake wodetsetsa, sanayese kuwuchepetsa mlandu wake. [kuchokera pa Machitidwe 26:10, 11].”—*Steps to Christ,* p. 41.

**b. Kodi Paulo adanena kuti chani mu kalata wake woyamba wa kwa Timoteo? 1 Timoteo 1:15.**

“Mwa ife tokha sitingathe kuona chilichonse koma kufooka kokha, palibe chotiyenereza ife kwa Mulungu, ndipo Satana amatiuza kuti zilibe phindu; patokha sitingathe kuchiritsa makhalidwe athu oyipa. Pamene tikuyesela kubwera kwa Mulungu, m'dani amatinong'oneza kuti, kupemphera sikopindulitsa kwa inu; kodi inu simunachite choyipa chija? Kodi inu simunamuchimwire Mulungu ndi kuwononga chikumbumtima chanu? Koma tikhoza kumuza m’danyo kuti, ‘mwazi wa Yesu Khristu mwana Wake umatisambitsa kutichotsera uchimo wonse.’ 1 Yohane 1:7. Pemene tikudzimva kuti tachimwa ndipo sitingathenso kupemphera, imeneyo ndiyo nthawi yoyenera kupemphera. Kaya tingachite manyazi motani ndi kudzimva kuchepetsetsa kwambiri, komabe tiyenera kupemphera ndi kukhulupirira. [kuchokera pa 1 Timoteo 1:15]. Chikhululukiro. . . ndi mphatso yoperekedwa kwa ife, ndyokhala nacho chilungamo chopanda banga cha Khristu, maziko ake popeleka.”—*Thoughts from the Mount of Blessing,* pp. 115, 116.

**c. Kodi ndi chani chomwe Mulungu walonjeza, tikavomereza machimo athu? 1 Yohane 1:9.**

“Mtima wodzichepetsa ndi wosweka, wogonjetsedwa ndi kulapa kwenikweni, udzayamikira chinachake cha chikondi cha Mulungu ndi mtengo wa Kalvari; ndipo monga momwe mwana amavomerezera kwa atate wake wachikondi, momwemonso moyo wolapadi udzabweretsa machimo ake onse pamaso pa Mulungu. Ndipo kwalembedwa, [kuchokera pa 1 Yohane 1:9].”—*Steps to Christ,* p. 41.

## MAFUNSO OBWEREZA PAWEKHA — Lachisanu n’chimodzi, Julayi 24

1. Tikavomereza machimo athu kwa Mulungu mokhulupirika, kodi timayima bwanji pamaso pake?
2. Kodi ndi mu zochitika ziti zomwe kuvomereza kwina kukuyenera kuperekedwa kwa anthu ena, nanga ndi chifukwa chani?
3. Ndi chifukwa chani kuli kofunika kuti kuvomereza kukhale kolunjika?
4. Fotokozani kuopsa kwa kudzilungamitsa.
5. Kodi chotsatira cha kuvomereza modzichepetsa ndi chani?




# Zopereka Za Sabata Loyamba

Lasabata, Ogasiti 1, 2026

## Nthambi ya General Conference yowona za Maphunziro

“Phunzitsani mwana poyamba njira yake; Ndipo angakhale akakalamba sadzachokamo” (Miyambo 22:6).

Tikukhala m'nthawi zovuta. Pakati pa anthu moyo wa chikunja omwe ukuchulukirachulukirabe, udindo wophunzitsa ana athu ndi achinyamata athu kuwopa Ambuye wakhala wofunika kwambiri kuposa kale lonse. Monga makolo, aphunzitsi, ndi ziwalo za thupi la Khristu, tili ndi ntchito yopatulika yokonzetsera m'badwo womwe udzatha kuteteza chikhulupiriro molimba mtima, modzichepetsa, komanso motsimikiza mtima.

“Sayansi ya maphunziro enieni ndi chowonadi, chomwe chikuyenera kuzikika kwambiri m'moyo chomwe sichingachotsedwe ndi chinyengo chomwe chili ponseponse.”—*Testimonies for the Church,* vol. 6, p. 131.

Mu nkhani yi, Dipatimenti yowona za maphunziro ya la likulu la mpingo yakhala ikugwira ntchito molimbikila kuti ilimbikitse ndikukuza masukulu athu amaphunziro ofalitsa utgenga wa bwino padziko lonse lapansi. Malo athu ambiri a maphunziro alibe zomangamanga zokwanira, maphunziro amakono, ndi zida zogwirizana ndi zinthu zenizeni za uzimu za ophunzira athu. Kuphatikizapo, mayiko angapo apempha za kutsekulidwa kwa masukulu atsopano amaphunziro omwe samangolimbikitsa chidziwitso chamaphunziro okha komanso mfundo za uthenga wabwino wosatha.

Chopereka chapaderachi chithandizira madera atatu ofunikira:

1. Kukonzanso masukulu ofalitsira uthenga wabwino omwe alipo;
2. Kukhazikitsa masukulu atsopano m'madera omwe akufunika mwayi wopeza maphunziro achikhristu a SDARM;
3. Kupititsa patsogolo ntchito yomasulira ndi kusintha kwazipangizo zophunzitsira zomwe zapangidwa ndi gulu lathu lophunzitsa kuti litumikire masukulu akudziko ndi masukulumofalitsa utyenga wa bwino mu zilankhulo zosiyanasiyana komanso m'madera osiyanasiyana.

“Maphunziro owona ndi maphunziro ofalitsa uthenga wa bwino. Mwana aliyense wamwamuna ndi wamkazi wa Mulungu amayitanidwa kukhala ofalitsa uthenga wa bwino; tayitanidwa kutumikira Mulungu komanso anthu anzathu; ndipo kuti ife tikayenerezedwe kutumikira mu utumiki umenewu chukuyenera kukhala cholinga chofunikira cha maphunziro athu.”—*The Ministry of Healing,* p. 395.

Chifukwa chake, tikukupemphani, abale ndi alongo okondedwa, kuti mupereke chopereka chanu ndi mtima wonse komanso malibgaliro ofalitsa uthenga wa bwino. Kuyika ndalama zathu mu maphunziro a ana athu ndi achinyamata ndiko kuyika ndalama mu tsogolo la mpingo, kufalitsa uthenga wabwino, komanso mu kholola lomaliza.

Ambuye awonjezere zopereka zanu ndikulimbitsa utumiki wofunikawu—ndipo masukulu athu akhaledi nyali zowala mumdima, kukonzetsera gulu lokhulupirika lIkukakomana ndi Mpulumutsi wathu yenwe akubweranso posachedwa.

*Nthambi ya General Conference Yowona za Maphunziro*

# Kudzipereka

**Vesi Loloweza**: "Ndipo mudzandifunafuna Ine, ndi kundipeza, pamene mundifuna ndi mtima wanu wonse." (Yeremiya 29:13).

**Zowerenga Zoonjezera:** *Steps to Christ,* pp. 43–48.

"Ndizosatheka kuti ife mu mphamvu zathu kuchirimika mu nkhondoyi; ndipo chirichonse chomwe chimatichotsa malingaliro athu kwa Mulungu, chilichonse chomwe chimatitsogolera ife ku kudzikuza, kapena kudzidalira patokha, ndithu chimenecho chikukonzetsera njira ya kugwa kwathu. Mfundo yaikulu ya Buku lopatulika ndi kuphunzitsa kusadalira mphamvu za munthu koma kulimbikitsa kudalira mphamvu za Mulungu."—*Patriarchs and Prophets,* p. 717.

## 1. NKHONDO YOLIMBANA NDI UNDEKHA — Loyamba, Julayi 26

**a. Kodi Paulo anafotokoza bwanji za nkhondo yachikhristu ndi zida zake zofunikila pa nkhondoyi? Aefeso 6:12–18.**

_______________________________________________

_______________________________________________

"Satana analimbana ndi Khristu pogwiritsa ntchito mayesero ake owopsa komanso ovuta zedi kuwazindikira, komabe anakanika mu mkangano uliwonse. Nkhondo zimenezo zidamenyedwa m'malo mwathu; zigonjetso zimenezo zimatithandiza ife kuti tigonjetse. Khristu adzapereka mphamvu kwa iwo aomwe akuyifunafuna. Palibe munthu amene angathe kugonjetsedwa ndi Satana popanda munthuyo mwini kulorera. Woyesayo alibe mphamvu zolamulira chifuniro cha munthu kapena kuwukakamiza munthu kuti achimwe. Satana angathe kukhumudwitsa munthu, koma sangathe kumuyipitsa munthu. Angathe kuyambitsa zowawa, koma sangathe kumudetsa munthu. Choonadi chakuti Khristu anagonjetsa chikuyenera kuwalimbikitsa omutsatira ake molimbika mtima kuti ayimenye nkhondo mwamphamvu yolimbana Satana komanso uchimo."—*The Great Controversy,* p. 510.

**b. Kodi ndi kuti komwe Satana akuyesetsa kuti apeze ulamuliro kotheratu? Miyambo 4:23.**

_______________________________________________

_______________________________________________

"Monga momwe munthu 'asinkhasinkha mu mtima mwake, ali wotere.' Miyambo 23:7. Mtima ukuyenera kukonzedwanso ndi chisomo cha umulungu, apo ayi kukhala kwa chabe kufunafuna chiyero cha moyo. Iye amene amayesera kumanga khalidwe labwino, ndi lolungama popanda chisomo cha Khristu, akumanga nyumba yake pam'chenga wogwedezeka. Nyumbayo idzagwetsedwa ndithu mu mkuntho wamphamvu wa mayesero."—*Patriarchs and Prophets,* p. 460.

**a. Kodi ndi chani chomwe chikuyenera kutayidwa ndi cholinga chakuti tikhale ophunzira ake a Khristu? Luka 14:33; Mateyu 6:24.**

---

"Podzipereka tokha kwa Mulungu, tiyenera kusiya zonse zomwe zingatilekanitse ife ndi Iye. Chifukwa chake Mpulumutsi akuti, [kuchokera pa Luka 14:33]. Chilichonse chomwe chingawuchotse mtima kwa Mulungu chikuyenera kutayidwa. Chuma ndi fano la anthu ambiri. Chikondi cha ndalama, khumbo lofuna chuma, ndi unyolo wagolide womwe umawamangirira anthu kwa Satana. Kutchuka komanso ulemu wa dziko lapansi zimapembedzedwa ndi gulu lina la anthu. Moyo wa mtambasale, komanso ufulu wosakhala ndi udindo uliwonse ndi fano la ena. Koma ma unyolo a ukapolowa akuyenera kuphwasulidwa. Sitingakhale theka limodzi kwa Ambuye ndi theka linanso ku dziko lapansi. Sitili ana a Mulungu pokhapokha ngati sititakhala ana ake kwathunthu."—*Steps to Christ,* p. 44.

**b. Kodi ndi kuyitana kuti kwa umulungu komwe Ambuye akupereka kwa onse amene akufuna moyo watsopano ndi mtima watsopano? Yesaya 1:18; Yeremiya 29:13; Yakobo 4:7–10.**

"Ulamuliro wa Mulungu, suli ngati monga momwe Satana amawuwonetsera, kuti ndi wokhazikidwa pa kugonjera mosazindikira, kapena ulamuliro wopanda nzeru. Ulamulirowu umakopa nzeru ndi chikumbumtima. . . . Mulungu samakakamiza chifuniro cha zolengedwa zake. Iye sangalandire ulemu womwe superekedwa mwa ufulu komanso mwanzeru. Kugonjera kokakamizidwa kokha kutha kulepheretsa kukula kwenikweni kwa malingaliro komaso kwa khalidwe; kugonjera kotereku kutha kumupangitsa munthu kukhala chinthu chongolamulildwa mopanda ufulu wosankha. Chimenecho sicholinga cha Mlengi. Iye amafuna kuti munthu, yemwe ndi ntchito yayikulu ya mphamvu yake ya kulenga, akafikile pamlingo wosinthika wapamwamba womwe iye angathe kuufikira. Mulungu amayika pamaso pathu madalitso apamwamba omwe amafuna atatibweretsera ife kudzera mu chisomo chake. Iye akutiyitana ife kuti tidzipereke kwa Iye, kuti Iye akachite chifuniro chake mwa ife. Zili kwa ife kusankha kumasulidwa ku ukapolo wa uchimo, kuti tigawane nawo ufulu waulemerero wa ana a Mulungu."— Ibid., pp. 43, 44.

"Khristu anawonetsedwa ngati mpulumutsi wa anthu. Anthu samayenera kumadalira mu ntchito za iwo eni, ndi mu chilungamo cha iwo eni, kapena mwa iwo okha mu njira ina iliyonse, koma mwa mwana wa Nkhosa wa Mulungu amene achotsa machimo a dziko lapansi. Woyimira Atate anavumbulutsidwa mwa Iye. Kuyitana kunaperekedwa kudzera mwa Iye, kuti 'Tiyeni tsono, tiweruzane,' atero Yehova: ngakhale zoyipa zanu ziri zofiira, zidzayera ngati matalala; ngakhale ziri zofiira ngati kapezi, zidzakhala ngati ubweya wa nkhosa woti mbu.' Kuyitana kumeneku kukufikiranso momveka bwino kwa ife lero lino. Musalole kuti kunyada, kapena kudzikuza, kapena kudzilungamitsa kuti kulepheretse wina aliyense kuvomereza machimo ake, kuti alandire lonjezano."—*Fundamentals of Christian Education,* p. 239.

**a. Kodi ndi chani chomwe chamupatsa Khristu ufulu wowatengera ana Ake kumwamba? Akolose 1:14; Ahebri 7:25.**

---

“Mkati mwa m'dima woopsa, womwe unkawoneka kuti unasiyidwa ndi Mulungu, Khristu anachotsamo madontho omaliza a mu chikho cha tsoka la anthu. Mu maola owopsa amenewo, Iye anadalira pa umboni wokuvomereza kwa Atate Wake womwe unaperekedwa kwa Iye m’buyomo. Iye ankadziwa bwino khalidwe la Atate Wake; Iye anamvetsa chilungamo Chake, chifundo Chake, ndi chikondi Chake chachikulu. Mwa chikhulupiriro Iye anapumula mwa Iye, amene chinali Chimwemwe chake kumumvera. Ndipo monga mukugonjera Iye anadzipeleka Yekha kwa Atate, lingaliro losiiyidwa mu chikondero cha Atate Wake linachotsedwa. Mwa chikhulupiriro, Khristu anali wogonjetsa.”—*The Desire of Ages,* p. 756.

“Mu mphatso ya Yesu, Mulungu anapereka kumwamba konse. Kutengera malingaliro a munthu, nsembe yotereyi inali kutaya chabe. Mu malingaliro a munthu, dongosolo lonse la chipulumutso ndi kutaya chifundo komanso zinthu zofunikira. Kudzikana komanso kudzipereka nsembe kwa mtima wonse zimatipeza kwina kulikonse. Khamu lakumwamba lingayang’ane modabwitsika ndi banja la anthu lomwe likukana kukwezedwa komanso kudzadzidwa ndi chikondi chopanda malire, chomwe chawonetsedwa mwa Khristu. Kotero angafuule niti, Chifukwa chani kutaya kwakukulu kotereku?

“Koma chitetezero cha dziko lotayika chinayenera kukhala chodzaza, chochuluka, komano chokwanira. Msembe ya Khristu inali yochuluka kwambiri kufikira moyo wina uliwonse womwe Mulungu adawulenga. Sikukanatheka kuyikidwa malire kuti chiwerengero cha omwe angalandire Mphatso yayikuluyo chisapitirire. Anthu onse sanapulumutsidwe; komabe dongosolo la kuwombola si kutaya chabe chifukwa choti silikukwaniritsa zonse zomwe ukoma mtima wake waperekedwera. Payenera kukhala zokwanira komanso zotsala.”—Ibid., pp. 565, 566.

**b. Kodi Yesu amafuna chani kwa onse amene akufuna kukhala ana ake ndi kufuna kulandira Mzimu wake? Miyambo 23:26.**

---

[Yesu] akuyembekezera mwachifundo kuti amve kuvomereza kwa a anthu osochera, ndi kulandira kulapa kwawo. Iye amayang'ana kubwezera kwa chiyamiko kuchokera kwa iwo, monga momwe mayi amayang'anira kumwetulira kochokera kwa mwana wake wokondedwa. Mulungu wamkulu amatiphunzitsa ife kumutchula Iye Atate. Iye akufunitsitsa kuti ife timvetsetse momwe mtima wake umatifunira mwakhama, komanso mwachifundo mu mayesero ndi mu masautso athu onse.”— *Gospel Workers,* p. 210.

“Kodi timataya chani, tikapereka zonse? Mtima wodetsedwa ndi uchimo, kuti Yesu awuyeretse, nawutsuke ndi mwazi wake, ndi kutipulumutsa kudzera mu chikondi chake chosayerekezeka. Komabe anthu amaganiza kuti ndi zovuta kutaya zonse! Ndili ndi manyazi pomva zomwe izi zikulankhulidwa, ndili ndi manyazi kulemba zimenezi.”—*Steps to Christ,* p. 46.

**a. Kodi khumbo lalikuru la Paulo kwa okhulupirira linali chiyani? Aroma 12:1; 1 Atesalonika 5:23.**

____________________________________________________________________

____________________________________________________________________

"Ngakhale zinenedwa kwa Israyeli wakale, mawu awa alinso ndi phunziro kwa anthu a Mulungu m'masiku ano. Pamene mtumwiyo anandaulira abale ake kuti apereke matupi awo 'nsembe yamoyo, yopatukika, yokondweretsa Mulungu,' iye anakhazikitsa mfundo za chiyeretso chenicheni. Sikuti chimenechi ndi chiphunzitso chabe, kapena malingaliro chabe, kapena mtundu wamawu chabe, koma ndi mfundo yamoyo, yogwira ntchito, mu moyo watsiku ndi tsiku. Mfundoyi imafuna kuti zizolowezi zathu za madyedwe, mamwedwe, ndi mavalidwe zikhale zotetezera thanzi lathu la thupi, thanzi la malingaliro, ndi thanzi la makhalidwe abwino, kuti tipereke kwa Ambuye matupi athu, osati chopereka choyipitsidwa ndi zizolowezi zolakwika, koma 'nsembe yamoyo, yopatukika, yokondweretsa Mulungu.'"— *The Sanctified Life,* pp. 27, 28.

"Tikuyenera kudzipereka tokha ku utumiki wa Mulungu, ndipo tikuyenera kuyesetsa kupereka pafupifupi chopereka changwiro mukuyesetsa kwathu konse. Mulungu sadzakondwera ndi chochepereka chilichonse chotsika kuposa chabwino chomwe ife tingapereke. Iwo amene amkonda Iye ndi mtima wonse, adzafunitsitsa kumupatsa Iye utumiki wabwino zedi wa moyo, ndipo nthawi zonse iwo adzakhala akuyesetsa kubweretsa mphamvu zawo zonse za umunthu kuti zikagwirizane ndi malamulo omwe adzalimbikitsa kuthekera kwawo kochita chifuniro chake."—*Patriarchs and Prophets,* pp. 352, 353.

**b. Pamene khamu la anthu linamva nkhani ya Petro pa tsiku la Pentekoste, kodi ndi chiyani chomwe chidalemetsa mitima yawo? Machitidwe 2:37, 38.**

____________________________________________________________________

____________________________________________________________________

"[Khamulo] linamva ophunzira akunena kuti anali Mwana wa Mulungu amene anapachikidwa uja. Ansembe komanso olamulira ananjenjemera. Kusweka mtima ndi chisoni chachikulu zinawakhudza anthuwo. "Analaswa mtima mwawo, natitu kwa Petro ndi atumwi enawo, 'Tidzachita chani amuna inu, abale?" Mkati mwa iwo omwe amkawamvetsera ophunzirawo panali Ayuda odzipereka, omwe anali owona mtima mu chikhulupiriro chawo. Mphamvu yomwe inatsogolera mawu a mlalikiyo inawatsimikizira kuti Yesu analidi Mesiya. . . .

"Petro anawatsimikizila anthu okhudzikawo kuti anakana Khristu chifukwa choti ananamizidwa ndi ansembe komanso ndi owalamulira; ndi kuti ngati akanapitirizabe kuyang'ana kwa anthu awa kuti apeze uphungu, ndi kuyembekezera kuti iwo amuvomereze Khristu, iwo eni asanachite zimenezo, sangathekumulandira Iye. Amuna amphamvu amenewa, ngakhale ankadzinenera kuti ndi a umulungu, anali ndi cholinga chofuna chuma ndi ulemerero wa dziko lapansi. Samkafuna kubwera kwa Khristu kuti alandire kuunika."—*The Acts of the Apostles,* pp. 43, 44.

## 5. KUPITIRIZA KUDZIPEREKA — Lachisanu, Julayi 30

**a. Ndi chani chomwe chimabweretsa kukhudzika kuti tidzipereke kwathunthu kwa Ambuye ndi kutha kuwonetsera chifaniziro cha Khristu? Afilipi 2:12, 13.**

“Mulungu sakukuuzani kuti mudzichita mantha kuti Iye adzalephera kukwaniritsa malonjezo Ake, kapena kuti kuleza mtima Kwake kudzatopa, kapena kuti chifundo Chake chidzaperewera. Chitani mantha kuti chifuniro chanu mwina sichidzagonjera ku chifuniro cha Khristu, kuti makhalidwe anu obadwa nawo ndi zizolowezi zanu zingadzalamulire moyo wanu. ‘Pakuti wakuchita mwa inu kufuna ndi kuchita komwe chifukwa cha kukoma mtima kwake ndiye Mulungu.’ Chitani matha kuti mwina undekha udzalowerera pakati pa moyo wanu ndi Mphunzitsi wamkulu. Chitani mantha kuti mwina chifuniro chanu chidzawononga cholinga chachikulu chomwe Mulungu anafuna kuchikwaniritsa kudzera mwa inu. Chitani mantha mukudalira mu mphamvu zanu, chitani mantha mukuchotsa dzanja lanu mu dzanja la Khristu ndi kuyesa kuyenda mu njira ya m’moyo popanda kupezekapo Kwake kosatha.”—*Christ’s Object Lessons,* p. 161.

**b. Ndimotani momwe kukhazikika mu chikhulupiriro ndi kudzipereka kwathunthu ku mfundo zoyenera kungachirikizidwire? Agalatiya 2:20; Mateyu 16:24, 25.**

“Iwo amene akufuna kulandira dalitso la kuyeretsedwa akuyenera koyambirira kuphunzira tanthauzo la kudzipereka msembe. Mtanda wa Khristu ndiwo mzati wapakati womwe pa pachikidwapo ‘ulemerero wolemera woposa waukulu kwambiri ndi wosatha.'”—*The Acts of the Apostles,* p. 560.

“Simungathe kuwusintha mtima wanu, simungathe pa nokha kupeleka chikondi cha mtima wanu kwa Mulungu; koma mungathe kusankha kumutumikira Iye. Mutha kumupatsa Iye chifuniro chanu; Kenako adzagwira ntchito mwa inu kuti mufune ndi kuchita mogwirizana ndi zomukondweretsa Iye. . . .

“Kudzera mu kugwiritsa ntchito bwino chifuniro chanu, kusinthika kwaphumphu kudzachitika m’moyo wanu. Popereka chifuniro chanu kwa Khristu, mumadzigwirizanitsa ndi mphamvu yomwe ili pamwamba pa maulamuliro ndi phamvu zonse. Mudzakhala ndi mphamvu yochokera kumwamba yoti ikulimbitseni, kotero kuti kudzera mu kudzipereka kosalekeza kwa Mulungu mudzapangidwa kukhala ndi moyo watsopano, ingakhalenso moyo wa chikhulupiriro.”—*Steps to Christ,* pp. 47, 48.

## MAFUNSO OBWEREZA PAWEKHA — Lachisanu n’chimodzi, Julayi 31

1. Kodi chofunika ndi chani kuti tikapambane mu nkhondo yolimbana ndi m’dani wa miyoyo yathu?
2. Kodi nkhondo yeniyeni ndiiti kuti tikamugonjetse m'dani wogonjetsedwa kale?
3. Kodi tingaphunzirepo chani kuchokera mu mphatso ya Khristu ya chipulumutso chathu?
4. Kodi cholinga cha Mulungu kwa okhulupirira n’chani, kuthupi ndi ku uzimu?
5. Ngati chifuniro chathu chikugwirizana ndi chifuniro cha Mulungu, ndi chani chomwe chidzachitike tsiku ndi tsiku?

# Chikhulupiriro ndi Kubvomereza

**Vesi Loloweza:** “Ndipo ndidzakupatsani mtima watsopano, ndi kulonga m'kati mwanu mzimu watsopano; ndipo ndidzachotsa mtima wamwala m'thupi, ndi kukupatsani mtima wamnofu” Ezekiele 36:26

**Zowerenga Zoonjezera:** *Steps to Christ, chapter 6, pp. 49–55.*

“Simungathe kuzitetezera machimo anu akale; simungathe kusintha mtima wanu ndi kudzipanga nokha kukhala woyera. Koma Mulungu walonjeza kukuchitiraniti izi zonse kudzera mwa Khristu.”—*Steps to Christ, p. 51.*

## 1. CHIKHULULUKIRO NDI MTENDERE — Loyamba, Ogasti 2

**a. Kodi ndi lonjezo lodabwitsa lanji la Mulungu la Chikhululukiro ndi mtendere? 1 Yohane 1:9**

______________________________________________________________________

______________________________________________________________________

______________________________________________________________________

“Mukuona kuti moyo wanu wadzazidwa ndi kudzikonda ndi uchimo. Mukulakalaka kukhululukidwa, kuyeretsedwa, kumasulidwa. Chiyanjano ndi Mulungu, kufanana ndi Iye – Mungachite chiyani kuti muchilandire?

“Ndi mtendere umene mukusowekera—Chikhululukiro cha Kumwamba ndi mtendere ndi chikondi m’moyo. Ndalama sizingagule ichi, luntha silingagule, nzeru siingachifikire; simungayembekeze, mwa kuyesetsa kwanu, kuchipeza. Koma Mulungu akupereka kwa inu monga mphatso, ‘opanda ndalama ndi opanda mtengo wake.’ Yesaya 55:1. Ndi chanu ngati mukufuna ndikutambasulira dzanja lanu ndikuchigwira ichi.”— *Steps to Christ, p. 49.*

**b. Kodi ndi lonjezo lina lotani lofunika limene lidzasanduliza umunthu kukhala munthu watsopano wogwirizana ndi Mulungu? Ezekieli 36:26.**

______________________________________________________________________

______________________________________________________________________

______________________________________________________________________

______________________________________________________________________

“Mwaulula machimo anu, ndi kuwachotsa mu mtima. Mwatsimikiza mtima kudzipereka nokha kwa Mulungu. Tsopano pitani kwa iye, ndikumupempha kuti akuchotsereni machimo anu ndi kukupatsani mtima watsopano. Ndiye khulupirirani kuti Iye amachita izi *chifukwa Iye walonjeza*. Ili ndi phunziro limene Yesu adaphunzitsa pamene Iye anali padziko lapansi, kuti mphatso imene Mulungu anatilonjeza ife, tiyenera kukhulupirira ife kuti tilandira, ndipo ndi chathu.”—*Steps to Christ, pp. 49, 50*.

**a. Kodi Yesu anauza wakufa ziwalo ku Betesida kuti achite chiyani, ndipo ife tingaphunzirepo chiyani pa zimene zinachitikazi? Yohane 5:1—9.**

“Tiyeni titembenukire ku nkhani ya wakufa ziwalo wa ku Betesida.Wovutika wosaukayo analibe thandizo; anali asanagwiritseko ntchito miyendo yake kwa zaka makumi atatu kudza zisanu ndi zitatu. Koma Yesu anamuuza kuti, ‘Nyamuka, yalula mphasa yako, nuyende.’ Munthu wodwala akanatha kunena , ‘Ambuye ngati mundichiritsa, ndidzamvera mawu anu.’ Koma, ayi, iye anakhulupirira mawu a Khristu, anakhulupirira kuti anachiritsidwa, ndipo anachita khama nthawi yomweyo; anafuna kuyenda, nayendadi. Iye anachita pa mawu a Khristu, ndipo Mulungu anapereka mphamvu. Anachiritsidwa.”— *Steps to Christ, p. 50.*

“Yesu sanamutsimikizire kuti Mulungu amuthandiza. Munthuyo akanatha kuima ndikukayikira, ndikutaya mwayi wake umodzi wochiritsidwa. Koma iye anakhulupirira Mawu a Kristu, ndipo m’kuchita mwa iwo analandira mphamvu.

“Kupyolera mu chikhulupiriro chomwecho tidzalandira machiritso auzimu. Mwa uchimo ife tinadulidwa kuchoka ku moyo wa Mulungu. Miyoyo yathu ndiyakufa. Mwa ife tokha sitingathe kukhala moyo wachiyero monga momwe munthu uja analiri wopanda mphamvu wosakhoza kuyenda. Pali ambiri omwe amazindikira kusowa thandizo kwawo, ndi amene amalakalaka moyo wauzimu omwewo umene udzawabweretse mu m’gwirizano ndi Mulungu; akungolimbikira mwachabe kuupeza. Pothedwa nzeru amafuula kuti, ‘munthu wosauka ine! adzandilanditsa ndani m’thupi la imfa iyi? Aroma 7:24. Lolani anthu okhumudwa awa, ovutikirawa ayang'ane m'mwamba. Mpulumutsi akuweramira pa ogulidwa ndi mwazi Wake, akunena ndi chikondi chosaneneka ndi chisoni, ‘Kodi ukufuna kuchiritsidwa?’ Iye akukuitanani kuwuka mu thanzi ndi mtendere.”— *The Desire of Ages, p. 203.*

**b. Kodi wochimwa akulonjezedwa chiyani kudzera mwa Khristu? 2 Mbiri 7:14; Hoseya 14:4**

“Simungathe kuzitetezera machimo anu akale; simungathe kusintha mtima wanu ndikuzipanga nokha kukhala woyera. Koma Mulungu walonjeza kuti adzakuchitirani zonsezi kudzera mwa Khristu. Inu *khulupilirani* lonjezoli. Wululani machimo anu ndikuzipereka nokha kwa Mulungu. *Funani* kumutumikira Iye. Mofanana ndi momwe mukuchitira izi, Mulungu adzakwaniritsa Mawu ake kwa inu. Ngati mukhulupirira lonjezo—kukhulupirira kuti mwakhululukidwa ndi kuyeretsedwa—Mulungu amapereka chowonadi; wachiritsidwa monga momwe Khristu anapatsa wakufa ziwalo mphamvu yoyenda pamene munthuyo anakhulupirira kuti iye anachiritsidwa. Zili choncho ngati mukhulupirira.

“Musadikire kuti *mumve* kuti mwachiritsidwa, koma nenani kuti, ‘Ndikukhulupirira; zili choncho, osati chifukwa ndikumva choncho, koma chifukwa Mulungu walonjeza.’ ” — *Steps to Christ, p. 51.*

**a. Pamene Yesu walandiridwa ngati Mpulumutsi, kodi chimachitika ndi chiyani ku machimo akale? Aroma 3:24, 25; 5:1, 9, 10.**

_________________________________________________________________

"Yesu anati, 'Zinthu zirizonse mukazipemphera ndi kuzipempha, khulupiriranі kuti mwazilandira, ndipo mudzakhala nazo.' Marko 11:24 . Pali chifukwa ku lonjezo ili—kuti tipemphere monga mwa chifuniro cha Mulungu. Koma ndi chifuniro cha Mulungu kutiyeretsa ife ku uchimo, kutipanga ife kukhala ana ake, ndi kutipangitsa ife kukhala ndi moyo woyera. Choncho tikhoza kupempha madalitso amenewa, ndi kukhulupirira kuti tazilandira, ndi kuthokoza Mulungu kuti tazilandira. Ndi mwayi wathu kupita kwa Yesu ndi kuyeretsedwa, ndi kuima pachilamulo opanda manyazi kapena chisoni."— *Steps to Christ, p. 51.*

**b. Kodi wokhulupirira ali ndi kaimidwe kotani pamaso pa Mulungu? Aroma 8:1.**

_________________________________________________________________

_________________________________________________________________

"Pamene moyo wa Mkhristu udzakhala wodzicepetsa, suyenera kukhala wachisoni ndi kuzinyazitsa. Ndi mwayi wa aliyense kuti akhale ndi moyo kuti Mulungu amuvomereze ndi kumudalitsa. Si chifuniro cha Atate wathu wakumwamba kuti tikhale otsutsidwa nthawi zonse ndi mdima. Palibe umboni wa kudzichepetsa kwenikweni pakupita ndi mutu utaweramitsidwa pansi komanso mtima wodzaza ndi maganizo aundekha. Tikhoza kupita kwa Yesu ndi kuyeretsedwa, ndi kuyima pa chilamulo opanda manyazi ndi chisoni."— *The Great Controversy, p. 477.*

"Pamene tidzipereka tokha kwathunthu kwa Mulungu, ndi kukhulupirira kwathunthu, mwazi wa Khristu umatsuka ku machimo onse. Chikumbumtima chikhoza kumasulidwa kukutsutsidwa. Kupyolera mu chikhulupiriro mu mwazi wake, onse akhoza kukhala angwiro mwa Yesu Khristu. . . . Sitiyenera kuda nkhawa ndi zomwe Khristu ndi Mulungu amaganiza za ife, koma zimene Mulungu amaganiza za Khristu, wolowa m'malo mwathu. Inu muli wolandiridwa mwa Wokondedwa."—*Selected Messages, bk. 2, pp. 32, 33*

**c. Kodi ndi kusintha kotani kumene kuyenera kuzindikirika ndi onse omwe adalowa mu pangano la ubale ndi Mulubgu ili? 1 Petro 1:18, 19; 1 Akorinto 6:19; 20; Agalatiya 3:26.**

_________________________________________________________________

_________________________________________________________________

"Kuyambira tsopano simuli a inu nokha, munagulidwa ndi mtengo wake." ( 1 Petro 1:18, 19 ) Kupyolera mu mchitidwe wopepuka uwu wa kukhulupirira Mulungu, Mzimu woyera wabala moyo watsopano mu mtima mwanu. Ndinu mwana wobadwira mubanja la Mulungu, ndipo Iye amakukondani monga momwe amakondera Mwana wake."— *Steps to Christ, pp. 51, 52.*

**a. Kodi wokhulupirira ayenera kukhala ndi makhalidwe otani? Akolose 2:6.**

---

“Tsopano popeza mwadzipereka kwa Yesu, musabwerere m’mbuyo, musazitengere kutali ndi Iye, koma tsiku ndi tsiku muzinena kuti, ‘Ine ndine wa Khristu; Ndadzipereka ndekha kwa Iye;’ ndipo mpempheni kuti akupatseni Mzimu Wake ndi kukusungani mwa chisomo Chake. Monga momwe zilili pakudzipereka nokha kwa Mulungu, ndi kumukhulupirira Iye, kuti mukhale mwana Wake, kotero muyenera kukhala mwa Iye. Mtumwiyo akuti, ‘Chifukwa chake monga munalandira Kristu Yesu Ambuye, yendani mwa Iye.’ Akolose 2:6 .

"Ena akuwoneka kuti akuganiza kuti ayenera kukhala pa chitetezero, ndipo ayenera kutsimikizira Ambuye kuti iwo akonzedwanso, iwo asanatenge madalitso Ake. Koma iwo akhoza kutenga madalitso a Mulungu ngakhale tsopano. Iwo ayenera kukhala nacho chisomo Chake Mzimu wa Khristu, kuthandiza zofowoka zawo, kapena sangathe kukaniza zoipa. Yesu amakonda kuti ife tibwere kwa Iye monga ife tiri, ochimwa, opanda thandizo, odalira. Ife tingabwere ndi kufooka kwathu konse, kupusa kwathu, uchimo wathu, ndi kugwa pa mapazi Ake mu kulapa. Ndi ulemerero Wake kutizungulira ife m'manja mwa chikondi chake ndikumanga mabala athu, kutisambitsa kutichotsera zodetsa zonse.”— *Steps to Christ, p. 52.*

**b. Ndi thandizo lanji lokonzedweratu ku zophophonya zomwe zimachitika mu dongosolo lakuphunzira? 1 Yohane 2:1, 2.**

---

“Chotsani kukayikira kuti malonjezo a Mulungu sanakonzedwere inu. Ndi a aliyense wolapa moona. Mphamvu ndi chisomo zaperekedwa kudzera mwa Khristu kuti zibweretsedwe ndi angelo otumikira ku moyo uliwonse wokhulupilira. Palibe amene ali ochimwitsitsa mpaka kuti sangapeze mphamvu, chiyero, ndi chilungamo mwa Yesu, amene adawafera iwo. Akuyembekezera kuwavula iwo zobvala zawo zamabanga ndi zodetsedwa ndi uchimo, ndikuwaveka iwo miinjiro yoyera ya chilungamo; Iye akuwalamula kuti akhale ndi moyo osafa ayi.” *–Ibid., pp. 52, 53*

**c. Fotokozani m’mene timalimbikitsidwira paulendowu. 1 Yohane 1:7; Agalatiya 5:16, 17, 25.**

---

“Iwo amene akuyenda m’njira zanzeru alinso m’masautso, ali opambana chimwemwe; pakuti Iye amene moyo wawo umkonda ayenda pambali pawo wosaoneka. Pa Kukwera kulikonse amazindikira momveka bwino kukhudza kwa dzanja Lake; ku masitepe aliwonse kunyezimira kwa ulemerero wochokera kobisika kumagwera pa njira zawo; ndipo nyimbo zawo za matamando, zokwera kwambiri, zimakwera mpaka kulumikizana ndi nyimbo za angelo pamaso pa mpando wachifumu.”— *Thoughts from the Mount of Blessings, p. 140.*

## 5. CHIKONDI CHA ATATE CHOWOMBOLA — Lachisanu, Ogasti 6

**a. Kodi zofunikira kuti tivomerezedwe ndi Mulungu ndi chiyani? Yesaya 55:7; 44:22.**

______________________________________________________________

______________________________________________________________

"Mulungu samachita nafe monga anthu okhala ndi malire amachitirana wina ndi mnzake. Zolingalira zake ndizo za chifundo, chikondi, ndi chifundo chachikulu."— *Steps to Christ, p. 53.*

"Aliyense amene pansi pa chidzudzulo cha Mulungu adzachepetsa moyo wake ndi kuvomereza ndi kulapa, monga Davide adachitira, akhale ndi chitsimikizo kuti chiyembekezo chilipo. Aliyense amene avomereza mwa chikhulupiriro malonjezo a Mulungu, adzapeza chikhululuko. Ambuye sadzataya konse munthu ngakhale m'modzi wolapa moona."— *Patriarchs and Prophets, p. 726.*

**b. Kodi maganizo enieni a Atate wathu wakumwamba ndi otani kwa onse amene ataya njira? Ezekieli 18:32; Luka 15:18—20.**

______________________________________________________________

______________________________________________________________

"Satana ndi wokonzeka kuba zitsimikizo zodalitsika za Mulungu. Iye akufuna kutenga kuwala kulikonse kwa chiyembekezo ndi mlezo uliwonse wa kuwala kuchokera ku moyo; koma inu musamulole kuchita ichi. Musamatchera khutu kwa woyesayo, koma muzinena kuti; 'Yesu anafa kuti ine ndikhale ndi moyo. Amandikonda, ndipo safuna kuti ndiononongeke. . . . Fanizo likukuuzani momwe wosochera adzalandiridwire: ( Luka 15:18—20 )

"Koma ngakhale fanizo ili, lachifundo ndi lokhudza mtima momwe liririmu, silinafikire kufotokoza mokwana chifundo chosatha cha Atate wakumwamba. Yehova ananena kudzera mwa mneneri wake kuti: 'Ndakukonda iwe ndi chikondi chosatha: chifukwa chake ndakukoka iwe ndi kukukomera mtima.' Yeremiya 31:3. Pamene wochimwa akali kutali ndi nyumba ya Atate, kuononga chuma chake mu dziko lachilendo, mtima wa Atate ukulakalaka pa iye; Ndipo Kulakalaka kulikonse komwe kungadzutsidwe m'mitima mwawo kukubwerera kwa Mulungu, ndi kuchonderera kofatsa kwa Mzimu Wake, kumukopa, kumupempha, kukokera wosokera ku mtima wa Atate wake wachikondi."— *Steps to Christ, pp. 53, 54*.

## MAFUNSO OBWEREZA PAWEKHA — Lachisanu n'chimozi, Ogasti 7

1. Kodi ndichiyani chimalowa m'moyo womwe machimo ake akhululukidwa?
2. N'chifukwa chiyani wakufa ziwalo wa ku Betesida anakwanitsa kuyenda mwadzidzidzi?
3. Tikalandira Khristu kukhala Mpulumutsi wathu, kodi ndilonjezo lanji limene lili lathu?
4. Kodi chinsinsi cha kuyenda mopambana ndi Khristu n'chiyani?
5. Longosolani kusiyana pakati pa njiru ya Satana ndi chikondi chowombola cha Atate.

LASABATA, Ogasti 15, 2026

Phunziro 7

# Yeso la Kukhala Ophunzira

**Vesi Loloweza**: Chifukwa chake ngati munthu aliyense ali mwa Khristu ali wolengedwa watsopano; zinthu zakale zapita, taonani, zakhala zatsopano. 2 Akorinto 5:17

**Zowerenga Zoonjezera:** *Steps to Christ 7, pp. 57—65*

"Khalidwe limaululidwa, osati ndi zochita zabwino nthawi zina kapena zochita zoipa nthawi zinanso, koma ndi zizolowezi zopitilira za mayankhulidwe ndi machitachita."—Steps to Christ, pp. 57, 58.

## 1. NTCHITO YA MZIMU — Loyamba, Ogasti 9

**a. Kodi ndi phunziro lanji lomwe Khristu anaphunzitsa pakufotokoza ntchito ya Kutembenuka mtima? Yohane 3:5—8.**

---

"Munthu sangathe kunena nthawi yeniyeni kapena malo , kapena kulondoloza zochitika zolumikizana mu dongosolo la kutembenuka mtima ; koma izi sizionetsera kuti iye ndiosatembenuka….Monga Mphepo , imene sioneka , komabe zosatira zimaonekera komanso kumvedwa , ndi m'mene Ulili Mzimu wa Mulungu mu ntchito yake pa mtima wa munthu. Mphamvu imeneyi yakulenganso yomwe palibe diso la munthu lingathe kuona, imabereka moyo watsopano; imalenga munthu watsopano mu chifanizo cha Mulungu." – *Steps to Christ, p. 57.*

**b. Kodi ndikusintha kotani komwe kudzaonekera mu moyo otembenuka moona? Aroma 12:9—18; 2 Akorinto 5:17.**

---

"Pamene sitingachite chilichonse chosintha mitima yathu kapena kudzibweretsa tokha muchiyanjano ndi Mulungu; Pamene sitikuyenera kuzidalira ife eni kapena ntchito zathu zabwino, miyoyo yathu idzaonetsera ngati chisomo cha Mulungu chikukhala mwa ife. Kusintha kudzaonekera mu khalidwe, zizolowezi ndi zofuna zathu. Kusiyana kudzaonekera mooneka bwino komanso motsimikizika chimene anali ndi chomwe ali…

"Ndizoona kuti payenera kukhala khalidwe la kunja labwino pamaso pa anthu popanda mphamvu yatsopano ya Khristu. Chikondi cha chikoka ndi khumbo lofuna kukweza ena zingapangitse moyo wokhazikika m'makhalidwe abwino. Kuzipatsa ulemu kwathu kungatitsogolere ku kupewa maonekedwe oipa. Mtima wodzikonda sungachite zinthu zachifundo. Ndi mwanjira yanji, tsono, yomwe tingadziwire mbali yomwe ife tili?

"ndi ndani ali ndi mtima? Ndi ndani amene malingaliro athu ali naye?" — *Ibid., pp. 57, 58.*

**a. Kodi ndi chipatso chanji chomwe chimabadwa mwa iwo odzazidwa ndi Mzimu Woyera? Agalatiya 5:22, 23.**

“Iwo amene amakhala cholengedwa chatsopano mwa Khristu Yesu amabala zipatso za Mzimu. . . Zinthu zimene ankadana nazo kale tsopano amazikonda, ndipo zimene ankakonda kale tsopano amadana nazo. Odzikuza ndi odzikweza amakhala ofatsa ndi otsika mu mtima. Achabe ndi amwano amakhala aulemu ndi osadzionetsera. Oledzera amakhala odziletsa, ndipo owononga amakhala oyera mtima. Miyambo yachabe ndi mafashoni a dziko lapansi amayikidwa pambali. Akhristu sadzafunafuna ‘kukongoletsa kwa kunja,’ koma ‘munthu wobisika wa mtima, mu chovala chosaola, cha mzimu wofatsa ndi wachete.’ 1 Petro 3:3, 4.”—*Steps to Christ, pp.* 58, 59.

“Chikoka cha Mzimu Woyera ndi moyo wa Khristu mwa munthu . Sitimuwona Khristu kapena kulankhula naye, koma Mzimu wake woyera ali pafupi ndi ife pamalo alionse. Amagwira ntchito mwa aliyense amene amalandira Khristu. Onse amene amadziwa kupezeka kwa Mzimu amaonetsera zipatso za Mzimu—chikondi, chimwemwe, mtendere, kuleza mtima, kufatsa, kuchita zabwino, chikhulupiriro.”—*SDA Bible Commentary* [E. G. White Comments], vol. 6, p. 1112.

**b. Kodi ndi Umboni wanji wa kulapa kwenikwenii? Ezekieli 33:14, 15.**

“Palibe umboni wa kulapa kwenikweni pokhapokha ngati kulapako kwabweretsa kukozanso kwa moyo. Ngati munthu abwezera chowinda, abweza zomwe anaba, avomereza machimo ake, ndi kukonda Mulungu ndi anzake, wochimwa akhoza kukhala wotsimikiza kuti wadutsa kuchokera ku imfa kupita ku moyo.

“Pamene ife, monga anthu ochimwa ndi ophophonya, timabwera kwa Khristu ndi kutenga nawo mbali m’chisomo chake chachikhululukiro, chikondi chimatumphuka mu m’mtima. Katundu aliyense amakhala wopepuka, chifukwa goli limene Khristu amapereka ndi lopepuka. Udindo umakhala chisangalalo, ndipo kudzipereka nsembe kumakhala chimwemwe. Njira imene kale inkaoneka ngati yakutidwa ndi mdima, imakhala yowala ndi kuwunika kwa Dzuwa la Chilungamo.

“Ukoma wa khalidwe la Khristu udzawoneka mwa otsatira ake. Chinali chisangalalo chake kuchita chifuniro cha Mulungu. Chikondi kwa Mulungu, ndi changu cha ulemerero wake, zinali mphamvu yoyendetsera moyo wa Mpulumutsi wathu. Chikondi chinakongoletsa ndi kukweza zochita zake zonse. Chikondi ndi cha Mulungu. Mtima wosakonzetseredwa sungayambitse kapena kubala chikondi. Chimapezeka mu mtima okha umene Yesu amaulamulira. ‘Tikonda ife, chifukwa anayamba Iye kutikonda.’ 1 Yohane 4:19. Mu mtima umenene wakonzedwanso ndi chisomo cha Mulungu, chikondi chimakhala mfundo yoyendetsera machitachita. Chimasintha khalidwe, chimayendetsa zilakolako, chimalamulira malingaliro, chimagonjetsa maudani, ndi kukweza zikhumbitso. Chikondi chimenechi, chikakhala m’moyo, chimakometsa moyo ndi kufalitsa chikoka chosinthira kwa onse ozungulira.”— *Steps to Christ, p. 59.*

**a. Kodi ndi Zolakwikwa ziti zowopsa zimene ambiri amene amadzitcha Akhristu amazivomereza? Afilipi 3:9; Aroma 10:3; Yakobo 2:17.**

"Pali zolakwa ziwiri zimene ana a Mulungu—makamaka amene angobwera kumene kuyamba kudalira chisomo chake—ayenera kusamala nazo kwambiri.

Choyamba, chimene tafotokoza kale, ndi kuyang'anira ku ntchito zawo, kapena kudalira zomwe angachite, Kuzibweretsa okha muchiyanjano ndi Mulungu. Iye amene akuyesera kukhala woyera mtima mwa ntchito zake zokha posunga lamulo, akuyesera zosatheka. Zonse zimene munthu angachite popanda Khristu zimakhala zodetsedwa ndipo kuzikonda ndi tchimo. Ndi chisomo cha Khristu chokha, kudzera mwa chikhulupiriro, chimene chingatipangitse ife kukhala oyera mtima.

"Cholakwika china, chomwe ndichowopsa mofanana, ndi kulingalira kuti chikhulupiriro cha mwa Khristu chimamasula munthu ku kusunga lamulo la Mulungu; kuti popeza mwa chikhulupiriro chokha timakhala nawo otenga mabli m'chisomo cha Khristu, zochita zathu zilibe ntchito pa chipulumutso chathu."—*Steps to Christ, pp. 59, 60.*

**b. Kodi lonjezo la pangano latsopano limasonyeza bwanji kuti chisomo cha Khristu sichimatimasula ku kumvera lamulo la Mulungu? Aheberi 8:10; 10:16.**

"Lamulo la Mulungu ndi chisonyezo cha khalidwe lake lenileni; ndi chithunzi cha mfundo yayikulu ya chikondi, ndipo ndiwo maziko a ulamuliro wake kumwamba ndi padziko lapansi. Ngati mitima yathu yasinthidwa muchifanizo cha Mulungu, ngati chikondi chaumulungu chadzalidwa m'moyo, kodi lamulo la Mulungu silidzachitika m'moyo? Pamene mfundo ya chikondi yadzalidwa mu mtima, pamene munthu wasinthidwa kuti akhale ngati chithunzi cha amene anamupanga, lonjezo la pangano latsopano limakwaniritsidwa [Ahebri 10:16]. Ndipo ngati lamulo lalembedwa mu mtima, kodi silidzatsogolera moyo? Kukhala omvera—utumiki ndi kudzipereka kwa chikondi—ndizo chizindikiro chenicheni cha kukhala ophunzira."— *Ibid., p. 60*

"Mulungu amafuna panopa chimodzimodzi ndi chimene anafunira kwa oyera awiri mu Edeni, kumvera kwangwiro ku zofuna zake. Lamulo lake limakhala chimodzimodzi mu mibado yonse. Muyezo wa chilungamo waukulu umene unaperekedwa mu Chipangano Chakale sunatsitsidwe mu Chatsopano. Si ntchito ya Uthenga Wabwino kufooketsa zofuna za lamulo loyera la Mulungu, koma kubweretsa anthu pamene angathe kusunga malamulo ake.

Chikhulupiriro mwa Khristu chimene chimapulumutsa moyo sichili monga chimene ambiri amachifotokoza. 'Khulupirirani, khulupirirani,' ndi kulira kwawo; 'khulupirirani mwa Khristu yekha, ndipo mudzapulumutsidwa. Ndi zimene muyenera kuchita.' Pamene chikhulupiriro chenicheni chimadalira Khristu mokwanira pa chipulumutso, chidzatsogolera ku kumvera kwathunthu lamulo la Mulungu."—*SDA Bible Commentary* [E. G. White Comments], *vol. 6, p. 1073.*

**a. Kodi ndichiyani chomwe chikuyembekezereka kwa anthu amene akufuna moyo wosatha? 1 Yohane 5:2, 3; 1 Akorinto 7:19.**

“Ngati mudzipereka kwa [Khristu], ndi kumuvomereza kuti ndi Mpulumutsi wanu, ngakhale moyo wanu ukhale wodzazidwa ndi machimo, chifukwa cha Iye mudzawerengedwa ngati olungama. Khalidwe la Khristu lidzayimirira m'malo mwa khalidwe lanu, ndipo mudzavomerezedwa pamaso pa Mulungu ngati kuti simunachimwepo.

Kuposera apo, Khristu amasinthanso mtima. Amakhala mu mtima mwanu mwa chikhulupiriro. Muyenera kusunga m’gwirizano uwu ndi Khristu mwa chikhulupiriro ndi kupereka mosalekeza chifuniro chanu kwa Iye; ndipo pamene mukuchita izi, Iye adzagwira ntchito mwa inu kuti mukhale ndi chikhumbo ndi kuchita mogwirizana ndi chifuniro chake. Chifukwa chake munganene kuti, ‘Koma moyo umene ndiri nao tsopano m’thupi, ndiri nao m’chikhulupiriro cha Mwana wa Mulungu, amene anandikonda, nadzipereka yekha chifukwa cha ine.’ Agalatiya 2:20. Ndipo Yesu ananena kwa ophunzira ake, ‘Pakuti wolankhula si ndinu, koma Mzimu wa Atate wanu akulankhula mwa inu.’ Mateyo 10:20. Ndipo ndi Khristu Wogwira ntchito mwa inu, mudzawonetsa mzimu womwewo ndi kuchita ntchito zabwino zomwezo ntchito za chilungamo, kumvera.

“Choncho tilibe kanthu mwa ife tokha komwe tingadzitamandire nako. Tilibe maziko a kudzikwenza. Maziko athu okhawo a chiyembekezo ali mu chilungamo cha Khristu chimene chimaperekedwa kwa ife, ndi mwa icho chimene chimapangidwa ndi Mzimu wake kugwira ntchito mwa ife ndi kudzera mwa ife.”—*Steps to Christ, pp. 62, 63.*

**b. Ngakhale Ambuye wapanga njira kuti aliyense apeze chipulumutso, n’chifukwa chiyani ena amalephera kupeza njira imeneyo? Aefeso 2:8, 9; Machitidwe 4:12; Aroma 9:30–33.**

“M’malo moti chimasule munthu ku kumvera, ndi chikhulupiriro chokha chimene chimatipatsa gawo mu chisomo cha Khristu, chimene chimatipatsa mphamvu kuti tikhale omvera…

“Chikhulupiriro chotchedwa cha mwa Khristu chomwe chimavomereza kumasulidwa kwa anthu ku udindo wokhala omvera kwa Mulungu, sichikhulupiriro, koma kudzikuza. ‘Pakuti muli opulumutsidwa ndi chisomo chakuchita mwa chikhulupiriro.’ Koma ‘chikhulupiriro, ngati chili chopanda ntchito, ndi chakufa.’ Aefeso 2:8; Yakobo 2:17. Yesu ananena za Iye mwini asanabwere padziko lapansi kuti, ‘Kuchita chikondwero chanu kundikonda, Mulungu wanga; Ndipo malamulo anu ali m’kati mwa mtima mwanga.’ Masalimo 40:8. Ndipo asanakwere kumwamba analengezanso kuti, ‘Ndasunga malamulo a Atate wanga, ndipo ndikhala m’chikondi chake.’ Yohane 15:10. Malemba amanena kuti, ‘Ndipo umo tizindikira kuti tamzindikira iye, ngati tisunga malamulo ake. . . . Iye wakunena kuti akhala mwa Iye, ayeneranso mwini wake kuyenda monga anayenda Iyeyo.’ 1 Yohane 2:3–6. ‘Chifukwa Khristu anavutika chifukwa cha ife, kutisiyira chitsanzo, kuti muyenera kutsatira mapazi ake.’ 1 Petro 2:21.”—Ibid., pp. 60–62.

## 5. KUKHALA MWA CHIKHULUPIRIRO — Lachisanu, Ogasti 13

**a. Kodi mtumwi Paulo ankakhala bwanji moyo wachipambano? 1 Akorinto 15:30, 31.**

"Muyenera kusunga kulumikizana uku ndi Khristu mwa chikhulupiriro ndi kupereka mosalekeza chifuniro chanu kwa Iye; ndipo pamene mukuchita izi, Iye adzagwira ntchito mwa inu kuti mukhale ndi chikhumbo ndi kuchita mogwirizana ndi chifuniro chake."— *Steps to Christ, pp. 62, 63.*

"Khristu, m'thupi lake la umunthu, anapanga khalidwe labwino kwathunthu, ndipo khalidwe limenelo akufuna kutipatsa ife. 'Zolungama zathu zonse ziri ngati chovala chodetsedwa.' Yesaya 64:6. Chilichonse chimene tingachite tokha chimakhala chodetsedwa ndi tchimo. Koma Mwana wa Mulungu 'anawonekera kuti achotse machimo athu; ndipo mwa Iye mulibe tchimo.' … Khristu anali womvera ku zofuna zonse za lamulo. Iye ananena za Iye mwini, 'Kuchita chikondwero chanu kundikonda, Mulungu wanga; Ndipo malamulo anu ali m'kati mwamtima mwanga.' Masalimo 40:8. … Mwa kumvera kwangwiro Iye wapanga kuti zikhale zotheka kwa aliyense kumvera malamulo a Mulungu. Pamene tidzipereka tokha kwa Khristu, mtima umayanjanitsidwa ndi mtima wake, chifuniro chimaphatikana ndi chifuniro chake, maganizo amakhala pamodzi ndi maganizo ake, malingaliro amakhala osungidwa mwa Iye; timakhala m'moyo wake. Ichi ndi chimene chimatanthauza kuvala zovala za chilungamo chake."—*Christ's Object Lessons, pp. 311, 312.*

**b. Kodi ndi chimwemwe chotani chomwe wolemba masalimo anachionetsera m'moyo wake? Masalimo 119:97.**

"Pamene tikulankhula za chikhulupiriro, pali kusiyana komwe tiyenera kukukumbukira. Pali mtundu wa chikhulupiriro chomwe chili chosiyana kwathunthu ndi chikhulupiriro chenicheni. Kukhalapo ndi mphamvu ya Mulungu, choonadi cha mawu ake, ndi mfundo zoona zimene ngakhale Satana ndi makamu ake sangathe kuzikana pa mtima. Baibulo limanena kuti 'ziwanda zimakhulupiriranso, ndipo zimanthunthumira,' koma ichi sichikhulupiriro. Yakobo 2:19. Pamene palibe kungokhulupirira mawu a Mulungu, koma kupereka chifuniro kwa Iye; pamene mtima waperekedwa kwa Iye, pamene chikondi chakhazikitsidwa pa Iye, pamenepo pali chikhulupiriro—chikhulupiriro chimene chimagwira ntchito mwa chikondi ndi kuyeretsa moyo. Mwa chikhulupiriro chimenechi mtima umasinthidwa kukhala chithunzi cha Mulungu."— *Steps to Christ, p. 63.*

## MAFUNSO OBWEREZA PAWEKHA — Lachisanu n'chimozi, Ogasti 14

1. Fotokozani umboni wa kutembenuka mtima.
2. Kodi kusiyana pakati pa munthu wakale ndi munthu watsopano ndi kotani?
3. Fotokozani zoopsa ziwiri zimene tiyenera kupewa m'moyo wathu wauzimu.
4. Pamene tikukhala m'chisomo, kumvera kumaikidwa malo anji?
5. Ndi malingaliro, zilakolako komanso zolinga zotani zimene zimakondedwa pamene Khristu akukhala mu mtima?

LASABATA, OGASTI 22, 2026

Phunziro 8

# Kukula mwa Khristu

**Vesi Loloweza:** "Ndikakonzere iwo amene alira maliro m'zioni, ndi kuwapatsa chobvala kokometsa mmalo mwa phulutsa, mafuta akukondwa mmalo mwa maliro, chobvala cha matamando m'malo mwa mzimu wopsinjika; kuti iwo achedwe mitengo ya chilungamo yakuiwoka Yehova, kuti iye alemekezedwe." (Yesaya 61:3)

**Zowerenga Zoonjezera:** *Steps to Christ,* pp.67—75.

"Ndinu odalira pa Khristu, kuti muyende moyo wangwiro, monga nthambi ku phatha lake mukukula ndi kubereka zipatso'—*Steps to Christ,* p. 69.

## 1. GWELO LA KUKULA — Loyamba, Ogasti 16

**a. Ndimotani momwe malemba anafotokozera zokhuza kukula muchikhristu? Yesaya 61:3;1 Peter 2:2; Aefeso 4:14,15; Marko 4:26,27.**

___
___
___
___

"Palibe mzeru ndi luntha la munthu zomwe zingathe kutulutsa moyo mu zinthu zochepa za chilengedwe. Ndi kudzera m'moyo wokhawo umene Mulungu mwiniyekha amaupereka kuti zonse, kaya zomera kapena nyama, zikhale ndi moyo. Choncho ndikudzeranso m'moyo wochokera kwa Mulungu womwewo m'mene moyo wauzimu umabadwira m'mitima ya anthu."—*Steps to Christ,* p .67

**b. Ndichiyani chomwe chimaonetsera kudalira kwathu pa Khristu mukukula ndi kukhwima? Hoseya 14:5—7; 1 Akolinto 3:6,7.**

___
___
___
___

"Kudzera mu Mphatso yake yapamwamba ya Mwana wake Mulungu anakuta dziko lonse ndi mpweya wake wa chisomo chenicheni monga momwe mpweya ukutira dziko lonse lapansi. Onse amene amasankha kupuma mpweya wa moyowu adzakhala ndi moyo ndi kukula kufikira mu msinkhu wa abambo ndi amayi a mwa Yesu Khristu .

Monga maluwa amatembenukira kudzuwa, kuti milezo ya kuwala ithandizire mukuonetsa bwino kukongola ndi maonekedwe ake, momwemonso ife tiyenera kutembenukira kudzuwa la chilungamo, kuti kuwala kwa kumwamba, kutiwalire, kuti khalidwe lathu lidzikula mofanana ndi Khristu.'—Ibid., p. 68.

**a. Ndi mfundo zanji zofunikira zimene Mbuye wathu anatambasulira kwa ophunzira ake iye asanamalidze utumiki wake wa dziko lapansi? Yohane 15:4—7.**

---

"Ambiri amaganiza kuti akhodza kuchita mbali ya ntchito zina pa iwo okha. Iwo anadalira mwa Khristu kuti machimo awo akhululukidwe, koma tsopano ndi mphamvu zawo zokha akuyetsera kuti akhale angwiro. Koma kuyesera kulikonse kwa mtundu uwu kumalephera. Yesu anati, popanda ine, simungathe kuchita kanthu. Kukula kwathu mu chisomo, chisangalaro chathu, kupindula kwathu zonse zimadalira pakulumikizana kwathu ndi Khristu. Pokhala mwa Iye tsiku ndi tsiku, ola ndi ola, timakula mwa chisomo. Iye sioyamba yekha, komanso wotsiriza wachikhulupiliro chathu. Ndi Khristu amene ali woyamba, wotsiliza ndi wa nthawi zonse. Iye ayenera kukhala ndi ife, sipokhapokha poyamba pokha ndi mapeto antchito yathu ayi, komanso mu khwelero lililonse la njira."—*Steps to Christ,* p.69.

"Ngati muli ofuna kuphunzira kufatsa ndi kuzichepetsa mtima mu sukulu ya Khristu, Iye moona azakupatsani mpumulo ndi mtendere. Ndi chobvuta kwambiri kusiya chifuniro chanu chomwe ndi njira zanu. Koma mukaphunzira kutero mudzapeza mpumulo ndi mtendere. Kunyada, undekha ndi zikhumbitso zanu zikuyenera kugonjesedwa; zifuniro zanu zikuyenera kumezedwa mu chifuniro cha Khristu. Choncho moyo wonse udzakhala monga nsembe yozipereka ya chikondi chosatsithika. Machitidwe ndi mawu anu zonse zidzaonetsera chikondi. Monga moyo wa mpetsa umafalikira kudutsira mu nthambi zikulizikulu kenako kufika pansi pa nthambi zing'onozing'ono, mpakana m'masamba akusonga, momwemonso chisomo ndi chikondi cha Khristu chimayaka ndi kukhazikika m'moyo, chimatumiza mphanvu zake kukafalikira ku mbali zonse za thupi lonse, ndi kulamulira machitachita a thupi ndi malingaliro."—*The SDA Bible Commentary* [E.G. White comments] vol.5,pp.1091.1092.

**b. Kodi chinsinsi chakukula mwa Khristu ndichiyani? Akolose 2:6; Ahebri 10:38.**

---

"Munazipereka nokha kwa Mulungu kuti mukhale wake modzadza, kumtumikira ndi kumumvera Iye, ndipo munatenga Khristu monga mpulumutsi wanu. Simungathe kuchita chozitetezera machimo anu mwa inu nokha kapena kusintha mtima wanu, koma pakuzipereka nokha kwa Mulungu, mumaonetsa chikhulupiliro kuti Iye mwa Khristu Yesu anachita zonse izi chifukwa cha inu. Mwachikhulupiliro mumakhala aKhristu, ndipo mwa chikhulupiliro mumakula mwa Iye. Kudzera mukupereka ndi kulandira muyenera kupereka zonse, mtima wanu, chifuniro chanu, utumiki wanu, kuzipereka nokha kwa Iye mukumvera zofuna zake zonse; ndipo muyenera kuzitengera zonse, Khristu, wodzala ndi m'dalitso wonse, kukhala mumtima mwanu, kukhala mphamvu yanu, chilungamo chanu, nthandizi wanu wamuyaya kuti akupatseni inu mphamvu zakumvera."—*Steps to Christ,* pp, 69,70

**a. Kodi ndi udindo wanji woyambilira wa ana a Mulungu pamene akuyamba tsiku lirilonse? Masalimo 5:3.**

"Dziperekeni nokha kwa Mulungu mamawa, chipangeni ichi kukhala ntchito yanu yoyambilira. Lolani kuti pemphero lanu likhale lotele, "Ambuye nditengeni ine monga m'mene ndiliri ndikuika mzeru zanga zonse pamapazi anu. Ndigwiritseni ntchito muutumiki wanu mukhale mwa ine, ndipo lolani ntchito zanga zilembedwe mwa inu. Ichi chikhale chochitika cha tsiku ndi tsiku. Mamawa ulionse ziperekeni nokha kwa Mulungu pa tsiku limenelo pelekani dongosolo lanu kwa Iye kuti zikatengedwe kapena kupelekedwa monga momwe chipambano chake chingalozere. Ndi mwa tsiku ndi tsiku momwe mungapelekere moyo wanu m'manja a Mulungu, ndipo moyo wanu uzaumbidwa mochulukira pa moyo wa Khristu."—*Steps to Christ,* p. 70.

**b. Ndi kuitanira kwanji kumene Khristu akukulitsa tsiku ndi tsiku? Mateyu 11:28, 29.**

"Kukhala moyo wanu mwa Khristu ndiko kukhala moyo wosapuma. Sipakuyenera kukhala kuzimva kokwanilisidwa, koma pakuyenera kulumikizana, chidaliro cha mtendere. Chiyembekezo chanu sichiri pa inu nokha; chili mwa Khristu. Zofooka zanu zimalumikizana ku mphanvu zake, kupanda chiziwitso kwanu kumalumikizana ndi mzeru zake, kulephera kwanu kulumikizana ndi kupilira kwake kwapamwamba. Tsopano simukuyenera kuziyang'anira pa inu nokha, musalore malingaliro anu akhazikike pa undeka, koma yang'anani pa khristu, lolani malingaliro anu akhazikike pa chikondi chake, pakukongola kwa ungwiro, za khalidwe lake. Khristu mukuzikaniza kwake, Khristu mukuzichepetsa kwake, Khristu muungwiro ndi kupatulika kwake, Khristu muchikondi chake chapamwamba, izi ndizo mfundo za maphunziro oti azilingalilidwa m'moyo. Ndi kudzera mukumukonda Iye, kuphunzira kwa Iye, kudalira modzaza pa Iye, kuti mumasandulika kukhala ofanana naye."—Ibid.,pp.70, 71.

**c. Kodi phata lenileni lokhalira ndi mtendere wammalingaliro ndi chiyani? Yesaya 26:3, 4; 30:15.**

"Onse angamutenge Khristu pa mawu ake, ndi kupereka miyoyo yawo kuti aisunge, kupereka miyoyo yawo kudongosolo lake, adzapedza mtendere ndi bata. Palibe chakudziko lapansi chingawapangitse iwo kukhala achisoni pamene Khristu mukupezeka kwa akuwapanga iwo kukhala amsangala. Mukubvomereza zochitika mumakhala mpumulo wa ngwiro… Miyoyo yathu itha kumaoneka yosowa chiyembekezo; koma pamene tizipereka tokha kwa wamkulu, kwa ogwira ntchito wamzeru, Iye azabweletsa njira ya moyo ndi khalidwe zimene zidzakhale za kuulemelero wake.

"Kumwamba kumayambira pamene kudzera mwa Yesu timalowa mpumulo wake. Timayankha kukuitanira kwake, Idzani, phunzirani kwa ine, ndipo mukubwela kumeneku timayamba moyo wamuyaya."—*The Desire of Ages,* p. 331.

**a. Kodi zotsatira ndizanji pamene tiloza malingaliro athu kukhazika pa Yesu mmalo momaziyang’ana tokha? 2 Akolinto 3:18.**

“Pamene tiyang’ana mosalekeza pa Yesu ndi diso lachikhulupiriro, tidzalimbikitsidwa. Mulungu adzapanga bvumbulutso lapamwamba kwa onse akumva njala ndi ludzu la Iye. Iwo adzapedza kuti Khristu ndi Mpulumutsi wa munthu aliyense payekha. Pamene iwo akudya pa mawu ake, adzapedza kuti ndi moyo ndi mzimu. Mawu amaononga khalidwe lachibadwa, khalidwe lakudziko, ndi kukhazikitsa moyo watsopano mwa Yesu Khristu, mzimu woyera umabwera m’moyo monga mtonthonzi. Kudzera mu mphanvu zotsinthira za chisomo chake, chithunzithunzi cha Mulungu chimaonekera mwa ophunzira, Iye amakhala cholengedwa chatsopano. Chikondi chimatenga malo achiwawa, ndipo mtima umalandira chifanizo cha Umulungu.”—*The Desire of Ages,* p. 391.

“Pamene malingaliro akhazikika pa undekha, iwo amachosedwa kwa Khristu, yemwe ndi gwelo la mphanvu ndi moyo. Ndi cholinga cha satana kuti chidwi chichoke kwa Mpulumutsi ndi kutipewetsa kulumikizana ndi kupereka moyo kwa Khristu. Zosangalatsa za mdziko, chisamaliro cha moyo ndi zovuta ndi zisoni, zolakwa za ena kapena zolakwa za iwe mwini ndi zophophonya, izi zonse iye adzafuna kutembenuzira malingaliro awo. Simukuyenera kulumikizana ndi zotengela zake. Ambiri amene ali ndi chikumbumtima chabwino ndinso amene ali ndi khumbo lokhala okondweretsa Mulungu Iyenso adzawatsogolera kukukhazikika mu zolakwitsa zawo ndi zofooka, ndi munjira imeneyi kuwalekanitsa iwo kwa Khristu amene amayembekezera kupeza chiyembekezo . Sitikuyenera kupanga undekha kukhala gwelo lathu ndi kukhazikika munkhawa ndi mantha za momwe tidzapulumutsidwire. Zonse izi zimachosa miyoyo kuchoka ku gwelo la mphamvu zathu. Perekani ndi kusunga miyoyo yanu kwa Mulungu ndi kudalira kwa iye. Lankhulani ndi kulingalira za Yesu. Lolani undekha uchotsedwe mwa Iye.”— *Steps to Christ,* pp. 71, 72.

**b. Ndi chiyani tingaphunzireko kuchokera mukusintha komwe kunabwela pa akuphunzira atatha iwo kukhala pamodzi ndi Khristu muutumiki wake wa tsiku ndi tsiku? Machitidwe 4;13.**

“Mukupenyerera pa (Yesu) timasandulika kukhala muchifanizo chake kuchoka kuulemerero kupita kuulemerero monga mwa mzimu wa Ambuye.’ 2 Akolinto 3:18.

“Ndimomwemonso mene ophunzira oyambilira anapezera kufanana ndi mpulumutsi wawo wokondedwa. Pamene ophunzirawo amanva mawu a Yesu, iwo amaona kusowekera kwawo kwa Iye. Iwo amaganiza, iwo apeza, iwo amamutsatira iye. Iwo anali ndi iye mnyumba, pa gome, mukuyandikana, m'maminda, iwo anali ndi iye monga ophunzira ndi mphuzitsi tsiku ndi tsiku kulandira kuchokera pa milomo yake chiphuzitso cha choonadi chopatulika. Iwo amamuyang’ana Iye monga akapolo kwa mbuye wawo, kuphunzira udindo wawo, ophunzira amenewo anali amuna onga zotengela zofooka monga tilili ife. Yakobo 5:17. Iwo anali ndi nkhondo yofanana yolimbana ndi tchimo. Iwo amasowekela chisomo chofanana kuti ayende moyo wangwiro.”— Ibid., pp.72,73.

## 5. LONJEZO KWA IFE — Lachisanu, Ogasti 20

**a. Ndi lonjezo lanji limene Yesu analisiya kwa omutsatira ake mukukumana ndi zovuta za udani wa mdzikoli? Mateyu 28:20**

_______________________________________________

_______________________________________________

“Pamene khristu amakwera kumwamba, chikumbumtima cha kupezeka kwake chinali pakati pawo pamodzi ndi otsatira ake. Kunali kupezeka kwa payekha, kodzaza ndi chikondi ndi kuunika. Yesu, mpulumutsi anayenda ndi kulankhula ndi kupemphera ndi iwo. Iye amene analankhula za chiyembekezo ndi chitonthozo m’mitima yawo, pamene uthenga wa mtendere unakali pa milomo yake, anachotsedwa pakati pawo kupita kumwamba, ndi kumveka kwa mawu ake kunabwelelanso pakati pawo pomwe khamu la Angelo limamulandira Iye, ndikuti “Ine ndili pamodzi ndi inu kufikira kumapeto nthwi ya dziko lapansi;” mateyu28:20.”—*Steps to Christ,* pp. 73.74.

**b. Ndi malangizo anji ofunikira amene Yesu anawasiira ophunzira ake chotelo kuti akazindikire choyenera kuchita munthawi ya kusowa? Yohane16:23,24; 14:16—18.**

_______________________________________________

“Pamene anasonkhana pamodzi khristu atakwela kumwamba iwo anali othekera kukupereka zosowa zawo kwa atate mudzina la Yesu…Iwo anakweza manja awo achikhulupiliro pamwamba ndi pambamba ndi wotsutsa wamkulu, Aroma8:34. Tsiku la pentecositi linawabweletsa iwo mukupezeka kwa mtonthonzi amene khristu analankhula za iye, “Iye adzakhala ndi inu;” ndipo Iye analankhulanso kuti, “Indetu, indetu, ndinena kwa inu, Wokhulupilira ine, ntchito zimene ndicita adzachita zoposa izi; chifukwa ndipita ine kwa Atate. Yohane 14:12; 6:7. Ndi kudzera mwa mzimu woyera, momwe Khristu akuyenera mopitilira kukhala m’mitima ya ana ake. Kulumikizana kwake kumakhala chifupi kwambiri kuposera m’mene anali ndi iwo mwakuthupi; kuunika, ndichikondi ndi mphanvu zokhalira mwa Khristu zinaonetsedwa kudzera mwa iwo, chotelo kuti anthu, mukuyang’ana modabwitsika; anatenga chiziwitso kwa iwo kuti iwo anakhalapo ndi Yesu.’ Machitidwe4:15.’—Ibid.,pp. 74, 75.

## MAFUNSO OBWEREZA PAWEKHA — Lachisanu n’chimodzi, Ogasti 21

1. Pamene tikukula monga ngati zomela, chifukwa chiyani tikusowekera thandizo lochokera kumwamba?
2. Monga zomera zimasowekera mibvumbi ndicholinga chokula muuzimu?
3. Ndichiyani chimapangitsa kuzipereka kwa tsiku ndi tsiku kukhala kofunikira kwa ife aliyense payekha payekha?
4. Chifukwa chiyani Mulungu ali ndi khumbo kwa ife mukuchotsa undekha pa Yesu nthawi zonse.
5. Ndi lonjezo lanji limene lingakhale mu zenizeni tsiku ndi tsiku mmoyo wa Okhulupilira aliyense?

LASABATA, OGASTI 29, 2026

Phunziro 9

# Ntchito komanso Moyo

**Vesi Loloweza**: 'Koma onse amene anamulandira Iye, kwa iwo anapatsa mphamvu yakukhala ana a Mulungu, kwa iwotu, akukhulupilira dzina lake;'(Yohane 1:12)

**Zowerenga Zoonjezera:** *Steps to Christ,* pp. 77—83

"Mzimu wa Khristu wachikondi wozipereka msembe ndi mzimu womwe umalamulira kumwamba ndi fungo lokoma mukufukiza kwake. Uwu ndi mzimu umene otsatira ake akhristu akuyenera kuonetsera, ntchito imene ayenera kuichita."—*Steps to Christ,* p.77.

## 1. MOYO KOMANSO KUUNIKA — Loyamba, Ogasti, 23

**a. Ndichiyani chimene chinanyozeleledwa ndi mtima wachibadwa— ndipo izi zinali ndi zotsatira zanji? Yohane1:4,5.**

__________________________________________________________

__________________________________________________________

"Mulungu ndi gwero la moyo ndi kuunika ndi chisangalaro kudziko lonse lapansi monga milezo ya kuunika yochokera ku dzuwa, monga akasupe amadzi otuluka kuchokera ku misinje yamoyo, madalitso amatuluka kuchokera kwa Iye kupita kuzolengedwa zake zonse. Ndipo kulikonse komwe moyo wa Mulungu ukhala m'mitima ya anthu, udzayenda kupita kwa ena mu chikondi ndi mdalitso."— *Steps to Christ,* p. 77.

**b. Pamene chikondi cha Khristu chili mumtima, Ndichiyani chidzaonekere m'moyo? 2 Akolinto2:14,15; 5:14.**

__________________________________________________________

__________________________________________________________

__________________________________________________________

"Pamene chikondi cha Khristu chikuonetseredwa mumtima, monga ngati zonunkhira zokoma sichingabisidwe. Chikoka chake chopatulika chidzakhala pa onse amene tikulumikizana nawo. Mzimu wa Khristu mumtima monga ngati msinje muchipululu, umayenda kutsitsimutsa onse ndi kukopa iwo amene ali okonzekera kuchiononongeko, kukhala ndi khumbo lokumwa ku madzi a moyo."—Ibid.

"Lolani dziko lione kuti ife sitinamizidwe muchidwi cha ife eni, koma kuti tikukhumba ena kugawana nawo mdalitso wathu ndinso mwayi wathu. Aloleni iwo kuona kuti chipembezo chathu sichimatipanga ife kukhala opanda chifundo kapena ozikweza.Tilole onse amene amazitcha kuti a Khristu, atumikire monga Iye mwini amachitira kuubwino wa anthu."—*The Desire of Ages,* p. 152.

**a. Pamene tamulandira Yesu monga mpulumutsi wathu, ndi chosowa chanji chomwe chimaperekedwa? Yohane 1:12,13; 1 Akolinto 1:4,5; Aroma 5:1,2.**

---

"Iwo amene ali ogawana nawo chisomo cha khristu azakhala okonzeka kupereka nsembe iliyonse, kuti ena omwe Iye anawafera akagawane nawo mphatso za kumwamba. Iwo azachita zonse zomwe angakwanitse kulipanga dziko kukhala lokoma kukhalamo. Mzimu umenewu ndiweniweni wotuluka ku moyo wotembenuka moona. Munthu akangobwera kwa Khristu, nthawi yomweyo mtima wake umayamba kukhala ndi chilakolako chofuna kudziwitsa ena za Bwenzi lamtengo wapatali limene wapeza mwa Yesu; choonadi chopulumutsa ndi chopatulitsa sichingabisike m'mtima mwake. Pamene tabvekedwa ndi chilungamo cha Khristu ndi kuzazidwa ndi chimwemwe cha mzimu wake wokhala mwa Iye, sitingakwanitse kuusunga mtendere wathu. Pamene talawa ndikuona kuti Ambuye ndi wabwino tidzakhala ndi chinachake cholankhula. Monga Filipo pamene anapedza mpulumutsi, tidzaitanira ena mukupezeka kwake."— *Steps to Christ,* p. 78

**b. Pamene tikukumana ndi mabvuto ndi zovuta, ndi uphungu wanji womwe tikupeza kwa mtumwi Paulo? Ahebri 4:16**

---

"Yesu amaziwa zosowa za ana ake, ndipo Iye amakonda kumvetsera kupemphero lawo. Tilore ana kuchoka kudziko lapansi ndi zilizonse zimene zingachotse malingaliro kuchoka kwa Mulungu, ndipo tiwalore iwo kuti amve kuti iwo ali okha pamodzi ndi Mulungu kuti maso ake amaona mkati mwa mtima, ndi kuwelenga zokhumba za moyo, ndikuti angathe kulankhula ndi Mulungu,"—*Sons and Daughters of God,* p. 121.

**c. Pamene takhala mwana wa Mulungu, ndi chiyani tingangongole kwa ena? Aroma1:14,15.**

---

"Ndi mwanjira yanji imene Paulo anakhalira wangongole pakati pa onse Ayuda ndi amitundu? Kwa iye kunapelekedwa ntchito, monga imene imaperekedwa kwa ophunzira aliyense wa Khristu, pitani kudziko lonse, ndikuphuzitsa ku dziko lonse ndikuwabatiza iwo mudzina la atate ndi mwana ndi mzimu woyera ; ndikuwaphunzitsa iwo kuti asunge zinthu zonse zimene ndinakulamulirani inu, ndipo onani Ine ndili pamodzi ndi inu nthawi zonse, kufikira kumapeto a dziko lonse lapansi; Mukumulandira Khristu, Paulo anabvomeleza utumiki umenewu. Iye anazindikira kuti pa iye panagonera mwayi wogwirira ntchito anthu amitundu yonse kwa ayuda ndi Amitundu, ophunzira ndi osaphunzira, kwa iwo okhala m'maudindo apamwamba ndi iwo otsikitsitsa pomwe anali moyo.'"—*The SDA Bible Commentary* (E.G. White Comments),Vol6,p.1067.

**a. Ngati mzimu woyera uli mumtima mwathu, kodi ndi chiyani chidzakhale choyambilira m'machitachita athu? Yohane 1:41, 42.**

---

"Tiyenera kufuna kupeleka kwa ena chikoka cha Khristu ndi zenizeni zake zosaonekazo za dziko likudzalo. Padzakhala chidwi chokhumba kutsatira mu njira imene Yesu anayenda. Payenera kukhala khumbo loona kuti iwo otizungulira ife 'awone mwana wankhosa wa Mulungu, amene achotsa chimo lake la dziko lapansi.'Yohane1:29.

"Pakuyetsetsa kudalitsa ena mdalitso udzatsatiranso pa ife eni. Ichi ndi cholinga cha Mulungu mukutipatsa mbali yochita mudongosolo la chiombolo. Iye anapeleka kwa anthu mwayi mukutenga nawo mbali mukhalidwe la umulungu ndipo ku mbali yawo, kuti apeleke mdalitso kwa anthu anzawo. Uwu ndiwo ulemu waukulu koposa, ndicho chimwemwe chachikulu koposa, chimene Mulungu angathe kupereka kwa anthu. Iwo amene angatenge nawo mbali mukugwira ntchito ya chikondi amabweletsedwa chifupi ndi Mlengi wawo.

"Mulungu akhoza kupereka mauthenga a choonadi, komanso ntchito yonse ya utumiki wa chikondi kwa angelo akumwamba. Iye akhoza kugwiritsa ntchito njira zina mukumalizitsa cholinga chake. Koma muchikondi chake chosaneneka Iye amasankha kutipanga ife ogwira nawo ntchito pamodzi ndi Iye mwini, mwa Khristu ndi angelo, kuti tikhoza kukagawana madalitso, chimwemwe, kukwedza uzimu, zimene zidzatsatira kutuluka muutumiki wopanda undekha.

Tinabweletsedwa muchiyanjano pamodzi ndi Khristu kudzera mukugawana naye mazunzo ake. Machitidwe onse ozipereka nsembe kuubwino wa ena umalimbikitsa mzimu wopambanitsa m'mitima yopereka, kuisendezera chifupi kwambiri kwa mombolo wadziko lapansi, Iye amene anali wolemera chifukwa cha ife… anakhala wosauka, kotero kuti kudzera mu uphawi wake tikakhale olemera.' 2 akolinto 8:9. Ndipo ndikuzera pamene tikwanilitsa cholinga cha Umulungu mukulengedwa kwathu kuti moyo ukhale mdalitso kwa ife."—*Steps to Christ,* pp. 78—80.

**b. Ndi chisanzo chanji cha Khristu chimene chingatitsogolere ife muubale wathu ndi abale athu ndi otizungulira athu? Agalatiya 6:9,10; Yohane 9:4.**

---

"Ngati mungapite ku ntchito monga khristu anapangira kuti ophunzira ake azikhala, ndikupindula miyoyo kwa Iye, mudzazimva kusowekera kwanu kwa zodutsamo zanu zokuya ndinso chiziwitso chachikulu mu zinthu za Umulungu, ndipo mudzamva njala ndi ludzu la chilungamo. Mudzachonderera Ambuye ,ndipo chikhulupiliro chanu chidzalimbikitsidwa , ndipo moyo wanu uzamwa modzama pa chisime chachipulumutso. Zotsutsa ndi Mayetsero osawelengeka adzakutsogolera iwe ku Buku lopatulika ndi pemphero. Inu mudzakula mwachisomo ndi chiziwitso cha Khristu, ndipo muzakudza zodutsamo zapamwamba."—Ibid., p.80.

**a. Tchulani choopsa chachikulu kwa ife monga mamembala ampingo lero. Malaki 3:8—8.**

“Munthawi yathu ino (Osunga sabata oyembekezera kubwela kwa Khristu) choopsa chawo chachikulu ndicho kuchuluka kwa katundu wawo. Ambiri akupitilira kuchulukitsa zotsamalira zawo ndi ntchito zawo; iwo ali ndi zochuluka. Zotsatira zake , Mulungu ndi zosowekela zake ku ntchito yake zili chifupi kuiwalidwa ndi iwo; iwo afa kuuzimu. Akusowekera kupereka nsembe kwa Mulungu mu zopereka. Nsembe sizikumachuluka, koma malomwale zikutsika ndi kuonongedwa…mochuluka pakati pa anthu athu. Izi mangoonetsera kuonongeka kwa iwo amene akuimilira mu ichi.”—*Testimonies for the church,* vol. 1, p. 492.

**b. Ndi thandizo lanji la akhristu lomwe lingathandize okhulupilira kukula muchisomo ndi mchiziwitso cha Ambuye wathu Yesu Khristu?1 Peter 4:8—10; Ahebri 13:2.**

“Mwayi womwe unaperekedwa kwa Abrahamu ndi Loti sunatimanenso ife. Mukuonetsa kulandila alendo kwa ana a Mulungu, ifenso tidzalandira angelo m'nyumba zathu. Ingakhale masiku athu ano, Angelo mumaonekedwe aumunthu amalowa m’nyumba za anthu ndikusamaliridwa ndi iwo. Ndipo Akhristu amene amakhala mu kuwala kwa nkhope ya Mulungu amatsagana nthawi zonse ndi angelo osawoneka, ndipo Angelo oyera mtima amenewa amasiya mdalitso m’nyumba zathu. ”—Ibid., vol.6,p.342.

**c. Ndi chosowa chanji chimene chingakwanilitsidwe ndi okhulupilira lero? 2 Akolinto 10:16.**

“Mamembala a mipingo yathu akhoza kukwanilitsa ntchito imene, tsopano lino, movuta iwo angoyiyamba. Palibe amene angapite kudela latsopano ndicholinga chongozisangalatsa mu dziko lapansi; koma pamene pali potsegula kupeza zosamalira zamoyo uno, tilole mabanja amene ali odzika midzu mchikhulupiliro alowe, banja limodzi kapena awiri apite kudera , kukagwira ntchito monga atumiki. Ayenera kukhala ndi chikondi pa miyoyo, ndi kunyamula udindo wogwira ntchito chifukwa cha iwo, ndipo ayenera kuphunzira njira zowabweretsera iwo m’choonadi. Iwo atha kugawa zowelenga zathu, kupanga mikumano mnyumba zawo, kukhala olumikizana ndi anzawo owazungulira, ndikuwaitanira iwo kufika ku mkumanowu . Umu ndi momwe iwo angaonetsere kuunika kwawo kuti kuwalire mu ntchito zabwino.”—Ibid., vol.8. p.245.

“Kwa nthawi yaitali Mulungu wakhala akudikira mzimu wautumiki kulamulira mu mpingo wonse ndicholinga choti wina aliyense atha kumugwilira ntchito Iye molingana ndi kuthekera kwake. Pamene mamembala amumpingo wa Mulungu akuchita ntchito yawo yosankhidwira mumadera awo osowa, m'nyumba ndi mutalimutali, pokwanilitsa utumiki wa uthenga wabwino, posachedwapa dziko lonse la pansi lidzachenjezedwa ndipo Ambuye Yesu adzafika kudziko lino ndi mphanvu ndi ulemerero.”—The Acts of the Apostles, p. 111.

## 5. NTHUMWI ZOKHULUPIRIKA — Lachisanu, Ogasti 27

**a. Ndichiyani chimene tikuyembekezera kwa onse amene apatsidwa uthenga wabwino makamaka kwa ogwira ntchito ya Ambuye? 1.Akolinto 4:1,2; Chibvumbulutso 2:10.**

---

"Ndi mwayi wa alonda pamakoma a Zioni kukhala chifupi ndi Mulungu, ndikukhala obvomelezeka mukulandira mzimu wake, ndicholinga choti atha kukagwira ntchito kudzera mwa iwo kuwauza ochimwa za chionongeko chawo, ndikuwalodzera iwo ku malo otetezeka. Osankhidwa a Mulungu, osindikizidwa ndi mwadzi wozipereka, ayenera kulanditsa amuna ndi amayi ku chionogeko chikudza. Mokhulupilika iwo ayenera kuchenjeza anthu amzawo za zotsatira zenizeni zakuphwanya kwa lamulo, ndipo mokhulupirika iwo ayenera kuyang'anira chidwi cha Mpingo."—*Gospel Workers,* p. 15.

**b. Ndi chitsanzo chanji chimene Daniel anaika pa achinyamata alero? Daniel 1:8, 15.**

---

"Ambuye akufuna ife tiphunzirenso phunziro kuchokera mu zodutsamo za Daniel. Pali ambiri amene angakhale amuna amphanvu monga ngati ahebri okhulupilikawa iwo akuyenera kudalira pa Mulungu ku chisomo kukhala ogonjetsa, ndi mu mphanvu ndi kuyesetsa kwawo mu ntchito zawo. Danieli anaonetsera khalidwe labwino la ungwiro, kwa onse kuyambira atsogoleri ndinso pa achinyamata. Iye anaima monga wochitira umboni Mulungu,ndipo anafuna kutenga ntchitoyi kuti asachitise manyazi kumwamba mukumva mawu ake kapena mukuyang'ana ntchito yake. Pamene Danieli amafunikira mukutenga gawo lozikondweretsa la pagome la a Mfumu, iye sanathamangire mu mudyo wake, ingakhale kuzionetsera chidwi choti atha kudya ndi kumwa monga angazikondwerestere. Opanda kuyankhulapo mawu oipa, iye anaitengela nkhaniyi kwa Mulungu. Iye ndi azanke anafuna mzeru kuchokera kwa Mulungu, ndipo pamene anabwela kuchokera kumapemphero okhulupilika mfundo zawo zinachitika. Ndi chidaliro chawo choona ndi chikhristu chawo cha ulemu, Danieli anapereka mlandu kwa olamulira amene anali owalamulira, kuwapempha kuti akuyenera awapatse chokudya chophweka. Achinyamatawa anaganiza kuti mfundo zawo zachipembezo zili pangozi, ndipo iwo anadalira pa Mulungu , amene amamukonda ndi kumtumikira."—*Testimonies to Ministers,* p. 263.

## Mafunso Obwereza Pawekha — Lachisanu n'chimodzi, Ogasti 28

1. Ndimukhalidwe lanji la dziko limene lingapangitse kukhala chofunika kwa Mulungu kubweletsa kuunika kwake ku ilo?
2. Ndikusintha kwanji kodabwitsa kumene kudzaonekere mumoyo wa okhulupilira?
3. Pamene madalitso alandilidwa, kodi kuyankha kwake kudzakhala kwanji?
4. Tchulani njira zina zimene wina aliyense wa ife tingathandizire ena.
5. Ndimotani momwe kukhulupirika kwa Danieli kungandilimbikitsire ine?

# Zopereka za Sabata Loyamba

**Lasabata, September 5, 2026**



## Sukulu ya Maphunziro a Utumiki wa Baibulo ku Philippines

Pamene tikukumbutsidwa za ntchito yaikulu yopita ku dziko lonse lapansi ndikukapanga ophunzira, tikuyenera kuchitapo kanthu. Sukulu ya Maphunziro a Utumiki wa Baibulo ndi malo apadera osulira ndi kukonzetsera antchito ku munda wa Mphesa wa Ambuye. Kuyambira pomwe inayambitsidwa mu February 1984, sukuluyi yakhala nyali ya chikhulupiriro, kukonzetsera mitima ndi malingaliro a iwo amene ali ndi chikhumbo chokalalikira uthenga wabwino kwa mitundu yonse. Ophunzira ambiri amene amaliza pulogalamu ya zaka ziwiri ya maphunziro a utumiki yomwe malowa amapereka ena a iwo tsopano ndi atumiki ofalitsa uthenga wabwino kunja kwa dzikolo, ndipo ena ambiri ndi atsogoleri komanso azibusa omwe akufalitsa uthenga wa chipulumutso m'madera okhala anthu ambiri ku zilumba za ku Philippines.

Pokhala mu Cabatang, Tiaong, ku chigawo cha Quezon mdziko la Philippines, Sukulu ya Maphunziro a Utumiki wa Baibuloyi yakhala ikugwira ntchito mosalekeza kupereka maziko olimba a Baibulo kwa omwe akufuna kukhala atumiki a uthenga wabwino ku Philippines komanso m’dera lonse la Pacific. Malowa apereka kuthekera kuti ophunzira adzitha kukhalako, kuphunzira Chingerezi, komanso kuphunzitsidwa kukhala atumiki a uthenga wabwino, ogulitsa mabuku, ogwira ntchito zaumoyo, ndi oyang’anira omwenso akufunikira kwambiri mdzikolo komanso kunja kwake. Malowanso agwiritsidwapo ntchito ngati kochitira maseminale, misonkhano ya achinyamata, komanso makonferensi.

Pamene ntchito ya kukonzanso yakula ku Philippines, kukulitsa ndi kukonzanso malowa kwakhala kofunikira kwambiri tsopano kuti apitirize kuthandiza moyenera ntchito ya Mulungu kupita chitsogolo. Poyang’anira zosowa zimenezi, madongosolo akuchitikanso kuti msonkhano wa General Conference udzachitikirenso pamalo pomwepa. Ndi dalitso lalikulu bwanji kudzakhala ndi msonkhano wa okhulupirira kumeneko, komwenso masomphenya a mautumiki olalikira ndi kutsitsimuka mu uzimu zidzakhala patsogolo!

Zopereka zanu za Sabata Loyamba lero zithandiza kwambiri pomangira kukulitsa komwe kwakhala kofunikira kwambiri pa malowa. Pamene tikupereka, tiyeni tikumbukire mawu a 2 Akorinto 9:7, “Yense achite monga anatsimikiza mtima, si mwachisoni kapena mokakamiza, pakuti Mulungu akonda wopereka mokondwerera.”

Zopereka zanu zithandize kukweza sukuluyi, kulimbikitsa cholinga chake, ndi kubweretsa antchito okonzeka kulalikira uthenga wabwino wosatha. Tiyeni tipereke mwa chikhulupiriro ndi chimwemwe, podziwa kuti zopereka zathu zibalila zipatso zosatha za ufumu wa Mulungu.

Zikomo, ndipo Ambuye akudalitseni koposa pamene mukupereka!

*Abale ndi Alongo anu ku Philipine*

LASABATA, SEPTEMBER 5, 2026

Phunziro 10

# Kudziwa Mulungu

**Vesi Loloweza:** "Wokhala nazo nzeru asamalire izi, ndipo azindikire zachifundo za Yehova" Masalmo 107:43.

**Zowerenga Zoonjezera:** *Steps to Christ,* pp.85–91.

"Chidziwitso chonse chowona ndi kukula kwenikweni zonse zimachokera mu kudziwa Mulungu."—*Education,* p. 14.

## 1. MULUNGU AMADZIWULULA YEKHA

**Loyamba, Ogasti 30**

a. **Kodi ndikudzera mu zinthu ziti za m'dziko lino m'mene Yehova akuitanira anthu kuti abwere kwa Iye? Masalmo 19:1–6; Miyambo 2:1–5.**

"Pali njira zambiri zomwe Mulungu akufuna kuti adzibvumbulutsire yekhz kwa ife ndi kutibweretsa mu chiyanjano ndi Iye. Chilengedwe chimalankhula ndi malingaliro athu mosalekeza. Mtima wotseguka udzakhutitsidwa ndi chikondi ndi ulemerero wa Mulungu monga zabvumbulutsidwa kudzera mu ntchito za manja ake. Khutu lomvetsera limatha kumva ndikumvetsetsa zolankhula za Mulungu kudzera mu zinthu zachilengedwe. Minda yobiriŵira, mitengo italiitali, mphukira ndi maluwa, mtambo wodutsa, mvula yokugwa, kasupe wotumphuka, ulemelero wakumwamba, zimalankhula ndi mitima yathu, ndi kutiitanira ife kuti timudziŵe Iye amene anazipanga zonsezo."—Steps to Christ, p. 85.

b. **Kodi Yesu anagwiritsa ntchito chiyani kukhazikitsa choonadi m'malingaliro a omvera ake? Mateyu 13:3, 34.**

"Mpulumutsi wathu anamanga maphunziro ake a mtengo wapatali ndi zinthu za chilengedwe. Mitengo, mbalame, maluwa a m'zigwa, zitunda, nyanja, ndi miyamba yokongola, limodzinso ndi zochitika ndi malo ozungulira moyo wa tsiku ndi tsiku, zonsezo zinagwirizanitsidwa ndi mawu a chowonadi, kuti motero maphunziro Ake akakumbukiridwe kaŵirikaŵiri m'maganizo, ngakhale pakati pa zotangwanitsa za moyo wa munthu wotopetsa.

"Mulungu akufuna kuti ana Ake ayamikire ntchito Zake ndi kusangalala ndi kukongola kophweka, kwachete kumene Iye wakometsera nako dziko lathu lapansi lino."—Ibid

**a. Ndi phunziro lanji limene lingaphunziridwe kuchokera mu chilengedwe—mwachitsanzo maluwa, mbalame, ndi nyenyezi? Aroma 1:20; Machitidwe 14:17.**

---

““M’kafukufuku wa sayansi . . . tiyenera kupeza chidziŵitso cha Mlengi. Sayansi yowona yonse imangotanthauza kumasulira kwa manja a Mulungu m’zinthu zakuthupi. Sayansi imabweretsa umboni watsopano chabe wa nzeru ndi mphamvu za Mulungu kuchokera mu kafukufuku wake. Moyenerera, buku la chilengedwe ndi mawu olembedwa zimatithandiza kudziŵa Mulungu mwa kutiphunzitsa kanthu kena ka malamulo anzeru ndi opindulitsa amene Iye amagwiritsira ntchito.”—*Patriarchs and Prophets,* p. 599.

“Ngati titakhala anthu omvetsera, ntchito zolengedwa za Mulungu zidzatiphunzitsa maphunziro amtengo wapatali a kumvera ndi kukhulupirira. Kuchokera ku nyenyezi zimene zimayenda m’njira zawo zosawoneka mlengalenga nthawi ndi nthawi, kufikira ku kachidutswa kochepetsetsa, zinthu za m’chilengedwe zimamvera chifuniro cha Mlengi. Ndipo Mulungu amasamalira chirichonse ndipo amasunga chirichonse chimene Iye adachilenga.”—*Steps to Christ,* pp. 85, 86.

**b. Pamene tikuganizira kukongola ndi mtendere wa chilengedwe chosawonongeka, tiyenera kukumbukira chiyani chokhudza dziko latsopano lolonjezedwa? 1 Akorinto 2:9; Chibvumbulutso 21:1.**

---

“Lolani malingaliro anu ajambule nyumba ya opulumutsidwa, ndipo kumbukirani kuti idzakhala yokongola kuposa momwe mungaganizire. Mu mphatso zosiyanasiyana za Mulungu m’chilengedwe, timangowona kuwala kochepa kokha kwa ulemerero wake.”—*Steps to Christ,* pp. 86, 87.

“Mpingo wa Mulungu wapatsidwa mavumbulutso a cholinga chosatha cha Yehova. Anthu ake aloledwa kupenya mopitirira mayesero a tsopano lino kufikira ku zipambano za mtsogolo, pamene nkhondo ikadzatha, opulumutsidwa adzalowa ndikukhala m’dziko lolonjezedwa. Masomphenya awa a ulemerero wa mtsogolo, zojambulidwa ndi dzanja la Mulungu, ziyenera kukhala zokondedwa ku mpingo wake lero.”—*Prophets and Kings,* p. 722.

“M’Baibulo cholowa cha opulumutsidwa chimatchedwa ‘dziko.’ Ahebri 11:14—16. Kumeneko Mbusa wakumwamba amatsogolera gulu Lake ku akasupe a madzi amoyo. Mtengo wa moyo upatsa zipatso zake mwezi ndi mwezi, ndi masamba a mtengowo ndi ochiritsira amitundu. Pali mitsinje yoyenda nthawi zonse, yonyezimira ngati krustalo, ndipo pambali pake mitengo yoweyula yomwe imayika mithunzi yake panjira zokonzedwera owomboledwa a Yehova. Kumeneko zigwa zotambalala zimasefukira kukhala mapiri okongola, ndipo mapiri a Mulungu amakulitsa nsonga zake zazitali. M’zigwa zamtendere zimenezo, pambali pa mitsinje yamoyo imeneyo, anthu a Mulungu, omwe kwa nthawi yayitari akhala alendo ndi ogonera, adzapeza pokhalapo.”—*The Great Controversy,* p.675.

**a. Ndi maphunziro ati ofunikira kwambiri omwe tingaphunzire kuchokera kwa aneneri kuti atilimbikitse pa nthawi ya kufooka ndi mayesero? Yakobo 5:17; Aroma 8:28; 1 Yohane 5:14.**

"Muzokumana nazo zathu komanso malo otizungulira, m'zosintha zatsiku ndi tsiku zimene zikuchitika mozungulira ife, tingapeze maphunziro amtengo wapatali ngati mitima yathu ili yotseguka kuti tiizindikire. . . . [Makolo akale ndi aneneri] anthu 'omvera zilakolako monga ife.' Yakobo 5:17 . Timaona mmene anavutikira mu zofooketsa monga zathu, m'mene anagwera m'mayesero monga ife tachitira, ndipo komabe analimbikanso mtima ndi kugonjetsa mwa chisomo cha Mulungu; ndipo, poyang'anitsitsa, titonthozedwa m'kulondola kwathu chilungamo." — *Steps to Christ,* pp. 87, 88.

**b. Ngati Mulungu amasamalira zinthu za chilengedwe, kodi sadzasamalira kwambiri ana ake? Masalmo 107:43; 145:15, 16.**

"Chilengedwe ndi mabvumbulutso zonse pamodzi zimachitira umboni za chikondi cha Mulungu. Atate wathu wakumwamba ndiye gwero la moyo, la nzeru, ndi la chimwemwe. Talingalirani za kusintha kwawo kodabwitsa ku zosoŵa ndi chimwemwe, osati cha munthu kokha, komanso cha zamoyo zonse. Dzuwa ndi mvula, zimene zimasangalatsa ndi kutsitsimutsa nthaka ya dziko, zitunda, nyanja, ndi zigwa, zonse zimatiuza za chikondi cha Mlengi." — Ibid., p. 9.

**c. Kodi lonjezo la chisamaliro cha Mulungu liyenera kutitsogolera ku chiyani? Mateyu 6:30–34.**

"Tikamayesa kusamalira tokha zinthu zomwe tikuyenera kuchita, ndi kudalira nzeru zathu zokha kuti tipambane, timakhala tikutenga umene Mulungu sanatipatse, ndipo tikuyesera kuwunyamula popanda thandizo lake. Tikudzitengera udindo womwe uli wa Mulungu, potero tikudziyika tokha m'malo mwa Mulunguyo. Tikhoza kukhala ndi nkhawa ndi kuyembekezera ngozi ndi imfa, chifukwa zidzatigwera ndithu. Koma tikamakhulupiriradi kuti Mulungu amatikonda ndipo amafuna kutichitira zabwino tidzasiya kudera nkhawa za m'tsogolo. Tidzakhulupirira Mulungu monga mmene mwana amadalirira kholo lake lachikondi. Ndiye mavuto athu ndi zowawa zidzatha, chifukwa chifuniro chathu chidzamezedwa ndi chifuniro cha Mulungu."— *Thoughts from the Mount of Blessing,* pp. 100, 101.

**a. Ndikuti komwe Khristu anayika mabvumbulutso omveka bwino a dongosolo la Mulungu la chipulumutso cha anthu? Yohane 5:39; Yesaya 34:16.**

---

"Mulungu amalankhula nafe m'Mawu ake. Mmenemu tiri ndi mabvumbulutso omveka bwino a khalidwe lake, mmene amachitira ndi anthu, komanso ntchito yayikulu ya chiwombolo."—*Steps to Christ,* p. 87.

**b. Ndi chiyani chomwe chiyenera kumachitidwa tsiku ndi tsiku ndi aliyense yemwe akukhumba kukula mukulimbika ndi mphamvu za Mulungu? Yohane 6:53, 63; Akolose 3:1, 2.**

---

"Mutu wa chiombolo ndi womwe angelo amalakalaka kuyang'anamo; idzakhala sayansi ndi nyimbo ya owomboledwa m'mibadwo yosatha ya muyaya. Kodi sikoyenera kuti zilingaliridwe ndi kuphunziridwa mosamalitsa tsopano? Chifundo chosatha ndi chikondi cha Yesu, nsembe yoperekedwa chifukwa cha ife, zimayitanitsaa kusinkhasinkha mozama ndimosamalitsa kwambiri. Tiyenera kukhazikika pa khalidwe la Muomboli wathu wokondedwa ndi Mtetezi. Tiyenera kusinkhasinkha za ntchito ya Iye amene anabwera kudzapulumutsa anthu ake ku machimo awo."—Ibid., pp. 88, 89.

**c. Kodi tingatengere bwanji Mawu a Mulungu m'mitima yathu?? Mateyu 4:4; 2 Timoteyo 2:15.**

---

"Palibe amene ali ndi mzimu woyamikira chiphunzitso chake amene angawerenge ndime imodzi ya m'Baibulo popanda kupezamo mfundo yothandiza. Koma chiphunzitso chamtengo wapatali cha Baibulo sichiyenera kupezedwa mwa apo ndi apo kapena osaphunzira. Dongosolo lake lalikulu la chowonadi silimaperekedwa kotero kuti lizindikiridwe ndi woŵerenga wofulumira kapena wosasamala. Chuma chake chambiri chili pansi kwambiri, ndipo chingapezeke kokha mwa kufufuza mwakhama ndi kuyesetsa kosalekeza. Choonadi chimene chimapanga chinthu chachikulu chiyenera kufufuzidwa ndi kusonkhanitsidwa, 'kuno pang'ono, ndi ukonso pang'ono.' Yesaya 28:10.

"Pamene afufuzidwa motero ndi kusonkhanitsidwa pamodzi, adzapezedwa kukhala oyenererana bwino lomwe. Uthenga uliwonse ndi chowonjezera ku china, uneneri uliwonse ndi kufotokozera kwa wina, chowonadi chirichonse ndi chitukuko cha chowonadi china. Mitundu ya chuma cha Chiyuda imafotokozedwa momveka bwino ndi uthenga wabwino. Mfundo iriyonse m'mawu a Mulungu ili ndi malo ake, mfundo iliyonse imakhala nayo. Ndipo dongosolo lathunthu, m'kapangidwe ndi kachitidwe kake, limapereka umboni kwa Mlembi wake. Mapangidwe oterowo palibe malingaliro a munthu aliyense koma a Wopandamalire yekha amene angathe kukhala nawo kapena kuwamvetsetsa."—*Education,* pp. 123, 124.

## 5. KUPHUNZIRA BAIBULO — Lachisanu, Septemba 3

**a. Ndi chiyani chimene chinabweretsa chitonthozo ndi thandizo kwa Yeremiya pa nthawi yake yovuta? Yeremiya 15:16.**

"Palibe chinthu chomwe chimathandiza kwambiri kulimbitsa nzeru kuposa kuphunzira Malemba Opatulika. Palibe bukhu loposa lomwe liri ndi mphamvu zokweza maganizo, kupatsa mphamvu malingaliro, monga chowonadi chachikulu ndi cholemekezeka cha Baibulo. Zikanakhala kuti Mawu a Mulungu akuphunziridwa monga momwe zinayenera kumakhalira, anthu akanakhala ndi maganizo otambalala, khalidwe lolemekezeka, ndi cholinga chokhazikika zomwe ndizosowa masiku ano."—*Steps to Christ,* p. 90.

"Iye amene amapereka chidwi chachikulu ku Malemba Opatulika, kudzera mupemphero adzakhala ndi kumvetsetsa kwabwino komanso chiweruzo cholimba, monga ngati kuti potembenukira kwa Mulungu wafika pa mlingo wapamwamba wa nzeru."—*Mind, Character, and Personality,* vol. 1, p. 95.

**b. Ndi motani momwe Malemba Opatulika ayenera kuphunziridwira? Nanga ndi chiyani chomwe chiyenera kuyamba kuphunzira Baibuloko kusanachitike? Masalimo 119:9, 11, 16.**

"Choonadi cha Mulungu, monga golide, sichimakhala nthawi zonse powonekera; chikuyenera kupezeka kokha kudzera mu kuganiza mozama ndi kuphunzira."—*Gospel Workers,* p. 76.

"Monga wokumba migodi amapezera mizere ya miyala yamtengo wapatali yobisika pansi pa nthaka, choteronso amene amafufuza Mawu a Mulungu mosalekeza ngati chuma chobisika adzapeza chowonadi chamtengo wapatali kwambiri, chomwe ndichophimbika kwa munthu aliyense wofufuza mosasamala. Mawu owuziridwa, posungidwa ndi kuganiziridwa mumtima, adzakhala ngati mitsinje yotuluka ku kasupe wa moyo.

Baibulo siliyenera kuphunziridwa popanda kupemphera. Tisanatsegule masamba ake tiyenera kupempha chiwalitsiro cha Mzimu Woyera, ndipo tidzapatsidwa. . . . Angelo ochokera kudziko la kuwala adzakhala ndi iwo amene kudzera mukudzichepetsa kwa mtima wawo amafuna chitsogozo cha kumwamba."—*Steps to Christ,* p. 91.

## MAFUNSO OBWEREZA PAWEKHA — Lachisanu n'chimodzi, Septemba 4

1. Ndi njira iti yophunzitsira yomwe Mpulumutsi wathu anagwiritsa ntchito kufikira anthu?
2. Kodi Mulungu wapanga njira iti yodzibvumbulutsira yekha kwa anthu onse—kuphatikizapo onse amene alibe mwayi wowerenga mawu ake?
3. Ndi chiyani chomwe chingaphunziridwe kudzera mu zinthu zomwe Mulungu amapereka?
4. Fotokozani khalidwe lomwe tiyenera kukhala nalo pa Baibulo monga bvumbulutso la Mulungu.
5. Ndi chokumana nacho chotani cha Yeremiya chokhudza Malemba Opatulika chomwe chiyenera kubwerezedwanso?

# Mwayi wa Pemphero

**Vesi Loloweza:** “Koma iwe popemphera, lowa m’chipinda chako, nutseke chitseko chako, nupemphere Atate wako ali m’tseri, ndipo Atate wako wakuona m’tseri adzakubwezera iwe” (Mateyu 6:6).

**Zowerenga Zoonjezera:** *Steps to Christ,* pp.93–104.

“Pemphero ndilo kutsegulira mtima kwa Mulungu monga ngati kwa bwenzi. Osati kuti ndizofunikira kuti timudziwitse Mulungu chimene ife tiri, koma kuti zitithandize kuti timulandire Iye. Pemphero silimamupangitsa Mulungu kuti atsikire kwa ife, koma limatikweza ifeyo kwa Iye.”—*Steps to Christ,* p. 93.

## 1. WOPEMPHA WAMKULU — Loyamba, Septemba 6

a. **Monga Mwana wa munthu, ndi chiyani chomwe Yesu anachipeza kukhala chofunikira? Luka 5:16; Marko 6:46.**

________________________________________

________________________________________

________________________________________

“Onani Mwana wa Mulungu akuwerama m’pemphero kwa Atate Wake! Ngakhale ali Mwana wa Mulungu, amalimbitsa chikhulupiriro chake mwa pemphero, ndipo mwa kulumikizana ndi Kumwamba amatenga mphamvu yolimbana ndi zoipa komanso kutumikira zosowa za anthu. Monga Mbale Wamkulu wa mtundu wathu, Iye amadziwa zosowa za awo amene pozingidwa ndizofooka, komanso pokhala m’dziko la uchimo ndi mayesero, amafunabe kumutumikira. Iye amadziwa kuti atumiki amene amawawona kukhala ndikuthekera kowatumiza kukatumikira ndi anthu ofooka ndi olakwitsa; koma kwa onse amene amadzipereka kwathunthu kuntchito yake, Iye amalonjeza kuwapatsa thandizo lakumwamba. Chitsanzo cha Iye mwini ndi chitsimikizo kuti kupemphera moona mtima, mosalekeza kwa Mulungu mwa chikhulupiriro—chikhulupiriro chimene chimatsogolera kukudalira Mulungu kwathunthu ndi kudzipereka kotheratu kuntchito yake—chidzalimbika kubweretsa kwa anthu thandizo la Mzimu Woyera mu nkhondo yolimbana ndi uchimo.”—Gospel Workers, p. 511.

b. **Ndimotani momwe kachitidwe ka kapemphero ka Khristu kakukhalira chitsanzo kwa ife? Marko 1:35; Luka 6:12.**

________________________________________

________________________________________

________________________________________

“Yesu mwini, pamene anali kukhala pakati pa anthu, nthawi zambiri anali kukonda kupemphera.”—Steps to Christ, p.93.

**a. Kodi Yesu anawaphunzitsa ophunzira ake kuti adzipemphera motani? Luka 11:1–4.**

“Pamene Yesu anali padziko lapansi, anaphunzitsa ophunzira ake mmene angamapempherere. Iye anawatsogolera iwo kuti adzipereka zosowa zawo za tsiku ndi tsiku kwa Mulungu, ndi kutaya pa Iye nkhawa zawo zonse. Ndipo chitsimikizo chimene anawapatsa chakuti mapemphero awo adzamveka, ndi chitsimikizonso ngakhale kwa ife. . . .

Iye ndi m’bale wathu mu zofooka zathu, ‘anayesedwa m’njira zonse monga ifenso;’ koma monga wopanda tchimo, chikhalidwe chake chinakana zoipa; Iye anapirira nkhondo ndi kuvutika kwa mtima m’dziko la uchimo. Umunthu wake unapanga pemphero kukhala chofunikira komanso mwayi. Iye anapeza chitonthozo ndi chisangalalo polankhulana ndi Atate ake. Ndipo ngati Mpulumutsi wa anthu, Mwana wa Mulungu, anaona kufunikira kwa pemphero, koposa kotani ife anthu ofooka ndi ochimwa tikuyenera kuwona kufunikira kwa kupemphera mwakhama ndi mosalekeza?”— *Steps to Christ,* p.93, 94.

**b. Ndimotani momwe Baibulo likufotokozera za kudzipereka kwa Khristu, komanso chifukwa chimene izi zinali zofunikira kwambiri? Yesaya 50:4; Aheberi 2:10; 5:7–9.**

“Pamene umunthu unali pa Iye, anadzimva kusowekera mphamvu kwake kuchokera kwa Atate wake. Anali ndi malo apadera opempherako. Ankakonda kulumikizana ndi Atate wake m’malo chete a kumapiri. Munchitidwe umenewu, moyo wake woyera wa umunthu unalimbikitsidwa kuti athe kugwira ntchito ndi kupirira mayesero omwe angathe kukumana nawo. Mpulumutsi wathu amadziwa zofooka ndi zosowa zathu, chifukwa kuti anakhala wopempha, wopemphera usiku wonse, kufunafuna mphamvu zatsopano kuchokera kwa Atate ake, kuti akatulukire wolimbikitsidwa ndi wokonzeka kugwira ntchito ndi kupirira mayesero. Iye ndi chitsanzo chathu m’zinthu zonse.”— *Testimonies for the Church,* vol. 2, pp. 201, 202.

“Ndinaona kuti palibe ngakhale m’modzi mwa achinyamata makumi awiri amene amadziwa chimene chipembedzo chochitachita chiri. Amadzitumikira okha koma nkumadzitchula atumiki a Khristu; koma ngati tsoka limene liri pa iwo siliwonongedwa, posachedwapa adzazindikira kuti mphotho ya olakwa ndi yawo. Ponena za kudzikana kapena nsembe chifukwa cha choonadi, apeza njira yosavuta yopitirira zonsezi. Mmalo momadandaulira mwakhama ndi misozi ndi kulira mwamphamvu kwa Mulungu kuti apeze chisomo chakukhululukira ndi mphamvu kuchokera kwa Iye yopewera mayesero a Satana, achipeza kukhala chosafunikira kuti akhale owona ndi odzipereka; akuwona kuti akhoza kukhala bwino popanda zimenezi. Khristu, Mfumu ya ulemerero, ankachoka yekha nthawi zambiri kupita kumapiri ndi kumalo a chipululu kukapemphera kwa Atate wake; koma munthu wochimwa, amene mwa iye mulibe mphamvu, amaganiza kuti angakhale moyo popanda pemphero lowirikiza.”— Ibid., vol. 1, p. 504, 505.

**a. Kodi Yesu anasonyeza motani mtima wa Atate wake pa zosowa za anthu? Mateyu 6:6; 7:7–11.**

“Atate wathu wa kumwamba akuyembekezera kutipatsa ife chidzalo cha madalitso ake. Ndi mwayi wathu kumwa mochuruka pa kasupe wa chikondi chopanda malire. N’zodabwitsa motani kuti ife timangopemphera pang’ono! Mulungu ndiwokonzeka komanso wofunitsitsa kumva pemphero loona la ana ake odzichepetsa kwambiri, koma pali kunyalanyaza kwakukuru kowonekeratu kumbali yathu kumuuza Mulungu zosowa zathu. . . .

“Mulungu ndi wanzeru kwambiri kotero kuti salakwitsa, ndipo ndi wabwino kwambiri kotero kuti sangakanize chinthu chabwino kwa iwo oyenda molungama. Potero musaope kumukhulupirira, angakhale musakuwona yankho la pemphero lanu nthawi yomweyo. Khulupirirani lonjezo lake losatsutsika lakuti, ‘Pemphani, ndipo chidzapatsidwa kwa inu.’”—*Steps to Christ,* pp. 94, 96.

**b. Ndi chiyani chimalepheretsa mapemphero athu kumvedwa ndi Ambuye? Masalimo 66:18; Miyambo 28:13.**

“Malingaliro athu akhoza kuwoneka kuti ali kwa Mulungu; tikhoza kumalingalira pa ntchito zake, chifundo chake, ndi madalitso ake; koma zimenezi mukunena moona, sizitanthawuza kulumikizana naye. Pofuna kulankhulana ndi Mulungu, tiyenera kukhala ndi zoti timuwuze zokhudza moyo wathu weniweni.. . .

“Ndichiyani chimene Angelo akumwamba angaganize zokhuza anthu osowa thandizo, amene ali pachiwopsezo choyesedwa, pamene mtima wa Mulungu wa chikondi chopanda malire ukukhumba kuwathandiza, wokonzeka kuwapatsa zambiri kuposa zimene iwo angapemphe kapena kuganiza, chonsecho iwo amangopemphera pang’ono chabe komanso ali ndi chikhulupiriro chochepa kwambiri? Angelo amakonda kugwada pamaso pa Mulungu, iwo amakonda kukhala pafupi naye. Iwo amaona kuti kulumikizana ndi Mulungu ndicho chimwemwe chawo chachikulu; chonsecho ana a padziko lapansi, amene akusowekera kwambiri thandizo limene Mulungu yekha ndiye angapereke, amaoneka okhutitsidwa kuyenda popanda kuwala kwa Mzimu wake, yemwe ndiye bwenzi la kupezekapo kwake.

“Mdima wa woipayo umakuta onse amene amanyalanyaza kupemphera. Mayesero onong’oneza a mdani amawatsogolera iwo ku uchimo; ndipo zonsezi zimachitika chifukwa iwo sakugwiritsa ntchito mwayi womwe Mulungu wawapatsa muchikhazikitso cha kumwamba cha pemphero.. . .

“Ngati timasekelera zoyipa mumitima mwathu, ngati tikukakamilira ku tchimo lirilonse lodziwika, Ambuye sadzatimvera; koma pemphero la munthu wolapadi ndi wosweka mtima limalandiridwa nthawi zonse. Pamene zolakwa zonse zodziwika zakonzedwa, tikhoza kukhulupilira kuti Mulungu adzayankha mapemphero athu. Kuyenedwa kwathu sikungatibvomereze ku chifundo cha Mulungu; ndi kuyenera kwa Yesu kokha komwe kudzatipulumutse, mwazi wake ndiwo udzatitsuke; komabe tiri ndi ntchito yoti tichite pokwaniritsa zinthu zofunika kuti tilandiridwe.”—Ibid., pp.93–95.

**a. Ndi zinthu zofunika ziti za pemphero lopambana poyerekeza ndi pemphero lofooka komanso losagwira ntchito? Ahebri 11:6; Maliko 11:24.**

“Tikapanda kulandira zinthu zomwe tinapempha pa nthawi yomwe tinapemphera, tikuyenera kukhulupilirabe kuti Ambuye wamva ndipo adzayankha mapemphero athu. Ife tiri olakwa ndipo sitimawona patali, kotero kuti nthawi zina timapempha zinthu zomwe sizingatipatse madalitso, ndipo Atate wathu wa kumwamba mwachikondi amayankha mapemphero athu potipatsa zomwe zingatipindulitse kwambiri—zomwe ife tokha tingafune ngati tingawone zinthu zonse momwe ziliri ndi maso owunikiridwa ndi Mulungu. Pamene mapemphero athu akuoneka ngati sakuyankhidwa, tiyenera kukakamira ku lonjezo; chifukwa nthawi yoyankha idzafika ndithu, ndipo tidzalandira dalitso lomwe tikulisowa kwambiri.”—*Steps to Christ,* p. 96.

**b. Pofuna kuti pemphero limvedwe ndi Ambuye, kodi tiyenera kukhala ndi mzimu wotani? Mateyu 6:12; Maliko 11:25, 26.**

“Tikamabwera kupempha chifundo ndi madalitso kwa Mulungu tiyenera kukhala ndi mzimu wachikondi ndi wokhululuka mumtima mwathu. Tingapemphere bwanji kuti, ‘Mutikhululukire mangawa athu, monga ifenso tiakhululukira amangawa athu,’ chonsecho tikukhalabe mu mzimu wosakhululuka? Mateyu 6:12. Ngati tikufuna kuti mapemphero athu amvedwe, tiyenera kukhululukira ena mofanana ndi mmene ifeyo tikufunira titakhululukidwira.”—Ibid., p. 97.

**c. Ndichiyani chomwe tiphunzire kuchokera ku pemphero la Eliya lopemphelera mvula? 1 Mafumu 18:41–45.**

“Mnyamata wa Eliya anali kuyang’anira pamene Eliya anali kupemphera. Kasanu ndi kamodzi anabwerera kuchokera pa kuyang’anira, akunena kuti, Palibe kanthu, palibe mtambo, palibe chizindikiro cha mvula. Koma mneneriyo sanagonje ndi kukhumudwa. Anapitiriza kudzisanthula moyo wake kuti awone ngati panalipo pena pake pomwe analakwira Mulungu, anabvomereza machimo ake, ndipo potero anapitiriza kudzichepetsa pamaso pa Mulungu, uku akuyang’anirabe chizindikiro chakuti pemphero lake liyankhidwe. Pamene ankafufuza mtima wake, ankawoneka kukhala woperewera kwambiri, kwa iye yekha komanso pamaso pa Mulungu. Zinawoneka kwa iye mwini kuti anali chabe, ndipokuti Mulungu ndiye anali zonse; ndipo pamene anafika pa mfundo yodzikana yekha, ndikukakamilira kwa Mpulumutsi monga mphamvu yake yokha ndi chilungamo chake, yankho linabwera.”—*The SDA Bible Commentary,* vol. 2, p. 1035.

## 5. KUPIRIRA MUKUPEMPHERA — Lachisanu, Septemba 10

**a. Kodi atumwi akupereka malangizo otani ofunika okhudza pemphero? 1 Petro 4:7; Afilipi 4:6.**

___

___

___

"Pali kufunikira kwa khama mkupemphera; musalole chirichonse kuti chikusokonezeni. Yesetsani kwambiri kuti kulumikizana pakati pa Yesu ndi moyo wanu zisaleke. Funani mwayi uliwonse wopita kumalo amene mapemphero amachitikira. Iwo amene akufunadi kulumikizana ndi Mulungu amapezeka pa msonkhano wopemphererako, okhulupirika kuchita udindo wawo ndipo ali ndi changu chofuna kulandira madalitso onse amene angawapeze. Amagwiritsa ntchito mwayi uliwonse wodziyika okha pamalo amene angathe kulandira mizere ya kuwala kochokera kumwamba."—*Steps to Christ,* p. 98.

**b. Monga kholo lirilonse, kodi Ambuye amayembekezera kuti ana Ake achita chiyani? Luka 11:10, 13; Yohane 14:13, 14.**

___

___

___

"'M'dzina Langa,' Khristu anauza ophunzira Ake kuti adzipemphera. M'dzina la Khristu omutsatira Akeonse amkuyenera kuyima pamaso pa Mulungu. Kupyolera mu mtengo wake wa nsembe yomwe inaperekedwa chifukwa cha iwo, iwowa ali ofunikira kwambiri pamaso pa Ambuye. Chifukwa cha chilungamo cha Khristu chochokera kwa Iye, iwowa amawerengedwa kukhala anthu amtengo wapatari. Chifukwa cha Khristu, Mulungu amakhululukira iwo amene amamuopa Iye. Samawona kuipa kwa wochimwa mwa iwo. Amaona mwa iwo chifaniziro cha Mwana Wake, amene iwo amakhulupirira."—*The Desire of Ages,* p. 667.

"Palibe nthawi kapena malo amene sipoyenera kupereka pemphero kwa Mulungu. Palibe chomwe chingalepheretse kukweza mitima yathu mu mzimu wa pemphero lowona. Pakati pa khamu la anthu mumsewu, pakati pa kugwira ntchito, tingatumize pemphero kwa Mulungu ndi kupempha chitsogozo cha kumwamba, monga Nehemiya anachitira pamene anapempha pamaso pa Mfumu Artaxerxes. Malo a pemphero angapezeke kulikonse kumene tiri."—*Steps to Christ,* p. 99.

## MAFUNSO OBWEREZA PAWEKHA — Lachisanu n'chimodzi, Septemba 11

1. Ndi chitsanzo chiti cha kupirira m'pemphero chomwe chaperekedwa kwa okhulupirira onse?
2. Ndi ulosi uti womwe ukuwonetsa kufunika kwa pemphero m'mawa uliwonse?
3. Kodi chofunikira choyamba cha pemphero lopambana ndi chiyani?
4. N'chifukwa chiyani tiyenera kupitiriza kupemphera pamene tikadali kudikirirabe yankho?
5. Fotokozani tanthauzo lenileni la kupemphera m'dzina la Yesu.

LASABATA, SEPTEMBA 19, 2026

Phunziro 12

# Mmene Tingathanile ndi Kukaikila

**Vesi Loloweza:** "Koma apemphe ndi chikhulupiliro, wosakakika konse pakuti wokaikayo afanana ndi pfunde la mnyanja lotengeka ndi mphepo ndikuwinduka nayo." (Yakobo 1:6)

**Zowerenga Zoonjezera:** *Steps to Christ,* pp. 105—113

"Mulungu samatipempha ife kuti tikhulupilire, popanda maumboni okwanira amene ife tingakhazikitsepo chikhulupiliro chathu."—*Steps to Christ,* p. 105.

## 1. KODI KUKAYIKA NDI CHIYANI?

**Loyamba, Septemba 13**

**a. Ndichiyani chimene tikuyenera kukumbukira pamene tayesedwa kuti tidzisintasintha pakati pa chikhulupiliro ndi kukaikira? Yakobo 1:5-7.**

___

___

"Lonjezo la Mpulumutsi ndila kwa okhawo amene ali ofuna kutsatira ambuye mwanthunthu, Mulungu sakakamiza chifuniro cha wina aliyense; kotero Iye sangatsogolere iwo amene ali onyada kwambiri kukuphunzira, iwo amene amakhazikika mukutsatira kunjira za iwo eni. Kwa anthu amalingaliro awiri—iye amene amafuna kutsatira chifuniro chake, pamene akuzichula yekha kuti amachita chifuniro cha Mulungu—kwalembedwa, `Munthu ameneyu asaganize kuti azalandira kalikonse kuchokera kwa Mulungu.' Yakobo1:7."—*Patriarchs and Prophets,* p. 384.

**b. Ndichiyani chimene Ambuye wapereka ndi cholinga chogonjetsa kukaikira? Masalimo 119:105; Ahebri 11:1, 3, 6.**

___

"Chikhulupiliro chathu chiyenera kugonera pa maumboni, osati ku zoonetseredwa. Iwo amene akufuna kukaikira azakhala ndi mwayi pamene iwo amene amafuna kudziwa choonadi adzapeza maumboni ochuluka amene iwo angakhazikitsirepo chikhulupiliro chawo."—*Steps to Christ,* p. 105.

"Mulungu wapereka mu mawu ake umboni wokwanira wa khalidwe lake la umulungu. Choonadi chachikulu chimene chimakhuza chipulumutso chathu chinapelekedwa monveka bwino. Kudzera muthandizo la mzimu woyera, limene linalonjezedwa kwa onse amene akulifunafuna ilo mokhulupilika, munthu wina aliyense atha kuchizindikira choonadi ichi mwa iye yekha. Mulungu wapereka kwa anthu maziko olimba pamene angakhazikitsepo chikhulupiliro chawo."—*The Great Controversy,* pp, 526,527

**a. Kodi tingafotokoze motani za zinsinsi zimene Mulungu sanazifotokoze? Dentelonomo 29:29; Yobu 38:4—11.**

---

"Mawu a Mulungu, monga khalidwe la Olemba wa umulungu, amafotokoza zinsinsi zimene sizingamvetsetsedwe mwanthunthu ndi zolengedwa zokhala ndi malire. Kulowa kwa uchimo mudziko, kusandulika kwa Khristu m'thupi la umunthu, kubadwa kwake, kuuka ndi maphunziro ena ambiri operekedwa m'Buku Lopatulika, ndi zinsinsi zokuya zomwe mzeru zaumunthu sizingakwanitse kufotokozera kapena kumvetsetsa modzadza. Koma tilibe chifukwa chokaikira mawu a Mulungu chifukwa sitingathe kumvetsetsa zinsinsi za machitachita Ake."—*Steps to Christ,* p. 106.

"Mulungu samakakamiza anthu kugonjetsa kusakhulupilira kwawo. Pamaso pawo pali kuunika ndi mdima, choonadi ndi bodza. Zili kwa iwo kusankha chimene iwo angachilandire. Malingaliro a munthu anapatsidwa mphanvu zosiyanitsira chabwino ndi choipa. Mulungu anapanga kuti munthu asamapenge chisankho kuchokera mummene thupi lake likumvera, koma kuchokera mu kulemera kwa maumboni, mosamalitsa kufananiza lemba ndi lemba. Pokhala kuti Ayuda anaika pambali tsankho lawo ndi kufananiza ulosi wolembedwa ndi Mfundo zimene zinaonetsera moyo wa Yesu, iwo akanazindikira chiyanjano chokongola pakati pa ulosi ndi kukwanilisidwa kwake mu moyo ndi utumiki wa m'galileya wodzichepetsayu.

"Ambiri akunamizidwa lero munjira yofanana ndi yomwe Ayuda ananamizidwira. Aphuzitsi achipembezo amawelenga Baibulo mukuunika kwa chiziwitso cha iwo eni ndi miyambo, ndipo anthu fufuza malemba mwa iwo eni, ndikuweluza kwa iwo eni kuti choonadi ndi chiyani; komano iwo amagonjera ku chiweruzo cha atsogoleri awo, ndi kusiya miyoyo yawo mmanja mwa azitsogoleri awo. Kulalikira ndi kuphuzitsa kwa mawu Ake ndi njira imodzi yokha imene Mulungu anaidzodza mukufalitsa choonadi Chake; koma tikuyenera kubweletsa chiphuzitso munthu aliyense kumuyeso wa malemba opatulika."— *The Desire of Ages,* pp.458, 459.

**b. Kodi zimazindikirika motani mu Buku Lopatulika kuti pali zinthu zina zovuta kuzimvetsetsa? 2 Petro 3:16.**

---

"Kuvuta kwa Malemba Opatulika kwakhala kukugwiritsidwa ntchito ndi achikunja ngati mfundo yotsutsa Baibulo; koma kutali ndi izi, kumapanga umboni wamphanvu wa kuuziridwa kwake kwa umulungu. Koma ngati malemba samafotokozera za Mulungu koma icho chimene ifeyo tingathe kuchimvetsetsa mosavuta; Ngati ukulu ndi mphanvu Zake zikanamvetsetsedwa ndi malingaliro okala ndi malire, kutere Baibulo likana lopanda umboni wachindunji wa ulamuliro wa Umulungu. Maphunziro a ulemerero ndi chinsinsi ofotokozedwa mmalemba akuyenera kuutsa chikhulupiriro mwa iwo monga mawu a Mulungu."—*Steps to Christ,* p. 107,

**a. Kodi choopsa choziwika bwino kwa okhulupirira mumasiku ano otsiliza ndi chiyani? Ahebri 3:12; 2 Timoteo 4:3, 4.**

---

---

"Pamene Mulungu akutumiza kwa anthu machenjezo ofunikira kwambiri kotelo kuti uthengawu ukuonetsedwa ngati ukulalikidwa ndi Angelo opatulika owuluka pakatikati pa mlengalenga, Iye akufuna munthu aliyense wodzazidwa ndi mphanvu zakulingalira awulandire uthengawu. Chiweluzo choopsa chonenedwa motsutsana ndi kupembeza chilombo ndi fano lake (Chibvumbulutso 14:9—11), chidzatsogolera onse ku kuphunzira mwa mwakhama ulosi kuti aphunzire kuti chizindikiro cha chilombo ndi chiyani, nanga ndimotani tingapewere kuchilandira ichi. Koma magulu aanthu akupewetsa makutu awo kuchoka kukumvetsera choonadi ndipo akutembenukira ku nthano za chabe. Mtumwi Paulo anafotokoza, mukuyang'ana mmatsiku omalidza: "Nthawi idzafika imene sadzalora chiphuzitso cholamitsa." 2 Timoteo 4:3. Nthawi imeneyo yafika tsopano modzaza. Khamu laanthu silikufuna choonadi cha m'Baibulo, chifukwa chimatsutsana ndi mtima wa uchimo, wokonda dziko lapansi; ndipo Satana akupereka chinyengo chimene iwo achikonda."—*The Great Controversy,* pp. 594, 595.

**b. Ndichiyani chinaloseledwa zamakhalidwe la magulu awiri mumasiku otsiliza? Danieli 12:10; Chibvumbulutso 22:11.**

---

---

---

"Mulungu adzakhala ndi anthu padziko lapansi ochirikiza Baibulo, ndi Baibulo lokha basi, kukhala monga muyeso wa ziphuzitso zonse ndi maziko akukozanso konse. Maganizo a anthu ophunzira, Mfundo za sayansi, chikhulupiriro kapena mfundo za mabungwe a mpingo, zochuluka ndi zogawanika monga mipingo imene ziimira, mawu a gulu—osati mmodzi kapena onse aizi ziyesedwe monga umboni wa kapena wotsutsana ndi mfundo iliyonse ya chikhulupiriro cha chipembezo. Tisanavomereze chiphunzitso kapena lamulo lililonse, tiyenera kufunsa kuti kodi 'Atero Ambuye' pochirikiza chiphunzitsocho."—Ibid.,p 595.

"Kuunika kwatsopano kudzabvumbulutsidwabe mu mawu a Mulungu kwa iye amene akukhala mukulumikizana ndi dzuwa lachilungamo. Pasapezeke wina aliyense kufika kumapeto kuti palibe choonadi china chimene chingabvumbulutsidwe. Akhama, ofunafuna choonadi mwapemphero adzapeza miledzo yapamwamba yakuunika kuti ikawalabe kuchokera mmawu a Mulungu. Khamu la miyala ya mtengo wapatali siinamwazidwebe imene ikuyenera kusonkhanitsidwa pamodzi kuti ikakhale chuma cha otsala a anthu a Mulungu. Komano kuwala sikuperekedwa kuti kukhale mphamvu ya mpingo chabe, koma kuti kukawalire kwa iwo amene ali mumdima."—*Counsels on Sabbath shool work,* p. 34

**a. Kodi tingasiyanitse bwanji pakati pa chofunikira ndi chosafunikira? 2 Akolinto 13:5; Tito 3:9—11.**

---

"Pamene Mulungu wapeleka umboni okwanira wa chikhulupiliro, Iye sadzachotsa zozikanira zonse zopangitsa munthu kuti asakhulupilire. Onse oyang'ana kuli mbedza kuti akakolekeko kukaikira kwawo adzaipedza. Ndipo onse okana kulandira ndi kumvera mawu a Mulungu kufikira chikaiko chonse chitachotsedwa, ndipo palibenso mwayi ulionse wa kukaikira, iwo sazafika ku kuunika."—*The Great Controvesy,* p. 527.

**b. Kodi ndi mdalitso wanji udzafike pa odzichepetsa? Yakobo 4:6,10; 1 Petro 5:6, 7.**

" 'Zosowa zonse zinaperekedwa, njala ya moyo wanga inakwaniritsidwa; ndipo tsopano Baibulo kwa ine ndi chibvumbulutso cha Yesu khristu. Kodi mukufunsa kuti mchifukwa chiyani ndimakhulupirira Yesu? Chifukwa choti Iye ali kwa ine mpulumutsi wa umulungu. Chifukwa chiyani ndimakhulupilira Baibulo? Chifukwa ndalipedza kuti ndi mawu a Mulungu ku moyo wanga.' Titha kukhala ndi mboni mwa ife eni kuti Baibulo ndi loona, kuti Khristu ndi mwana wa Mulungu. Tikudziwa kuti sitikutsatira malingaliro opanda pake."—*Steps to Christ,* p. 112.

**c. Ndimotani mtumwi Paulo akufotokozera zodutsamo za moyo za okhulupilira tsopano ndinso mtsogolo? 1 Akolinto 13:12.**

"Mmoyo uno tingayambe kuzindikira chabe mutu wodabwitsa wa chiombolo. Ndi kuzindikira kwathu kochepaku tiyenera kulingalira moona manyazi ndi ulemerero, moyo ndi imfa, chilungamo ndi chifundo, zimene zinakumana mu mtanda; komabe mukutambasula kwambiri kwa mphamvu zathu za malingaliro sitingakwanitsebe kumvetsetsa kufunikira kwake modzadza. Kutalika ndi kufupika, kuzama ndi mukukula, kwa chikondi cha Mulungu zimazindikilika mochepetsetsa. Dongosolo la chipulumutso silingamvetsetsedwe modzadza, ingakhale pamene oomboledwa adzaziona momwe iwo amaoneredwa ndikuziwa mmene iwo amadziwidwira; koma kupyola mu mibadwo yamuyaya choonadi chatsopano cidzakhalabe chikutambasuka ku malingaliro odabwa ndi achimwemwe."—*The Great Controversy,* p. 651.

"Mwachikhulupiliro titha kuona kutsogolo ndi kumvetsetsa chowinda cha Mulungu mukukula kwa mzeru, mphanvu za umunthu kulumikizana ndi umulungu, ndipo mphanvu iliyonse ya moyo kubweletsedwa mu kulumikizana mwachindunji ndi phata lakuunika. Tingathe kukondwera kuti zonse zomwe zimatibvutitsa ife pazimene Yehova amachita zizapangidwa kukhala zosabvuta, zinthu zobvuta kuzimvetsetsa tidzapeza kufotokozera kwake mu nthawi imeneyo; ndipo pamene mzeru zathu zofooka zimapeza chisokonekero chokhachokha ndi malonjezo osweka, tidzaona ungwiro weniweni ndi chiyanjano chokongola. [1 Akolinto 13:12]'"—*Steps to Christ,* pp.112, 113.

## 5. CHOLINGA CHA MULUNGU KWA ANTHU AKE — Lachisanu, Septemba 17

**a. Ndimunjira yanji yozindikirika imene Yehova wakhala akutambasula mawu ake munthawi ino pamene chimalidziro chili pafupi? Chibvumbulutso 10:2, 6, 7.**

---

"Buku lomwe linasindikizidwa chidzindikiro silinali buku la Chibvumbulutso, koma gawo la ulosi wa Danieli limene limakhudzana ndi matsiku otsiliza. . . [Kuchokera pa Daniel 12:4.] Pamene bukuli linasegulidwa, kulengezedwa kunachitika, "Sipadzakhalaso nthawi." (Onani Chibvumbulutso 10:6.) Buku la Danieli tsopano ndilosasindikizidwaso, ndi chibvumbulutso chopangidwa ndi Khristu kwa Yohane chizafika kwa onse okhala pa dziko lapansi. Kudzera mukuchuluka kwa chidziwitso anthu akuyenela kukonzetseredwa kuima mu tsiku la mvula yamasika."—*Selected Messages,* bk. 2, p. 105.

"Ambiri anakhazikitsa lingaliro loti buku la chibvumbulutso ndi buku losindikizidwa, ndipo iwo sadzapereka nthawi yawo ndi kuwelenga zinsinsi zake. Iwo akulankhula kuti iwo ayenera kukhazikitsa chiyang'aniro pa ulemerero wa chipulumutso, ndikuti zinsinsi zobvumbulutsidwa kwa Yohane pa chisumbu cha patimo ndi chosafuna chidwi chawo kuposa izi. Koma Mulungu samalitenga bukuli kukhala lotere. . . .

"Buku lachibvumbulutso limatsegula ku dziko lapansi zimene zakhalapo, zimene ziripo, ndi chimene chidzabwere; ndimachenjezo a athu amene chimalidziro chadziko lapansi chawafikira. Liyenera kuwelengedwa ndimantha a ulemu…

"Ambuye mwini anabvumbulutsira kwa mtumiki wake Yohane zinsinsi za buku la Chibvumbulutso, ndipo lye anapanga kuti liyenera kusegulidwa kukuwelengedwa ndi onse. Mubuku limeneli mukutambasulidwa zochitika zimene kunthawi ino zinadutsa, ndi zina zopatsa chidwi za muyaya zimene zikuchitika motidzungulira ife; maulosi ena aiwo sanafike pokwanilitsidwa modzadza kufikira kutsekedwa kwa nthawi, pamene mkangano waukulu omaliza pakati pa mphanvu za kumidima ndi kalonga wakumwamba kuzachitika."—*The SDA Bible Commentary* [E.G. White comments], vol. 7, p. 954.

**b. Kodi okhulupilira ayenera kuchita chiyani pakuwelenga malemba? 2 Timoteo 2:15; Yohane 7:17.**

---

## MAFUNSO OBWEREZA PAWEKHA — Lachisanu n'chimodzi, Septemba 18

1. Ndikhalidwe lanji limene tiyenera kukhala nawo ndicholinga chomvetsetsa choonadi?
2. Fotokozani chifukwa chiyani simalemba onse amene angamvetsetsedwe.
3. Chifukwa chiyani ambiri samafuna kulandira choonadi cha m'baibulo?
4. Ndichiyani chimene iwo onse amene amafuna kukaikira nthawi zonse amapedza?
5. Chifukwa chiyani kufuna kumvera kulikofunikira kukumvetsetsa choonadi?

LASABATA, 26 SEPTEMBA, 2026

Phunziro 13

# Kukondwera mwa Ambuye

**Vesi Loloweza**: “Koma popeza mulawana ndi khristu zowawa zake, kondwerani; kutinso pabvumbulutso la ulemerero wake mukakondwere kwakukurukuru”. 1 Petro 4:13.

**Zowerenga Zoonjezera:** *Steps to Christ,* pp, 115–126.

“Ambuye amafuna kuti ana ake onse aamuna ndi aakazi akhale osangalala, amtendere, komanso omvera.”—*Steps to Christ,* p.124.

## 1. ONYAMULA NYALI

Loyamba, Septemba 20

**a. Kodi Yesu anati ophunzira ake ali ndi udindo wotani m'dziko lino? Mateyu 5:13–16.**

“Akhristu aikidwa ngati onyamula kuunika panjira yopita kumwamba. Ayenera kuwunikira dziko lapansi kuunika komwe kukuwalira kuchokera kwa Khristu. Moyo wawo ndi khalidwe lawo ziyenera kukhala zakuti kudzera mwa iwo ena apeze lingaliro lolondola la Khristu ndi utumiki Wake.”—*Steps to Christ,* p. 115.

**b. Kodi okhulupirira ayenera kukhala chiyani kwa anthu onse? Yohane 17:18, 23; 2 Akorinto 5:20.**

“Mwa aliyense wa ana Ake, Yesu amatumiza kalata ku dziko lapansi. Ngati ndinu wotsatira wa Khristu, amatumiza kalata kwa banja, mudzi, msewu, kumene mumakhala. Yesu, wokhala mwa inu, akufuna kulankhula ndi mitima ya iwo omwe samudziwa Iye. Mwina sawerenga Baibulo, kapena samva mawu omwe amalankhula nawo m'masamba ake; sawona chikondi cha Mulungu kudzera mu ntchito Zake. Koma ngati ndinu woimiradi Yesu, mwina kudzera mwa inu adzatsogoleredwa kuti amvetse zinazake za ubwino Wake ndikupeza mwayi womukonda ndi kumutumikira Iye.”—Ibid.

**c. Kodi ndi njira iti yokha yomwe ingatheke kukwaniritsa ntchito imeneyi? 2 Akorinto 3:2–5.**

**a. Kodi chionetsero chapamwamba kwambiri cha chikondi cha Mulungu kwa ana ake ndi chiyani? Yohane 3:16; Aroma 5:6–10.**

"Pamene tikuoneka kuti tikukayikira chikondi cha Mulungu ndi kusakhulupirira malonjezo Ake, timamunyoza Iye ndi kumvetsa chisoni Mzimu Wake Woyera. Kodi mayi angamve bwanji ngati ana ake akudandaula za iye nthawi zonse, ngati kuti sanali ndi cholinga chabwino kwa iwo, pamene khama lake lonse la moyo linali loti akwaniritse zofuna zawo ndi kuwatonthoza? Tiyerekeze kuti akukayikira chikondi chake; zingamuswe mtima. Kodi kholo lililonse lingamve bwanji ngati ana ake akuchitiridwa motere? Ndipo Atate wathu wakumwamba angatione bwanji pamene sitikukhulupirira chikondi Chake, chomwe chamupangitsa kuti apereke Mwana Wake wobadwa yekha kuti tikhale ndi moyo? Mtumwiyo akulemba kuti, 'Iye amene sanasiye Mwana Wake, koma anampereka chifukwa cha ife tonse, sadzatipatsanso ife zinthu zonse pamodzi ndi Iye?' Aroma 8:32. Komabe ndi angati, mwa zochita zawo, ngati si m'mawu, akunena kuti, 'Ambuye sakutanthauza izi kwa ine. Mwina amakonda ena, koma sandikonda ine."—*Steps to Christ,* pp. 118, 119.

**b. N'chiyani chimatsimikizira kuti Mulungu akufuna kupatsa ana ake zinthu zonse? Aroma 8:32.**

"Inu amene mumadziona kuti ndinu osafunika kwambiri, musaope kupereka mlandu wanu kwa Mulungu. Pamene anadzipereka mwa Khristu chifukwa cha machimo a dziko lapansi, Iye anatengera mlandu wa moyo uliwonse. 'Iye amene sanasiye Mwana wake, koma anampereka chifukwa cha ife tonse, adzalekera bwanji kutipatsa ife zonse kwaulere pamodzi ndi Iye?' Aroma 8:32. Kodi sadzakwaniritsa mawu achisomo operekedwa kuti atilimbikitse ndi kutipatsa mphamvu?

"Khristu safuna chilichonse choposa kuwombola cholowa Chake ku ulamuliro wa Satana."—*Christ's Object Lessons,* p. 174.

**c. Kodi chikondi ichi chingawonetsedwe bwanji mwa ife? 1 Yohane 4:9–12.**

"Antchito achikhristu omwe apambana pa khama lawo ayenera kudziwa Khristu; ndipo kuti amudziwe Iye, ayenera kudziwa chikondi Chake. Kumwamba, kuyenerera kwawo monga antchito kumayesedwa ndi kuthekera kwawo kukonda monga momwe Khristu anakondera ndi kugwira ntchito monga momwe Iye anagwirira ntchito.

"'Tisakonde ndi mawu,' mtumwiyo analemba, 'koma m'zochita ndi m'choonadi.' Khalidwe lachikhristu limakhala lokwanira pamene chilakolako chothandiza ndi kudalitsa ena chimachokera mkati nthawi zonse. Ndi mlengalenga wa chikondi ichi chozungulira moyo wa wokhulupirira chomwe chimamupangitsa kukhala fungo la moyo ku moyo ndi kumuthandiza Mulungu kudalitsa ntchito yake."—*The Acts of the Apostles*, p. 551

**a. Kodi n’chiyani chinazindikiritsa moyo wa Khristu mu ntchito yake yopulumutsa anthu? Yesaya 53:10, 7.**

______________________________________________________________

______________________________________________________________

“Moyo wa [Khristu] unali wodzipereka nthawi zonse. Analibe malo okhala m'dziko lino, kupatulapo pamene kukoma mtima kwa abwenzi kunamupatsa Iye monga woyenda m'njira." Iye anabwera kudzatithandiza kukhala ndi moyo wa anthu osauka, ndi kuyenda ndi kugwira ntchito pakati pa osowa ndi ovutika. Posadziŷika komanso mopanda ulemu, Iye anayenda pakati pa anthu amene anawachitira zambiri.”—*Gospel Workers,* pp. 42, 43.

“Misozi ya [Mwana wa Mulungu] sinali ya Iye mwini, ngakhale kuti ankadziwa bwino komwe mapazi ake anali kugwirira. Pamaso pake panali Getsemane, malo omwe ululu wake unali kuyandikira. Chipata cha nkhosa chinalinso choonekera, chomwe kwa zaka mazana ambiri anthu ophedwa chifukwa cha nsembe ankatsogoleredwa nacho, ndipo chinali choti chimutsegulire pamene ‘anabweretsedwa ngati mwana wa nkhosa wopita kukaphedwa.’ Yesaya 53:7. Pafupi panali Kalvari, malo opachikidwa. Panjira imene Khristu anali pafupi kuyendamo payenera kugwa mantha a mdima waukulu pamene Iye anayenera kupanga moyo wake kukhala nsembe ya uchimo. Komabe sikuti kuganizira za zochitika izi ndiko kunamupangitsa mthunzi mu ola lino la chisangalalo. Palibe chiyembekezo cha ululu wake woposa waumunthu chomwe chinaphimba mzimu wopanda dyera umenewo. Analirira zikwizikwi za Yerusalemu—chifukwa cha khungu ndi kusalapa kwa iwo amene anabwera kudzawadalitsa ndi kuwapulumutsa.”—*The Great Controversy,* p. 18.

**b. Mu kuvutika ndi kuyesedwa kwake, n’chiyani chinapatsa Yesu kulimba mtima kuti amalize Ntchito yake? Yesaya 53:11; Ahebri 12:2.**

______________________________________________________________

______________________________________________________________

“Zotsatira za mkangano wa Mpulumutsi ndi mphamvu za mdima ndi chisangalalo kwa oomboledwa, zomwe zimawonjezera ulemerero wa Mulungu kwamuyaya. Ndipo mtengo wa moyo ndi wofanana ndi umene Atate amakhutitsidwa ndi mtengo woperekedwa; ndipo Khristu mwiniwake, akuona zipatso za nsembe Yake yaikulu, amakhutitsidwa.”—Ibid., p. 652.

"Nthawi zambiri amati Yesu analira, koma sankadziwika kuti ankamwetulira." Mpulumutsi wathu analidi Munthu wa Zisoni, komanso wodziwa chisoni, chifukwa anatsegula mtima wake ku mavuto onse a anthu. Koma ngakhale kuti moyo wake unali wodziletsa ndipo unali ndi ululu ndi chisamaliro, mzimu wake sunasweke. Nkhope yake sinali ndi chisoni kapena kukhumudwa, koma inali yamtendere nthawi zonse. Mtima wake unali kasupe wa moyo, ndipo kulikonse kumene ankapita anali kunyamula mpumulo ndi mtendere, chimwemwe ndi chisangalalo.”— *Steps to Christ,* p. 120

**a. Pamene mayesero akumana ndi wokhulupirira, kodi n'chiyani chomwe chimaperekedwa kuti agonjetse nkhondo yauzimuyi? Aefeso 6:11–18**

____________________________________________________________

____________________________________________________________

"Onse ali ndi mayesero; chisoni chovuta kupirira, mayesero ovuta kukana. Musauze anzanu mavuto anu, koma perekani zonse kwa Mulungu m'pemphero. Pangani lamulo kuti musalankhule mawu amodzi okayikira kapena okhumudwitsa. Mukhoza kuchita zambiri kuti muwalitse miyoyo ya ena ndikulimbitsa khama lawo, mwa mawu a chiyembekezo ndi chisangalalo choyera."—*Steps to Christ,* pp. 119, 120.

**b. N'chifukwa chiyani ambiri amakayikira pakati pa chikhulupiriro ndi kukayikira akamayesedwa? Kodi ayenera kuchita chiyani? Mateyu 14:28–31; Yakobo 1:2.**

____________________________________________________________

"Pali anthu ambiri olimba mtima omwe ali pafupi kufooka chifukwa cha mayesero, omwe ali pafupi kufooka chifukwa cha kulimbana ndi iwo eni komanso ndi mphamvu za choipa. Musamulepheretse munthu wotereyu pankhondo yake yovuta. Mulimbikitseni ndi mawu olimba mtima komanso opatsa chiyembekezo omwe adzamulimbikitsa panjira yake. Motero kuwala kwa Khristu kungawale kuchokera kwa inu. 'Palibe aliyense wa ife amene amakhala ndi moyo kwa iye yekha.' Aroma 14:7. Ndi mphamvu yathu yosazindikira, ena angalimbikitsidwe ndi kulimbikitsidwa, kapena angakhumudwe, ndikuchotsedwa pa Khristu ndi choonadi.

"Pali ambiri omwe ali ndi lingaliro lolakwika la moyo ndi khalidwe la Khristu. Amaganiza kuti Iye analibe kutentha ndi dzuwa, kuti anali wouma mtima, wokhwima, komanso wopanda chisangalalo. Nthawi zambiri zochitika zonse zachipembedzo zimasokonezedwa ndi malingaliro oipa awa." —Ibid., p. 120.

**c. Kodi njira ya olungama imakhala yowala bwanji ngakhale pakati pa mayesero? Miyambo 4:18; Afilipi 4:4.**

____________________________________________________________

"Msewu ukhoza kukhala wovuta komanso wokwera movutikira; pakhoza kukhala ming'alu kudzanja lamanja ndi kumanzere; tingafunike kupirira zovuta paulendo wathu; tikatopa, tikafuna kupuma, tingafunike kupitiriza kugwira ntchito movutikira; tikafooka, tingafunike kulimbana; tikataya mtima, tiyenerabe kuyembekezera; koma ndi Khristu monga chitsogozo chathu sitidzalephera kufika pamalo omwe tikufuna. Khristu mwiniwake wayenda njira yovuta patsogolo pathu ndipo wakonza njira ya mapazi athu.

"Ndipo njira yonse yokwera msewu wotsetsereka wopita ku moyo wosatha ndi akasupe a chisangalalo chotsitsimutsa otopa."—*Thoughts from the Mount of Blessings,* p.140.

## 5. MPHOTHO YATHU NDI CHISANGALALO — Lachisanu, Septemba 24

**a. Ndi lonjezo liti la Yesu lomwe liyenera kutipatsa chifukwa chosangalalira ndi kutamanda Atate wathu wakumwamba? Yesaya 41:10; Luka 12:32; 1 Petro 4:13.**

“Si chifuniro cha Mulungu kuti anthu ake azilemedwa mosamala. Koma Ambuye wathu satinyenga. Satiuza kuti, ‘Musaope; palibe zoopsa panjira yanu.’ Amadziwa kuti pali mayesero ndi zoopsa, ndipo amachita nafe momveka bwino. Sanaganize zochotsa anthu ake m’dziko la uchimo ndi zoipa, koma amawatsogolera ku malo othawirako osalephera.”—*Steps to Christ,* pp. 122, 123.

**b. Tchulani malonjezo ena odabwitsa a mtendere ndi chimwemwe omwe Yesu wapereka Yohane 14:1—3, 27; 15:11; 16:20.**

“Sitingathe kusiya kuyembekezera zovuta zatsopano mu mkangano womwe ukubwera, koma tingathe kuyang'ana zomwe zapita komanso zomwe zikubwera, ndikunena kuti, ‘Yehova watithandiza mpaka pano.’ ‘Monga masiku anu, momwemonso mphamvu yanu idzakhala.’ Deuteronomo 33:25. Mayesero sadzapitirira mphamvu zomwe zidzapatsidwa kuti tipirire. Ndiye tiyeni tiyambe ntchito yathu komwe tikupeza, tikukhulupirira kuti chilichonse chomwe chingabwere, mphamvu yolingana ndi mayesero idzaperekedwa.

“Ndipo pang’onopang’ono zipata zakumwamba zidzatsegulidwa kuti ana a Mulungu alowe, ndipo kuchokera pakamwa pa Mfumu ya ulemerero madalitso adzamveka m’makutu mwawo ngati nyimbo yokoma kwambiri, ‘Idzani, inu odalitsidwa ndi Atate wanga, lowani ufumu wokonzedwera inu kuyambira kukhazikitsidwa kwa dziko lapansi.’ Mateyu 25:34. . . .

“Poganizira za cholowa chaulemerero chomwe chingakhale chake, ‘munthu angapereke chiyani chosinthana ndi moyo wake?’ Mateyu 16:26. . . . Moyo woomboledwa ndi kuyeretsedwa ku uchimo, ndi mphamvu zake zonse zolemekezeka zoperekedwa ku utumiki wa Mulungu, ndi wamtengo wapatali kwambiri; ndipo pali chimwemwe kumwamba pamaso pa Mulungu ndi angelo oyera pa moyo umodzi woomboledwa, chimwemwe chomwe chimafotokozedwa m’nyimbo za chigonjetso choyera.” —Ibid., pp. 125, 126.

## MAFUNSO OBWEREZA PAWEKHA — Lachisanu n’chimodzi, Septemba 25

1. Ndimotani momwe onse ngakhale osadziwa Baibulo adzafikiridwe ndi choonadi?
2. Kodi Ambuye amasonyeza bwanji chikondi chake chopanda malire kwa anthu?
3. Kodi Yesu anali ndi chitsimikizo chotani pamene ankakumana ndi mavuto ndi imfa yake?
4. Kodi ndi chofunika chiti chimene tiyenera kukumbukira tikakumana ndi mayesero?
5. Mu moyo wa tsiku ndi tsiku, kodi n’chiyani chomwe chiyenera kukhala m’maganizo mwa wokhulupirira?

# Zopereka za Sabata Loyamba



## Lasabata, Julayi 5, 2026

**Kukuza Tchalitchi ku Chennai, India**

Tiyeni tigwirane manja kuthandiza kumalizitsa kumanga tchalitchi cha mu mzinda okhala ndi miyoyo 12 miliyoni (onani p. 4.)



## Lasabata, Ogasti 1, 2026

**Department ya Maphunziro ya General Conference**

Taitanidwa kuti tiphunzitse, tiphunzitse, tiphunzitse, ndipo ndalama zikufunikira kuti izi zichitike bwino. (onani p 25.)



## Lasabata, Septemba 5, 2026

**Sukulu Yophunzitsa za Mishonale ya Baibulo ku Philippines**

Tiyeni tilimbitse sukuluyi kuti ikhale zonse zimene Mulungu akufuna kuti ikhale (onani p. 51.)